


# Utumiki Wamphamvu



*Buku La Atumiki a Pentecoste*

**Denzil R. Miller**

# Utumiki Wamphamvu

*Buku La Atumiki a Pentecoste*

Mlembi  
Denzil R. Miller

Womasulira  
Lawrence Chipao

## Copyright

©2011 Denzil R. Miller. All rights reserved. No part of this book may be reproduced, stored in a retrieval system, or transmitted in any form or by any means—electronic, mechanical, photocopy, recording, or otherwise—without prior written permission of the copyright owner, except brief quotations used in connection with reviews in magazines or newspapers.

## Copyright–Chichewa

Buku ili ndi chimasuliro cha buku la *Power Ministry: A Handbook for Pentecostal Preachers*, lolembedwa ndi a Dr. Denzil R. Miller, ndi kusindikizidwa ndi a ATTS ku Springfield, MO, USA. Chilolezo chakumasulira bukuli chinaperekedwa ndi a Denzil R. Miller ku sukulu ya AGST ku Malawi.

Malemba onse a m’Baibulo amene alembedwa mkatimu, kupatulapo amene aonetseredwa kochokera kwake, achokera mu Buku Lopatulika: Ndilo Mau a Mulungu. Copyright 1922, 1936, 1966, 1992, 1996, a Bible Society of Malawi.

Palibe gawo lirilonse la buku ili limene lingalembedwenso kapena kusandulizidwa mu njira ina iliyonse popanda kupempha chilolezo kwa mwani wake. Zilolezo zonse zasungidwa ndi mwini wake.

This book is a translation of the book, *Power Ministry: A Handbook for Pentecostal Preachers*, by Denzil R. Miller

PneumaLife Publications - 2011  
Springfield, MO, USA

# Za Mkatimu

Mau Otsogolera .....	iv
----------------------	----

## Gawo I: Kumvetsetsa Utumiki wa Mphamvu

Chaputala 1: Kutanthauzira Utumiki Wamphamvu .....	3
Chaputala 2: Kulongosolera Utumiki wa Mphamvu .....	13
Chaputala 3: Utumiki wa Mphamvu ndi Ufumu wa Mulungu .....	23
Chaputala 4: Utumiki wa Mphamvu ndi Kulalikira Uthenga Wabwino .	31

## Gawo II: Kukonzekera Utumiki wa Mphamvu

Chaputala 5: Kukonza Utumiki wa Mphamvu .....	45
Chaputala 6: Ubatizo wa Mzimu Woyera ndi Utumiki wa Mphavu .....	57
Chaputala 7: Kulandira Mphatso ya Mzimu Woyera ndi Utumiki wa Mphamvu .....	67
Chaputala 8: Kulalikira ndi Zipatso za Mzimu .....	75
Chaputala 9: Kutsogoleredwa Moyenera Mutumiki Wamphamvu. ....	87
Chaputala 10: Zida Zathu Zoyenerera pa Chikhalidwe .....	97

## Gawo III: Kuchitachita mu Utumiki Wamphamvu

Chaputala 11: Kuchiritsa Odwala .....	111
Chaputala 12: Kutulutsa Ziwanda .....	125
Chaputala 13: Kugonjetsa Mizimu ya m'Madera .....	137
Chaputala 14: Kupemphera ndi Okhulupilira Kuti Alandire Mzimu Woyera .....	147
Chaputala 15: Utumiki wa Mphamvu mu Misonkhano ya Usodzi .....	159
Zowonjezera A: Utumiki wa Yesu wa Machiritso mu Mabuku a Uthenga Wabwino .....	171
Zowonjezera B: Njira Zomwe Yesu Anagwiritsa Ntchito Pochiritsa Anthu	173
Mabuku Agwiritsidwa Ntchito a m'Chingelezi .....	179
Mabuku Ena a m'Chingelezi Othandizira .....	181



# Mau Otsogolera

## Chiyambi

Mu zaka zapitazo, atsogolera a masukulu ndi a mipingo ya mu Africa anapempha phunziro latsopano. Phunziro lake lidzakhudza zinthu zimene zimakhudza miyoyo ndi utumiki wa abusa a ku Africa, amishoni, alaliki ndi atsogolera a mipingo. Zinthu izi zikukhudzana ndi utumiki wa “kulimbana ndi mphamvu.” Anthu ambiri amafunsa kuti, Kodi tingatumikire bwanji mu mphamvu ndi mukudzodza kwa Mzimu Woyera? Kodi tingapemphere bwanji ndi odwala ndi kuona iwo akuchiritsidwa? Kodi tingatsogolere bwanji Akhristu kudzadzidwa ndi Mzimu Woyera?

Buku ili lalembedwa kuti liyankhe mafunso ofunikira amenewa. Liri ndi zolinga zitatu izi:

1. Kupereka manziko a Baibulo a mphamvu ya utumiki. Utumiki wokhazikika ndi wovomerezeka ukhonzha kumangika pa manziko a mtundu uwu okha. Cholinga ichi chakwaniritsidwa mu Gawo I: “Kumvetsa Utumiki wa Mphamvu.”
2. Kupereka ndandanda wa kukonzekera kwa moyo wa iwo akufuna kutumikira mu utumikiwu mu mphamvu ya Mzimu Woyera. Kodi mtumiki wa Pentekoste akhale munthu wotani? Kodi iwo adziwe chiyani ndipo akhale ndi chiyani asanayambe kutumikira? Mayankho ku mafunso awa akambidwa mu Gawo II: Kukonzekera Utumiki wa Mphamvu.”
3. Kupereka zitsanzo zogwirika za mmene mlaliki wa Pentekoste angachitire mu utumikiwu. Cholinga ichi chakambidwa mu Gawo III: “Kuchitachita mu Utumiki wa Mphamvu.”

*Utumiki Wamphamvu* ndi wochitachita, ndipo ndi maphunziro a iwo amene akutumikira. Maphunzirowa amatsogolera iwo amene akufunitsitsa kumvera Yesu pa utumiki wa kulalikirira Uthenga Wabwino wotsatiridwa ndi zizindikiro (Marko 16:15-20).

## Zofunikira kwa Ophunzira

Simungathe kulandira phindu lonse la bukuli pakungoliwerenga chabe. Kuwerenga ndi kofunikadi inde koma kuwerengako *kutsatiridwe* ndi zintchito zake monga mmene bukuli likukambira. Cholinga chanu chachikulu

chisakhale kungokhonza mayeso. Muyenera kuphunzira kutumikira moyenerera mumphamvu ndi mukudzodza kwa Mzimu Woyera. Muchite izi motsatiridwa ndi zizindikiro.

## **Zofunikira Kumaphunzirowa**

Zofunikira izi kwa mphunzitsi zizathandiza kupititsa patogolo cholinga cha buku ili. Ophunzira aphunzire (kuchita izi m'moyo mwao) mfundo ziri mu chaputala chilichonse. Aphunzitsi athandizire pogwiritsa ntchito njira zakaphunzitsidwe koyenera. Zina mwa njirazi ndi izi:

- kupereka ndime zoti awerenge.
- kungopereka chiphunzitso.
- kukambirana m'kalasi.
- kupereka ntchito yoti ilembedwe ndi kupereka mayeso.

Mowonjezera ku zokambirana m'kalasi, kutuluka m'kalasi ndi kupita ku utumiki wa kunja ndi kofunikira. Maphunziro oterewa atha kuperekedwa mosiyanasiyana. Njira ziwiri zaphindu ndi izi:

- kukhala ndi magulu ophunzilira sabata iliyonse.
- kulimbikitsa ophunzira kumayeserera utumikiwu kunja.

## **Magulu Othandizira**

Magulu ophunzilira ayenera kukhala ngati nthawi yowonjezera ku makalasi a nthawi zonse. Mu magulu awa a sabata ndi sabata ophunzira akumane pakungolambira, kupemphera ndi kukhulupilira Mulungu kuyenda pakati pao. Aphunzitsi alimbikitse ophunzira kukumvetsera kwa Mzimu. Alimbikitse ophunzira kupempherera odwala amene apezeka pakati pao. Aphunzitsi ndi ophunzira onse pamodzi alore Mzimu wa Ambuye kuyenda ndi kumasula mphatso m'miyoyo yao.

Mu nthawi iyi yophunzira mochitachita, aphunzitsi nawonso akhale ngati m'modzi wa ophunzira. Apewe kuonetsera ngati kuti amadziwa zonse. Athe kuwauza ophunzira kuti iwo nawonso akufuna kuphunzira zina zimene zingachitike.

Ndi thandizo la utsogolera wa sukulu yanu, magulu othandizira atha kuphatikizirapo misonkhano ya kulandira Mzimu Woyera masana a tsiku lina lirilonse. Nthawi iyi mutha kuyitana ophunzira a sukulu yonse kuti atengepo nawo gawo lakulandira Mzimu Woyera kapena machiritso. Mu nthawi iyi aphunzitsi ndi ophunzira atha kupanga zomwe akhala akuphunzira m'kalasi. Ophunzira adzalimbikitsidwa pamene Mulungu adzakhala akuyenda ndi kudalitsa mapempherowo.

## **Kutumikira Kunja**

Aphunzitsi atha kukonza nthawi yakuturuka ndi kalasi lonse mu njira ziwiri. Poyamba, atha kungowatuma ophunzira kuti akatumikire malo ena ake. Kachiwiri, akhonza kuyenda nao ndi kuwapatsa chitsanzo chakutumikira.

**1. Zochita Ophunzira.** Mphunzitsi atumize ophunzira ali awiri awiri kukachita utumiki wa mphamvu. Utumiki wake uphatikizirepo kuchiritsa odwala, kuturutsa ziwanda ndi kupempherera ofuna kudzadzidwa ndi Mzimu Woyera. Ophunzirawa ayenera kubwerera kusukulu ndi kukanena zomwe akumana nazo kwa anzao m'kalasi. Kukambirana kotere kudzalimbikitsa ndi kukonza ophunzira m'malo mmene sanachite bwino. Iyi ndi njira yomwe Yesu anagwiritsapo ntchito mu Luka 10:1-24.

**2. Kupereka Chitsanzo.** Apa, mphunzitsi ayenera kutsogolera ophunzira ku utumiki. Agawe kalasi lake mu magulu ang'ono ang'ono, ndi kumayenda ndi gulu limodzi pa nthawi. Iye atha kumagwirizana ndi mipingo yoyandikira kuti akatumikire ku mipingoyo. Pamene ayitanidwa kapena kuvomerezedwa kukatumikira ku mpingo, ayenera kupita ndi ophunzirawo ndi kukachita monga mwa phunzitori.

Aphunzitsi pamodzi ndi ophunzira ayenera kumafunafuna kumene angapeze mwayi wakutumikira utumiki uwu wa mphamvu. Ophunzira amene adwala ayenera kuchiritsidwa. Ophunzira ena afunika kudzadzidwa ndi Mzimu Woyera. Ophunzira ayenera kuthandizana mu utumiki uwu wakupempherera anzao kuti adzadzidwe ndi Mzimu Woyera.

**Gawo I**

**Kumvetsetsa Utumiki  
wa Mpamvu**



## Chaputala 1

# Kutanthauzira Utumiki Wamphamvu

## Kufunikira kwa Utumiki wa Mphamvu

Yesu sanausiye Mpingo wake wopanda mphamvu pamene Iye anabwerera ku mwamba kwa Atate. Iye anaulonjeza Mpingo kuti adzaupatsa mphamvu yakufalitsira Uthenga Wabwino wa Khristu (Machitidwe 1:8).

Ambuye wathu anakwaniritsa lonjezanoli pa tsiku la Pentekosti (Machitidwe a Atumwi 2). Zotsatira zake ndizo kuti Mpingo wa m'Chipangano Chatsopano unatumikira mwa mphamvu yayikulu ndipo Zozizwitsa zinaonekera.

Mpingo uli ndi udindo wochokera kwa Khristu wa kufalitsa Uthenga Wabwino wa Khristu ku maiko onse. Mpingo ufunikira anthu otumikira mu mphamvu ya Mulungu pa zifukwa zinai izi:

- tiri pa nkondo
- mdani ali ndi mphamvu
- ntchito ndi yayikulu
- utumiki wa mphamvu umachita kwakukulu.

### Tiri pa Nkhondo

Baibulo limatiphunzitsa kuti ana a Mulungu ali pankhondo yayikulu ya uzimu. Nkhondoyi ili pakati pa ana a Mulungu ndi Satana komanso omutumikira ake. Mu Mateyu 13:39, Yesu ananena kuti mdani wathu ndi

mdyerekezi (onaninso mu Luka 10:19). Paulo anafotokoza za nkondo ya uzimuyi motere.

*Chifukwa kuti kulimbana kwathu sitilimbana nao mwazi ndi thupi, komatu nao maukulu, ndi maulamuliro, ndi akuchita zolimbika a dziko lapansi a mdima uno, ndi a uzimu a choipa m'zakumwamba Aefeso 6:12.*

Paulo anatinso tiyenera kugwiritsa ntchito zida za mphamvu za Uzimu pomenya nkondoyi: “Pakuti sitinyanyamphiradi tokha, monga ngati sitinafikira kwa inu; pakuti tinadza kufikira inunso mu Uthenga Wabwino wa Khristu” (2 Akorinto 10:14). Malinga awa ndi auzimu amene womanga wake ndiye mdani wathu. Tifunadi utumiki wamphamvu chifukwa chakuti tiri pankondo imene ili yooneka.

### **Mdani ali ndi Mphamvu**

Satana ndi mdani wamphamvu wa mpingo komanso Uthenga Wabwino. Mu Luka 10:19 Yesu ananena motere “Mphamvu ili yonse ya mdaniyo;” Satana wayika gulu la ankondo ake lalikulu, ndi lodzipereka potsutsa kuti Uthenga Wabwino usalalikidwe. Komatu ife tingathe kumugonjetsa Satana ndi mphamvu yayikulu yoposera yake- mphamvu iyi ndi mphamvu ya Mzimu Woyera.

### **Ntchito ndi Yayikulu**

Ntchito yampingo ndi yayikulu. Utumiki wamphamvu ndiyo njira yokhayo yomwe tingathe kumaliza ntchitoyi. Mu ulamuliro wake waukulu, Yesu anatilamula kuti tilalike uthenga wabwino padziko lonse lapansi. Tiyenera kulalikirira Uthenga Wabwino monga umboni ku mayiko onse Yesu asanabwerenso kudzatenga mpingo (Mateyu 24:14).

Pakali pano anthu opitirira ma biliyoni atatu sanamvebe umboni wokwana wa Uthenga Wabwino. Anthu ambiri ali m'maiko amene akulamuliridwa ndi zipembezidzo zoipa. Zipembezidzo zimenezi zimatsutsa mwankhaza za kulalikiridwa kwa Chikristu. Sitingathe kuwafikira otayika m'maiko amenewa popanda mphamvu yochokera kumwamba.

Yesu analonjeza kuti adzapereka mphamvu kwa omutsata iye kuti akachite ntchito yake yayikuluyi:

*Komatu mudzalandira mphamvu, Mzimu Woyera atadza pa inu: ndipo mudzakhala mboni zanga m'Yerusalemu, ndi m'Yudeya lonse, ndi m'Samariya, ndi kufikira malekezero ace a dziko. (Machitidwe 1:8).*

Yesu Khristu anatinso adzatsimikizira mau ake ndi zizindikiro za mphamvu pamene ife tiri kutumikira.

*Mukani ku dziko lonse lapansi, lalikirani Uthenga Wabwino kwa olengedwa onse. ... Ndipo zizindikilo izi zidzawatsata iwo akukhulupirira m'dzina langa adzaturutsa ziwanda; adzalankhula ndi malankhulidwe atsopano; adzatola njoka, ndipo ngakhale akamwa kanthu kakufa nako, sikadzawapweteka; adzaika manja ao pa odwala, ndipo adzachira (Mk. 16:15b, 17-18)*

Njira yokhayo tingathe kupititsa patsogolo ufumu wake wa Khristu padziko la pansu ndikuonjezera mphamvu yakuchitachita pamene pali mphamvu. Mphamvu yoyambilira ya Mulungu ndi mphamvu ya Mzimu Woyera imene ilikugwira ntchito kudzera mu Mpingo. Yesu anati, “Ndipo kuyambira masiku a Yohane Mbatizi, kufikira tsopano lino, Ufumu wa Kumwamba uli wokangamizidwa, ndipo okangamirawo aukwatula ndi mphamvu” (Mateyu 11:12).

## **Utumiki wa Mphamvu Umachita Kwakukura**

Chifukwa chomaliza chimene tiyenera kutengerapo gawo pa utumiki wamphamvu ndicho kuti utumiki wa mphamvu umachitadi kwakukulu. m'Buku la Machitidwe a Atumwi timawerenga kupambana kwa ntchito ya Mpingo Woyamba uja. Kupambana kwa mpingo kunabwera ndi mphamvu zapaderadera za Mzimu Woyera - zizindikiro zinali kuwatsatira.

Zoona zake zomwe zimachitika mu Mpingo Woyamba uja zilinsu mu Mpingo wa lero. A John Wimber, m'buku lawo lotchedwa “Power Evangelism” (Usodzi wa Mphamvu) (1986, tsamba 31) anati, “Tikaona pa dziko lonse lapansi, kukula ndi kuchuluka kwa mpingo (70%) kuli kutchitika pakati pa mipingo ya Pentekoste ndi okhulupilira mphatso za Mzimu Woyera.” Magulu awiriwa amakhulupirira komanso kuyembekezera mphamvu ya Mzimu Woyera kugwira ntchito m'mautumiki awo. A Wimber akunenapo zomwe a Peter Wagner adakambapo motere:

Pali kugwirizana pakati pa kuchulukitsa mipingo ndi utumiki wa machiritso ... pamene uthenga ulalikiwa koyamba m'dera lina lililonse ndipo ngati sitipita ndi kuvetsetsa komanso kugwiritsa ntchito mphamvu za kuya za Mzimu Woyera, sitingathe kupititsa patsogolo Uthenga Wabwino (1986, tsamba 39).

Tonse timafuna kuti tichite bwino mu utumiki wathu wofalitsa uthenga. Apa ndipamene tifunika kutsanzira njira zomwe zili m'Chipangano Chatsopano. Tiyenera kugwiritsa ntchito mphamvu ngati zomwe atumwi anagwiritsa. Tiphunzire kuchita monga Atumwi anachitira, kuyenda komanso kutumikira mu mphamvu ya Mzimu Woyera.

## **Kutanthauzira Mau Ena Omwe Agwiritsidwa Ntchito**

Kuti titumikire mu mphamvu ya Mzimu tiyenera kumvetsa bwino bwino kuti Utumiki wa Mphamvu ndi chiyani. Chotero, tifunika kutanthauzira mau ena okhudzana ndi utumiki wa Umulungu.

### **Utumiki wa Mphamvu.**

M' buku ili lonse, tatanthauzira *utumiki wa mphamvu* kuti ndiwo utumiki umene umachitika mopyola zinthu za chilengedwe zomwe ife tizidziwa. Utumikiwu umachokera kwa Mzimu wa Mulungu pakupititsa patsogolo Ufumu wa Mulungu. Utumiki wa mphamvu umalozera ndi kusonyeza mphamvu ya Mulungu. Zina mwa zina za muutumikiwu ndi izi:

- Zizindikiro ndi Zozizwa
- Machiritso ochokera ku mphamvu ya Mulungu
- Kutulutsa ziwanda
- Utumiki wa mphatso za Mzimu
- Ndi zina zonse zimene zimaonetsa mphamvu ya Mulungu komanso kupezeka kwake.

Tibwerezenso kunena kuti cholinga chake cha utumiki wa mphamvu ndi kupititsa patsogolo Ufumu wa Mulungu.

### **Kulimbana kwa Mphamvu**

Tikhoza kutanthauzira mau akuti *kulimbana kwa mphamvu* m'njira ziwiri. Kutanthauzira mosaganizira madera onse, mau awa amatanthauza kudzudzula mphamvu za mdima (kutsutsana ndi ziwanda). Kudzudzula uku kumachitika mu mphamvu ya dzina la Yesu. Molingana ndi mmene a Allen Tippet ananenera, adati kulimbana kwa mphamvu ndiko “kulimbana koopsya pakati pa Ufumu wa Mulungu ndi ufumu wa Satana” (1986 tsamba 16). A Peter Wagner nawonso adatanthauzira mauwa mofanana motere: Kulimbana kwa mphamvu ndiko kuwonekera poyera kwa zochitika kuti Yesu ndiye wamphamvu zoposa milungu komanso mizimu ina imene anthu ena amayipembedza kapena kuyiopa” (1989, tsamba 4). Ife tikugwirizana nako kutanthauzira kumeneku, koma zimene zanenedwazo ndi zocheperapo poyerekeza ndi m'mene tifunira kuphunzira mbuku lino.

Monga tagwiritsira ntchito m'buku ili mau akuti *kulimbana kwa mphamvu*, ali ndi tanthauzo lalikulu ndithu. Mauwa akutanthauza kuti, izi ndi zochitika zooneka ndi maso za ukulu wa mphamvu ya Mulungu popititsa patsogolo ufumu Wake pa dziko lapansi.

Chiri chonse choyenera kugonjetsedwa kuti uthenga wabwino ukhulupiliridwe chimencho ndicho kulimbana kwa mphamvu .... Kutulutsa ziwanda ndi njira imodzi yowonetsa kulimbana kwa mphamvu. Komatu kulimbana kwa mphamvu, sipokhapo pamene Satana watulutsidwa, kapena ziwanda zasonyeza kupezeka kwao .... Pamene Ufumu wa Mulungu udza motsutsana ndi ufumu wa dziko lapansi (pamene Yesu akumana ndi Satana), pamakhala kulimbana.

### **Kulimbana pa Choonadi**

Kulimbana pa choonadi kumachitika polengeza momveka bwino Uthenga Wabwino wa Yesu Khristu. Izitu zimachitika pamene pali kulimbana kwa mphamvu. Kulimbana kwa mphamvu kumachitika pofuna kugonjetsa mphamvu za m'dima, pamene kulimbana pa choonadi kumachitika potsutsana ndi ziphunzitso zonama za chipembedzo kapena za mtundu wa anthu mdera lao. Ziphunzitso zonamazi zimamanga anthuwo muukapolo pamene kulimbana pa choonadi kumatengera iwo ku kumasulidwa. Ndichifukwa chake kuti kulimbana pa choonadi kuyenera kutsatirana ndi kulimbana kwa mphamvu. Phunziro ili la kulimbana ndi choonadi lakambidwanso mozama m'mutu wa chinayi wa bukuli.

## Usodzi wa Mphamvu

Mphamvu ya usodzi imaoneka pamene kulimbana kwa mphamvu ndi kulimbana pa choonadi zachitika motsatana. Onani mmene tafotokozera pa Chithunzi 1.1 m'musimu.

---

### Chithunzi 1.1 Masamu a Usodzi wa Mphamvu

Kulimbana Kwa Mphamvu + Kulimbana pa Choonadi = Usodzi wa Mphamvu

---

A Wimber anati usodzi wa mphamvu ndiko kuwonetsera Uthenga Wabwino umene umadza ndi mphamvu ya Mulungu kudzera mu zizindikiro ndi zozizwa ... Usodzi wa Mphamvu ndiwo usodzi umene umafika kwa anthu potsatira ndi pothandizidwa ndi kupezeka kwa Mulungu (1986, tsamba 35).

Usodzi wa mphamvu umaoneka pamene mphamvu ya Mulungu iposa chilengedwe chirichonse molumikizana ndi kulalikidwa kwa Uthenga Wabwino komanso motsindika ndi moveka bwino.

## Machiritso a Mphamvu

Machiritso a Umulungu atha kugawidwa pawiri. Gawo loyamba ndilo *machiritso a Pangano*. Kuchiritsidwa kwa Pangano kumachokera pa ntchito yomwe Yesu anachita poluzanitsa anthu ndi Mulungu pa Mtanda wa Kalvari (Yesaya 53:45; 1 Petro 2:24). Yesu anapereka machiritso kwa ana onse a Mulungu: iwo onse amene avomereza Khristu kukhala Mbuye ndi Mpulumutsi wao. Mu Mateyu 15:26, Yesu anati machiritso ndiwo “mkate wa ana.” Machiritso a Mulungu ndi chimodzi cha zinthu zozizwa zimene Khristu anatichitira pa mtanda.

Gawo lachiwiri ndilo *machiritso a mphamvu*. Awa ndiwo machiritso amene amasonyeza kupezeka kwake kwa Mulungu komanso mphamvu ya Ufumu wa Mulungu. Mulungu akhoza kuchiritsa ngakhale anthu osakhulupirira kapena osatembenuka mtima kudzera mu mphamvu yamachiritso. Kuchilitsidwaku kumachitika pamene Uthenga Wabwino wa Khristu walalikidwa komanso ngakhale usanalalikidwe konse. Mphamvu yochiritsayi imatsimikizira zoonza za kupezeka kwa Mulungu. Mphamvu

yochiritsayi imatchulidwa kuti “zizindikiro ndi zozizwa” mu mabuku a Mateyu, Marko, Luka, Yohane ndi Machitidwe a Atumwi.

### **Zizindikiro ndi Zozizwa**

Mau amenewa amapezeka pafupipafupi m’Chipangano Chatsopano “zizindikiro ndi zozizwa.” Mauwa akupezeka mu Machitidwe 2:22 ndipo akunena za utumiki wa Yesu. Koma mu Machitidwe 2:43 mauwa akunena za utumiki wa mpingo patangopita masiku pang’ono kuchokera patsiku la Pentekoste: “Koma panadza mantha pa anthu onse; ndipo zizindikiro ndi zozizwa zambiri zinachitika ndi atumwi.”<sup>1</sup>

M’Buku Lopatulika, Mau akuti zizindikiro ndi zozizwa nthawi zambiri amagwiritsidwa ntchito pamodzi. Zizindikiro ndi zomwe zimaloza ku chinthu china. “Zizindikiro” (mu chi Herene: Semeion) mauwa m’Chipangano Chatsopano amanena za zinthu zodabwitsa koma zokhala ndi cholinga. Zizindikiro zimasonyeza kuti ufumu wa Mulungu wafika ndipo kuti Uthenga wake (Uthenga Wabwino) ndi woona.

Mu Marko 16:17, Yesu ananenetsa kuti adzalimbikitsa kulalikidwa kwa Uthenga Wabwino ndi zizindikiro. Ndipo mu Marko 16:20 tiwona kuti Uthenga Wabwino umene ophunzira a Yesu analalikira unatsimikizika ndi kulimbikitsidwa ndi zizindikiro. Ifenso lero tikhoza kuyembekezera kuti pamene tirikularikira Uthenga Wabwino, Mulungu adzalimbikitsa uthengawo ndi zizindikiro zotsatirapo.

Mau akuti zozizwa (mu chi Herene: *tera*) amanena za ntchito yodabwitsa ya Mulungu imene imapangitsa oyiwonawa kudabwa. Nthawi ina Yesu anachiritsa m’nyamata yemwe anali ogwidwa ndi ziwanda. Luka 9:43 akulemba kuti anthu “Ndipo onse anadabwa pa ukulu wache wa Mulungu ... pamene onse analikuzizwa ndi zonse anazichita.” Ichi ndi chitsanzo cha kudabwitsika.

---

<sup>1</sup> Muyenere kuwerenganso bwinobwino ndime zina zimene zatchulidwa za “zizindikiro ndi zozizwa.” Ichitu ndi chitsanzo cha kuonetsa mgwirizano wa kufalitsa uthenga mu Chipangano Chatsopano: Machitidwe 4:29-30, 5:12; 6:8; 14:3; Aroma 15:19; Ahebri 2:3-4).

M’Buku la Machitidwe, zozizwa zomwe atumwi anachita zinabweretsa chidwi chachikulu pakati pa anthu:

- anadabwa (2:7; 3:10)
- anathedwa nzeru (2:12)
- anachita mantha (2:43)
- analemekeza Mulungu (4:21)
- anachita mantha akulu (5:5, 11)
- chimwemwe chachikulu (8:8)
- anadabwa (8:13)
- ambiri anakhulupilira Ambuye (9:42 onaninso 1 Akor. 2:4-5).

A Jesse Moon anasanthula mu Buku Lopatulika zolinga zisanu ndi ziwiri za zizindikiro ndi zozizwitsa zomwe zipezeka m’Chipangano Chatsopano. Iwo anati zizindikiro ndi zozizwa:

1. Zinasonyeza ndikutsimikiza kuti Khristu ndiye Mesiya ndipo izo zinapangitsa anthu kuti amukhulupirire Iye (Machitidwe 2:22, Ahebri 2:4);
2. Zinapangitsa anthu kukhala ndi chidwi pa Uthenga Wabwino;
3. Zinasonyeza umboni wonse kuti Khristu ndi Mbuye wa Moyo (woukitsidwa kwa akufa) wa Mpingo;
4. Zinatsimikizira kuona kwake kwa Mau olalikidwa (Machitidwe 4:29-30; 14:3; Aroma 15:19; Ahebri 2:3-4);
5. Zinasonyeza okhulupirira owona komanso chipembedzo choona (Marko 16:15-18; 2 Akor 12:12);
6. Zinakwaniritsa zimene anthu amazifuna;
7. Zinapititsa patsogolo Ufumu wa Mulungu pa dziko lapansi (Machitidwe 5:12-14; 8:5-13).

Zolinga zonse izi za zizindikiro ndi zozizwa ndi zofunika. Ife tiyenera kupemphera moona mtima kuti zizindikiro ndi zozizwazi zikhale mbali imodzi ya utumiki wathu. Zimenezi ndi zofunikira kwambiri masiku ano monga momwe zinali nthawi ya atumwi.

## **Kuonanso Phunziro Mwachidule**

Mulungu watipatsa ife chifungulo chofunikira kuti tifikire nacho dziko lapansi ndi Uthenga Wabwino wa Khristu. Izi ndi kulalikira kodzera mu kudzodzedwa potsatana ndi zizindikiro komanso zozizwa. Tiyenera ife kumvetsa ndi kupitiriza kutumikira mu mphamvu ya Mzimu Woyera. Tikatero tidzaona zotsatira ngati zomwe zinali m'Chipangano Chatsopano. Cholinga chabuku lino ndicho kuti tikwaniritse zotsatira zimenezi. Choncho chidziwitso chanu chatsopanochi chigwirizane ndi chikhulupiriro chanu, komanso kudzichepetsa kwanu ku Mzimu Woyera pamene mutumikira.



## Chaputala 2

# Kulongosolera Utumiki wa Mphamvu

### **Kulimbana kwa Mphamvu m'Chipangano Chakale**

Machitidwe ambiri a kulimbana kwa mphamvu akupezeka poyambilira mu Chipangano Chakale. Pali zitsanzo ziwiri zomwe zikugwirizana ndi mfundonyi. Mose anagonjetsa milungu ya mu Aigupto m'Kulimbana kwa mphamvu. Zotsalira zake ndizo kumasulidwa, ndi mtendere pa ana a Israyeli. Komanso Eliya ndi aneneri a Baala anakumana mu kulimbana kwa mphamvu za uzimuku. Kulimbanaku kunadzetsa chitsitsimutso pa ana a Israyeli Eliya atagonjetsa.

### **Mose Agonjetsa Milungu ya Aigupto**

Timawerenga m'mene Mose anagonjetsera milungu ya m'Aigupto mu Eksodo 5-12. Mulungu anauza Mose kuti ayambe kulimbana ndi mphamvu za Farao kaye. Kulimbanaku kunali kwa pakati pa Mulungu ndi milungu ya Aigupto (Eksodo 12:12). Pomaliza, Paulo anati milunguyo inali ziwanda (1 Akor. 10:19).

A Don Williams akufotokoza za kulimbana kwa uzimuku mu Aigupto. Iwo akuti,

Eksodo 5-12 ikukamba za ntchito za mphamvu za Mulungu, zizindikiro zake ndi zodabwitsa zake ... ichi ndi chitsanzo cha zomwe zinachitika za Kulimbana kwa Mphamvu, zomwe zikuonetsera kuti Mulungu ali ndi

mphavu kuposa milungu ya Aigupto. Pa chozizwitsa chirichonse Mulungu analikugonjetsa molunjika milungu yonse ya Aigupto (1989, p. 82).

A Fred Haltom akugwirizana nazo zakuti Mulungu anali kupereka zozizwitsa kuti agonjetse milungu yonse ya m'Aigupto mwantheradi.

Mulungu anatumiza milili ya magari, achule ndi nsabwe kugonjetsa **Nu**, mulungu wa mtsinje wa Nile; **Hekt**, mulungu wa nthaka (dera); ndi **Geb**, mulungu wa dziko lonse. Anatumiza milili ya zouluka, matenda pa ziweto ndi zotupa pa anthu kugonjetsa **Scarob**, mulungu wa tizilombo ta m'mbewu; **Apis**, mulungu wa ziweto za zimuna; ndi **Thoth**, mulungu wa nzeru ndi maphunziro a mankhwala. Anatumiza matalala, dzombe, ndi mdima kugonjetsa **Ntu**, mulungu wa mlengalenga; **Anubis**, mulungu wa malo olimidwa; ndi **Ra**, mulungu wa dzuwa ndipo pomalizira pake panali kuphedwa kwa ana onse oyamba a mu Aigupto komwe kunali kugonjetsa **Farao** mwini, mfumu ya milungu (1989, p. 103).

Milungu ya Aigupto inali maukuru ndi maulamuliro a ziwanda ndi zimphamvu zake. Mphamvu za ziwandazi zinali kumanga anthu mu ukapolo wa uzimu. Tsono, ulendo wotuluka mu chipsinjo cha Aigupto unaposeera kungomasulidwa ku zowawa za thupi kwa ana a Mulungu. Ulendowu umaonetsera za kumasulidwa kwa Israyeli m'moyo wa uzimu kuchoka ku mphamvu za m'dima. Ichi chinawapatsa iwo ufulu wolambira Mulungu Yehova yekha.

### **Eliya Agonjetsa Aneneri a Baala pa Phiri la Karimeli**

1 Mafumu 18:20-46, amatiuza za nkhani ina ya kulimbana kwa mphamvu. Eliya anakumana ndi ansembe odzala ndi ziwanda za mulungu wa Akanani, Baala. Zochita za ziwanda m'Chipangano Chakale, zimakhudzana ndi kudzadzidwa ndi ziwandazo. Izi zinali chimodzimidzi mu zochitika za ansembe a Baala (Unger, 1971). Eliya sanali kungolimbana ndi chipembedzo cha Baala chokha, koma anali kulimbananso ndi ziwanda zomwe zinapereka mphamvu ku chipembedzochi.

Kulimbanaku kunakhudza kulimbana kwa mphamvu komanso kulimbana kwa choonadi (1 Mafumu 18:21). Mulungu anatsitsa moto kuchokera

kumwamba kuti unyeketse nsembe yodzazidwa ndi madzi. Apa Mulungu anadzionetsera yekha bwino lomwe kuti Iye ndiye wamphamvu kuposa Baala. Panthawi yomweyo Eliya anawauzitsa anthu kuti atsate Mulungu woona ndi wa moyo!

Kulimbana kwa mphamvu kumene kukupezeka m’Chipangano Chakaleku, kunaonetsera mphamvu yayikulu ya Mulungu kwa Israyeli komanso ku magulu ena onse a anthu owazungulira. Iye yekha ndiye woyenera ntchito zathu ndi kupembedzedwa.

## **M’mene Yesu Anagwiritsira Ntchito Kulimbana ka Mphamvu**

Kawirikawiri Yesu Khristu amagwiritsa ntchito kulimbana kwa mphamvu mu utumiki wake. Kudzera mu izi, Yesu anadzionetsera yekha kuti anali “wodzozedwa” wochoka kwa Mulungu. Anaonetseranso ufumu wa Mulungu kuti unadza kugonjetsa ufumu wa satana (Luka 11:20). Yesu anagwiritsa ntchito kulimbana kwa mphamvu pa zolinga zinayi.

- kuvumbulutsa cholinga cha utumiki Wake.
- kuthandizira kugwira ntchito yake.
- kuthandizira kuphunzitsa ophunzira ake
- pa kupatsira utumiki wake kwa ophunzira Ake.

Tsono tisanthula cholinga chirichonse pachoka pachokha:

### **Pa Kuvumbulutsa Cholinga cha Utumiki Wake**

Chimodzi mwa zifukwa zomwe Yesu anabwerera ku dziko lapansi ndicho “kuononga mphamvu za m’dierekezi” (1 Yohane 3:8). Ngakhale ziwanda zomwe anali kukumana nazo zinadziwa bwino lomwe za choonadi ichi. Tikuchipeza choonadi ichi mu Marko 1:23-24a:

*Ndipo pomwepo panali munthu m’sunagoge mwao ali ndi mzimu wonyansa; ndipo anafuula iye, kuti, “Tiri ndi chiyani ife ndi Inu Yesu wa ku Nazarete? Kodi mwadza kuti mudzationonge ife?”*

Mu Luka 4:18-19, Yesu anavumbulutsa dongosolo la utumiki wake. Utumiki wake udzakhudza madera a kuchitachita asanu ndi limodzi.

1. *Kudzozedwa*. Anatumikira pansi pa kudzoza kwa Mzimu woyera (“Mzimu wa Ambuye ali pa Ine, chifukwa chake Iye anandidzoza ...,”)
2. *Kulalikira*. Analalikira uthenga wabwino kwa otaika (“... *ndiuze anthu wosauka uthenga wabwino.*”)
3. *Kumasula*. Anamasula iwo amene anali omangidwa ku uchimo ndi mphamvu za mdierekezi. (“*Anandituma Ine kulalikira am’singa mamasulidwe ...,*”)
4. *Kuchiritsa*. Anachiritsa odwala. (“... *ndi a khungu kuti apenyenso.*”)
5. *Kutulutsa*. Anatulutsa onse omangidwa mu uzimu, mthupi, mchipembedzo, mchuma kuwasandutsa mfulu (“...*kutulutsa ndi ufulu, wophwanyika.*”)
6. *Kulengeza*. Analengeza kuti nthawi ya kudza kwa ufumu wa Mulungu kuti yafika (“*kulalikira chaka chosankhika cha Mulungu.*”)

### **Pa Kuthandizira Kugwira Ntchito Yake**

Yesu anali kulengeza momveka bwino lomwe kuti anadza kudzagonjetsa ndi kuononga ntchito za mdierekezi. Anaonetsa izi kudzera m’kulimbana kwa mphamvu kumene kunachitika mu utumiki wake.

Utumiki wa Khristu unatsamiri pa magawo awiri a kulalika-kuphunzitsa (kulengeza) ndi kuchiritsa ndi kumasula omangidwa (chionetsero) (onani Mateyu 4:23; 9:35). Iye nthawi zonse anali kuphatikiza ma utumiki awiriwa. Kulimbana kwa mphamvu ndi kulimbana kwa choonadi kunampangitsa kukwanirita cholinga cha utumiki wake.

Utumiki wa Yesu umaonetsa zitsanzo zambiri za machitidwe a kulimbana kwa mphamvu. Tasankhula zitsanzo zinayi zokha mu phunziro ili:

- Kuyesedwa m’chipululu,
- Chozizwitsa chake choyamba cholembedwa mu Uthenga Wabwino wa Marko.
- Kulimbana kwake ndi chiwanda cha ku Gerasa.
- Kuchiritsidwa kwa m’nyamata wodzadzidwa ndi ziwanda

**1. Kuyesedwa m'chipululu,** (Luka 4:1-13). Mu kuyesedwa kwake ku chipululu, Yesu analimbana ndi Satana maso ndi maso. Luka anaonetsetsa napeza kuti Yesu anali “wodzadza ndi Mzimu Woyera” pamene anakumana ndi Satana (4:1). Iyi inali nkondo yoyamba ya Yesu Khristu kulimbana ndi mphamvu za mdima. Izi zinachitika kumayambiro kwenikweni kwa utumiki wake. Yesu anamuonetsera mphamvu zake Satana amene ali mfumu ya ziwanda. Nkhani ya kugonjetsedwa kwa Satana iyenera kuti inafalitsidwa mu ufumu wake wonse wa ziwanda mwa msanga. Kuyambira pamenepo, ziwanda zinamudziwa Yasu ndi kuopa mphamvu yake. Mu Marko 1:23-24 muli chitsanzo cha momwe ziwanda zinachitira pomuona Iye.

**2. Chozizwa chake choyamba cholembedwa mu Uthenga Wabwino wa Marko** (Marko 1:21-26; onaninso 3:10-11). Chozizwa choyamba cha Khristu cholembedwa m'buku la Marko ndi chimodzi cha kulimbana kwa mphamvu pa ziwanda kwenikweni mu utumiki wake. Chirichonse chokhudzana ndi kupezeka kwa Khristu chinali chobweretsa chisokonezo ku ziwanda. Ziwandazo zinalira mwa mantha pamene Iye anafika pafupi nazo. Nthawi zambiri Yesu amalamulira ziwandazo kuti “khalani chete” ndipo “tulukani.” Zinalibenso chisankho china koma kungomumvera Iye!

**3. Kulimbana kwake ndi chiwanda cha ku Gerasa** (Marko 5:1-20). Yesu nthawi zambiri anali kukumanizana ndi kuthamangitsa ziwanda. Nkhani ya chiwanda cha ku Gerasa ndi chitsanzo chabwino chopezeka m'buku Lopatulika. Monga mu chitsanzo chachiwiri pamwambapa, munthuyo anaopa kupezeka kwa Yesu. Munthuyo anamasulidwa kwathunthu ndi lamulo la Yesu.

**4. Kuchiritsidwa kwa m'nyamata wodzadzidwa ndi ziwanda** (Marko 9:14-32). Nkhani yomwe ikupezeka mu Marko 9 ikuonetsa Yesu akulimbana komanso kugonjetsa mphamvu za ziwanda. Chiwanda chinayenera kumvera lamulo la Yesu. Patapita nthawi pang'ono, ophunzira ake anafunsa chifukwa chomwe iwo sanathe kutulutsa chiwandacho. Yesu ananena nawo kuti kusoweka kwawo kwa pemphero<sup>2</sup> ndiko kunapangitsa kuchepa mphamvu zao (9:29).

Yesu anachita zizindikiro, zodabwitsa, ndi zozizwa zambiri mu Utumiki wake wonse. Nthawi ndi malo ofotokozera izi zonse ndiwo achepa. Komabe,

---

<sup>2</sup> “Ndi kusala kudya” (Baibulo la chingelezi la NKJV)

tiyenera tipange utumiki wa Yesu kukhala woyenera kusanthulidwa moyo wathu wonse. Tikhoza kuphunzira zambiri za momwe tingachiritsire odwala ndi kugonjetsa ziwanda potsanzira machitidwe a Yesu.

### **Pa Kuthandizira Kuphunzitsa Ophunzira Ake**

Yesu anadza kudzaononga ntchito za mdyerekezi. Anaphunzitsa ophunzira ake ndi ife tonse kuchita chimodzimodzi. Ichi ndi chifukwa chimodzinso cha zifukwa zimene Baibulo limalongosolera tsatanetsatane zokhudza Utumiki wa Khristu. Limafotokoza momveka bwino za mmene Yesu anachilitsira odwala ndi kumasula a m'singa. Baibulo limatiwonetsa momwe Yesu anatumikilira. Ife, monga anachita ophunzira oyamba, tikhonza kutsanza Iye pakuti tidziwa zomwe anachita.

Mu Luka 9:1-6 ndi 10:1-23, Yesu anatumiza ophunzira ake ku utumiki wa maphunziro. Luka 10:1-12 amatiuza za nthawi yachiwiri yomwe Iye anawatuma. Atabwerako, anakanena kwa Yesu zotsatira za utumiki wawo (10:17) ndipo Iye anatenga nthawi yotalikirapo kuwalangiza. Mu chaputala chotsatira, Yesu anawaphunzitsa momwe angagonjetsere mphamvu za ziwanda (Lk 11:4-26). Werengani ndi kusanthula mofatsa ndime yofunikirayi.

### **Pa Kupatsira Utumiki Wake kwa Ophunzira Ake**

Chimodzi mwa zolinga zofunika za Yesu, chinali “kusamutsa” utumiki wake ndi kuupereka kwa ophunzira ake. Ananeneratu kuti iwo adzakhudzidwa ndi Utumiki wa Mphamvu, monga Iye anakhudzidwira. Yesu anasankha ophunzira khumi ndi awiri nawatuma “kukalalika ndi kukhala ndi ulamuliro wotulutsa ziwanda” (Mk 3:14-15). Anayenera iwo kukhala ndi utumiki wophatikiza, wokhudza kulimbana kwa mphamvu ndi kulimbana kwa choonadi.

Mu Luka 9:1-2, Yesu anatumiza khumi ndi awiriwo ku utumiki. *“Nawapatsa mphamvu ndi ulamuliro pa ziwanda zonse ndikuchiritsa nthenda. Ndipo anawatuma kukalalika ufumu wa Mulungu ndi kuchiritsa anthu odwala.”* Komanso apa tikuona utumiki wake wa chionetsero ndi kulengeza ukutsimikiziridwa. Tikuonanso chitsimikizo monga chomwechi mu Lk.10:17-20.

M'Buku la Marko pa nkhani ya lamulo ili lalikuru, Yesu analamulira mpingo wake kuti unyamule Uthenga Wabwino ndi kufikira nawo ku dziko lonse lapansi. Tsono analonjeza ophunzira ake (ndi ifenso) kuti zizindikiro za

utumiki zidzawatsatira (16:15-18). Ophunzira ake anapita nakakwaniritsa utumikiwo wa kuonetsera ndi kulengeza (16:19-20). Tiyenera kuchita monga awa oyamba anamvera mauwa. Tiyenera kupita mu mphamvu ya Mzimu Woyera, kulalikira Uthenga Wabwino wotsatiridwa ndi zizindikiro.

Yesu anachita chinthu chake chomaliza chakusamutsira utumiki wake kwa ophunzira ake. Anawapatsa kudzoza komweko ngati kumene kunapereka mphamvu ku utumiki wake (Machitidwe 10:38). Yesu anachita ichi pa tsiku la Pentekoste “*ndipo anadzazidwa wonse nayamba kulankhula ndi malilime ena, monga Mzimu anawalankhulitsa.*” (Machitidwe 2:4). Mphamvu yomweyo imene inapatsidwa pa tsiku la Pentekoste ikupezekabe kwa ife lero. Ndi mphamvu iyi, tikhoza nafenso kuchita ntchito za mphamvu za Yesu.

## **Kulimbana kwa Mphamvu mu Utumiki wa Mpingo Woyamba**

Ophunzira analandira mphamvu ya Mzimu pa tsiku la Pentekoste. Kenako anapita nakayesera utumiki monga wa Yesu. Ophunzirawo anaonetsera kuti Ufumu wa Mulungu unadza mu mphamvu yayikulu. Anachita izi kudzera mu zozizwa, zizindikiro, ndi zodabwitsa zomwe anali kuchita.

### **Kuunika Zochitika za Utumiki wa Mpingo Woyamba**

Mpingo m’Buku la Machitidwe unakula mofulumira kwambiri chifukwa cha kupezeka kwa mphamvu ya Mzimu Woyera. Iyi inali mphamvu yomweyo imene inapangitsa Yesu kuchita ntchito yake. Onani mau awa “*nayamba kuzichita ndi kuziphunzitsa*” (Machitidwe 1:1): “*Taonani Teofilo inu mau aja oyamba ndinakuuza, za zonse Yesu anayamba kuzichita ndi kuziphunzitsa.*” Ganizo liri apa ndilakuti mpingo unali kupitiriza utumiki wa Khristu, ndi ntchito zake za mphamvu. Izi ndi zomwe mpingo woyamba unachita.

Zizindikiro ndi zodabwitsa zinali zofunikira kwambiri mu utumiki wa mpingo woyamba. Buku la Machitidwe limaonetsa kuti atumwi anali kutumikira monga Yesu anali kuchitira. Iwo anatsatira kwathunthu momwe Yesu anali kuchitira: chionetsero ndi kulengeza. Mu Utumiki wao munalinso izi:

- Zizindikiro ndi zodabwitsa,
- Machiritso,
- Kutulutsa zidwanda,
- Zozizwa mu chilengedwe ndi mu chakudya,
- Kuukitsa akufa,
- Malilime,
- Uneneri,
- Masomphenya,
- Ndi zozizwa zina.

Zizindikiro ndi zodabwitsa, kuphatikizidwa ndi ulaliki wodzozedwa, zinali kudabwitsa anthu ambiri. Ophunzirawo anali kulalikira Uthenga Wabwino ndi mphamvu, ndipo anthu mazana mazana anali kupulumutsidwa. Zoterezi zingachitike ngati titatsatira machitidwe onga a utumiki wa Yesu.

### **Zitsanzo za Kulimbana kwa Mphamvu mu Utumiki wa Mpingo Woyamba**

Tsono tilingalira zitsanzo ziwiri mwachidule mwa zitsanzo zambiri zomwe zimapezeka m’Buku la Machitidwe. Tsatanetsatane wa zitsanzo izi ziperekedwa mu Chaputala 4.

*1. Pa tsiku la Pentekoste.* Werengani mofatsa Machitidwe 2:1-41), ndipo muyankhe mafunso anayi otsatirawa.

- a. Kodi ndi chionetsero chiti cha machitachita a mphamvu ya Mulungu chomwe chinachitika pa tsiku la Pentekoste?
- b. Kodi khamu la anthu linachitapo chiyani pa kutsanulidwa kwa Mzimu Woyera pa anthu chikwi kudza khumi ndi awiri?
- c. Kodi kukumana kwa choonadi kunalipo. Ngati inde, fotokozerani mwachidule.
- d. Kodi zotsatira zake za kulimbana kwa mphamvu uku zinali zotani?

*2. Machiritso pa khomo la Kachisi lotchedwa lokongola.* Werengani mofatsa Machitidwe 3, ndipo muyankhe mafunso anayinso otsatirawa:

Chaputala 2: Kulongosolera Utumiki wa Mphamvu

- a. Kodi ndi chiwonetsero chanji cha machitachita a mphamvu ya Mulungu chomwe chinachitika pa khomo la kachisi lotchedwa Lokongola?
- b. Kodi khamu la anthu linachitapo zotani pa chionetsero cha mphamvu ichi?
- c. Kodi kukumana kwa choonadi kunalipo apanso. Ngati inde, fotokozerani mwachidule.
- d. Kodi zotsatira zake za kulimbana kwa mphamvu uku zinali zotani?



### Chaputala 3

# Utumiki wa Mphamvu ndi Ufumu wa Mulungu

## Kutanthauzira Ufumu wa Mulungu

Kodi mumaganiza chiyani pamene mumva mau akuti *Ufumu wa Mulungu*? Akhristu ambiri samvetsa nkhani ya phunziroli. Izi ndi zomvetsa chisoni. Ufumu wa Mulungu ndi chimodzi mwa nkhani zikuluzikulu za Chipangano cha Tsopano. Kumvetsetsa Ufumu wa Mulungu ndikofunikira kwambiri pa utumiki wa mphamvu.

### Kulamulira kwa Mulungu

Mau akuti *ufumu* munkhaniyi sakutanthauza malo kapena chigawo cha dera. Koma mauwa akulongosola za **kulamulira** (ulamuliro) kwa mfumu. Ufumu wa Mulungu ukhoza kutanthuzidwa mosavuta pongonena kuti kulamulira kwa Mulungu. Ndi ulamuliro **wopambana** wa Mulungu pa chilengedwe Chake. Nthawi zambiri timati Ufumu wa Mulungu wafika. Apa timatanthauza kuti Mulungu wafika kukhazikitsa ulamuliro Wake pa dziko.

### Nthawi Ziwiri za Ufumu wa Mulungu

Timanena za Ufumu wa Mulungu mu nthawi yalero ndi yamtsogolo. Ufumu ulipo lero tsopanolino - nthawi yalero. Komanso ufumu ulikudza – masiku amtsogolo. “Tikhoza kunena momangilira motere: ufumu ulidi pakati pathu, koma osati wonse. Apa ndiye kuti,okhulupilira, amakhala mu ufumu wadza ndi ulikudza. (Williams, 1989, p.82).

1. *Ufumu wa Mulungu uli pakati pathu kale.* Iwo unadza mu umunthu wa Yesu Khristu ndi kupyolera mu utumiki wake (Luka 17:20-21). Ufumu unadzanso ndi mphamvu yayikulu pa Tsiku la Pentekoste (Machitidwe a Atumwi 1:8; onaninso Marko 9:1). Apa ndi pamene Mzimu Woyera anatsanulidwa mu mpingo. Kupyolera mu zimene zinachitikazi pa Pentekoste, Yesu anasamutsira utumiki Wake wa ufumu ku mpingo.

Anthu tsopano akukangamira [Ufumu wa Mulungu] kapena kukangamizidwa nao mwaphamvu (Mateyu 11:12-13; Luka 16:16). Kulandidwa kwa ulamuliro wa Satana kunayamba kale, mphamvu ya nyengo ya kutsogolo ikugwira kale ntchito yake mu dziko tsopano lino, ndipo mdalitso la umesiya liripo kwa iwo amene akuvomereza kulilandira. (kuzmic, 1988, p. 523)

2. *Ufumu wa Mulungu siunabwere wonse.* Udzabwera wonse mokwanira pamene Khristu adzafikanso. (Chivumbulutso 11:15). Ndi zoonza kuti Ufumu wa Mulungu unafika kale. Kugweredwa ndi kulandidwa kwa ufumu wa Satana kunayamba kale. Tikhonza kunena kuti kugweredwa kumeneku ndi gawo la *lero* la Ufumu. Komabe, Khristu sanakhazikitse ufumu wake wonse pa dziko lapansi. Izi zidzachitika pamene adzabwera, “ndi mphamvu ndi ulemerero waukuru” Mateyu 24:30). Pa nthawiyo, Khristu adzagonjetsa mdyerekezi, ndipo adzakhazikitsa kwathunthu ulamuliro wake pa dziko. Timatchula gawo ili kuti *lisanafike* (lamtsogolo) la Ufumu.

Izi ndi choonadi chozama: Ufumu wafika (tsopano), ulikudzabe (usanafike). Izinso zimathandiza kulongosolera za zimene tikumana nazo masiku a lero lino. Zimalongosolanso za chigonjetso chathu pa Satana ndi zimphamvu zake (tsopano). Zimalongosolanso kupitilira kwa nkhondo yathu ndi iye (usanafike). Zimalongosolanso za chifukwa chimene ambiri amachiritsidwira modabwitsa (tsopano), komabe ambiri ndikumadwalabe ngakhale kumwalira kumene (usanafike). Tiri ndi mphamvu pa ziwanda (tsopano), komabe Satana akupitilira kulamulira ndi kuzunza anthu ochulukana (usanafike). Ufumu wa Mulungu unafika mu gawo chabe. Komabe, tsiku lina udzafika wonse mokwanira. Tsopano lino tiri nazo mphamvu ndi ulamuliro pa ziwanda, Nthawiyo mphamvu zonse za mdima zidzagonjetsedwa kwathunthu ndi komaliza.

## **Kudza kwa Ufumu wa Mulungu**

### **Yesu Anabwera Kulengeza Kulamulira kwa Mulungu**

Nkhani ya Ufumu wa Mulungu inali nkhanu ya pa phata pa maulaliki a Khristu. “*Kundiyenera Ine ndilalikire Uthenga Wabwino wa Ufumu wa Mulungu ku midzi yinanso:chifukwa ndinatamidwa kudzatero*” (Luka 4:43).<sup>3</sup> Peter Kuzmic analemba:

Nkhani ya Ufumu wa Mulungu imatenga malo ofunikira zedi mu kuphunzitsa ndi mu utumwi wa Yesu. Ganizo la mtengo wake ili la Khristu, monga lakhala likutchulidwira, ndi nkhanu yayikuru ya kulalikira ndi chifungulo ku kumvetsetsa utumiki wake wa Khristu. (1988,p. 522)

Yesu anayamba utumiki wake pa kulengeza, “*Nthawi yakwanira ndipo Ufumu wa Mulungu wayandikira*” (Marko 1:15) Apa ndiye kuti analengeza kufika kwa ulamuliro wa Mulungu pa dziko lapansi. Ufumu wa Mulungu tsopano unali wakufikirika ndi anthu onse amene angafune kuulandira. “Chaka chosankhika cha Ambuye” (Luka 4:19) chinali tsopano chitafika. Mulungu anafika ku dziko lapansi mu umunthu wa Yesu Khristu kudzatenga zonse zimene ziri zake. Izi zinabweretsa mdalitso wa kumwamba kwa munthu (Luka 2:10-14).

Mu mabuku a Uthenga Wabwino, Ufumu wa Mulungu inalinso nkhanu yayikulu kwa ophunzira pamene amalalikira. Yesu anawauza kulalikira Ufumu wa Mulungu ndi kuonetsera mphamvu yake (Mateyu 10:7; Luka 9:2; 10:9-11).

### **Kubwera kwa Ufumu wa Mulungu Kumatsatirana ndi Kulimbana**

Kwa nthawi yoyamba Ufumu wa Mulungu unadza mu umunthu wa Yesu Khristu. Tsopano lino uli kupitilira kupyolera mu mpingo Wake, modzadzidwa ndi Mzimu Woyera. Satana, mbava ndi wonyenga, mothedwa nzeru adakatsutsanabe ndi Mulungu. Kuma Mulungu anabwera kudzatenga molanda zonse zimene mdyerekezi anaba. Kupitilira kwa Ufumu wa Mulungu

---

<sup>3</sup> Onaninso Mateyu 4:23; Marko 1:14-15; Luka 8:1, 9, 9:11.

kuli kutsatiridwa ndi kulimbana kwakukuru ndi ufumu wa Satana (onani Aefeso 6:12).

## **Ufumu wa Mulungu Umabwera ndi Mphamvu**

Ufumu wa Mulungu pakudza siubwera mwamantha kapena momapepesa ayi. Umabwera ndi mphamvu! Paulo anati, *“Pakuti Ufumu wa Mulungu suli m’mau, koma mumphamvu”* (1 Akorinto 4:20). Kunena moona, iyi ndi njira yokhaya imene Ufumu wa Mulungu umabwerera. Satana mwamakani amayesa kukaniza Ufumuwa ndi Mulungu kulamulira. Ufumu wa Mulungu uyenera kupitabe patsogolo mu mphamvu. Wonyengayo ayenera kukankhidwira kunja ndi mphamvu.

*Koma ngati Ine ndimaturutsa ziwanda ndi mphamvu yake ya Mzimu wa Mulungu, pomwepo Ufumu wa Mulungu unafika pa inu. Kapena akhoza bwanji munthu kulowa m’banja la munthu wolimba, ndi kufunkha akatundu ake, ngati iye sayamba kumanga munthu wolimbayo? Ndipo pomwepo adzafunkha za m’banja lake. (Mateyu 12:28-29)*

Mpingo ndi chida cha Mulungu cha kupititsira ufumu Wake patsogolo. Yesu analankhula za tsiku limene ophunzira Ake adzaona Ufumu wa Mulungu ukubwera mu mphamvu: *“Ndithu ndinena ndi inu kuti, Alipo ena akuimilira pano, amene sadzalawa imfa konse, kufikira akaona Ufumu wa Mulungu utadza ndi mphamvu”* (Marko 9:1). Zoonza zake ndi kuti ophunzira anali ataona Ufumu wa Mulungu uli kupita patsogolo mwa mphamvu mu utumiki wa Khristu. Komabe, Marko 9:1 akulongosola za nthawi ya patsogolo. Yesu amalankhula za zimene zidzachitika ena mwa anthuwo asanamwalire polingalira za Tsiku la Pentekoste. Pa tsikulo, mpingo Wake udzavekedwa ndi mphamvu yochokera kumwamba (Luka 24:49).

Ufumu wa Mulungu uli *kupitilirabe* kudza mu mphamvu. Izi timazona nthawi zonse pamene tiona wina adzadzidwa ndi Mzimu Woyera, kapena kukhudzika ndi Mzimuyo.

## **Zizindikiro za Kudza kwa Ufumu**

Zizindikiro, zodabwitsa ndi zozizwa zimachitira umboni kuti Ufumu wa Mulungu uli pakati pathu. Zimaonetsanso **chithunzi cha mtsogolo** cha zimene

zidzachitike pamene Ufumu wa Mulungu udzafika mu mphamvu yonse. Mwa chitsanzo, machiritso a umulungu amapereka chithunzi cha kutha kwa kuzunzika konse ndi matenda (Chivumbulutso 21:4). Kuturutsa ziwanda kumapereka chithunzi chakuonongedwa kwa Satana komaliza pa nthawi imene Yesu adzabweranso (Chivumbulutso 20:10).

Yesu anaphunzitsa ophunzira ake kupemphera motere, “*Ufumu wanu udze*” (Mateyu 6:10). Mukutero, amawaphunzitsa iwo (ndi ife) kupemphera makamaka pa zinthu zitatu izi:

1. *Chipulumutso*. Tiyenera kupemphera kuti anthu apulumutsidwe. Ufumu wa Mulungu umabwera kwa munthu payekha payekha pamene iye abadwa mwatsopano. Izi ndi zimene Yesu anatanthauza pamene anati, “*Ufumu wa Mulungu uli m’kati mwa inu*” (Luka 17:21b).

2. *Zigonjetso za mu moyo wa uzimu ndi wa thupi*. Tiyenera kupemphera kuti anthu adzadzidwe ndi Mzimu Woyera, achiritsidwe ndi kuomboredwa ku kuzunzidwa ndi ziwanda. Ufumu wa Mulungu umadza ndi mphamvu pamene anthu alandira mphamvu ya Mzimu. Izi zimaonekeratu poyera pamene anthu amasulidwa ndi mphamvu ya Mulungu (Mateyu 12:28; Luka 10:9; 11:20).

3. *Kubweranso kwa Khristu*. Tiyenera kupemphera kuti Yesu abwerenso kachiwiri (Chivumbulutso 22:20). Iye akubwera kudzagonjetsa Satana ndi kukhazikitsa Ulamuliro Wake wopambana mu dziko lapansi. Apa ndipo pamene Ufumu wa Mulungu udzafika wonse mu chidzalo chake.

## **Kulalika Uthenga Wabwino wa Ufumu wa Mulungu**

### **Kuitanidwa Kukulalikirira Uthenga Wabwino wa Ufumu wa Mulungu**

Yesu anatuma ophunzira ake kukalengeza kuti Mulungu wafika kudzakhazikitsa Ufumu Wake. “*Ndipo Uthenga uwu Wabwino wa Ufumu udzalalikiidwa pa dziko lonse lapansi, ukhale mboni kwa anthu a mitudu yonse; ndipo pomwepo chidzafika chimaliziro*” (Mateyu 24:14).

Ufumu wa Mulungu unali nkhani yayikulu ya pa phata pa utumiki wa Khristu. Mabuku a Uthenga Wabwino anayi aja onse amalankhula za Ufumu nthawi zoposera makumi asanu ndi anayi. Yesu atauka kwa akufa, anakhala masiku makumi anayi ndi ophunzira akulankhula nawo za Ufumu wa Mulungu (Machitidwe a Atumwi 1:3). Anawaonetsera kufunikira kwakuti iwo adzadzidwe ndi Mzimu Woyera (Machitidwe a Atumwi 1:4-5). Anakambanso

za kuchitira umboni mu mphamvu ya Mzimu (machitidwe a Atumwi 1:8). Yesu anatuma omutsatira ake kukalalikira Uthenga Wabwino wa Ufumu wa Mulungu. Pamene anatuma khumi ndi awiri, anawapatsa malangizo apaderadera:

*Ndipo Iye anaitana pamodzi khumi ndi awiriwo nawapatsa mphamvu ndi ulamuliro pa ziwanda zonse, ndi zakuchiritsa nthenda zonse. Ndipo anawatuma kukalalikira Ufumu wa Mulungu, ndi kuchiritsa anthu odwala. (Luka 9:1-2)*

*Ndipo pamene mulikupita lalikirani kuti, Ufumu wa Kumwamba wayandikira. Chiritsani akudwala, ukitsani akufa, konzani akhate, turutsani ziwanda: munalandira kwaulere, patsani kwaulere. (Mateyu 10:7-8)*

Kwa ophunzira makumi asanu ndi awiri, anawapatsa malamulo ofanana. *“Ndipo chiritsani odwala ali momwemo nimunene nao, Ufumu wa Mulungu wayandikira kwa inu” (Luka 10:9a).*

Ufumu wa Mulungu unapitirira kulengezedwa mu buku lonse la Machitidwe a Atumwi. Apo tikuona mpingo ukulalikira ndi kuphunzitsa Uthenga Wabwino. Tikutha kuona chitsanzo cha dongosololi mu utumiki wa Filipo ku Samariya. Iye analalikira Khristu (8:5) ndipo anachita zozizwa (8:6). Mu kumangilira tingati, Filipo anali *“wakulalikira Uthenga Wabwino wa Ufumu wa Mulungu ndi dzina la Yesu Khristu” (8:12).*

Mu Aefeso, paulo anaphunzitsa kwa miyezi itatu za Ufumu wa Mulungu (Machitidwe a Atumwi 19:8;20:25). Ndipo ku Roma, *“Nalandira onse akufikira kwa iye, ndi kulalikira Ufumu wa Mulungu, ndi kuphunzitsa za Ambuye Yesu Khristu ndi kulimbika konse (Machitidwe a Atumwi 28:30 b-31).*

### **Kutanthauzira Uthenga Wabwino wa Ufumu**

Kodi Uthenga Wabwino wa Ufumu wa Mulungu umene Yesu anatomizira omutsatira ake kukalengeza ndi chiyani? Matanthauzo osiyanasiyana amapezeka pa mauwa *Uthenga Wabwino wa Ufumu wa Mulungu..* A George Ladd anatanthauzira mauwa motere, *“Nkhani yofunikira ndi yabwino yokhudzana ndi Ufumu wa Mulungu.”* Anaonjezeranso kuti

Uthenga Wabwino ndi Uthenga umene unalalikidwa ndi atumwi mu Mpingo Woyamba.” (1981, p. 59). Ife tikugwirizana ndi kutanthauzira kwa a Ladd, koma tikufuna kuonjezera maganizo ena. Zoonadi kuti Uthenga Wabwino wa Ufumu ndi nkhani yofunikira ndi yabwino ya Ufumu wa Mulungu. Koma ili nkhani yofunikira ndi yabwino kuyilengeza pogwiritsa ntchito *njira zofanana* ndi zimene Yesu ndi atumwi anagwiritsa. Mu maganizo awa, a Tom Marshall anapereka tanthauzo labwino zedi la Uthenga Wabwino wa Ufumu: Uthenga Wabwino wa Ufumu ndi uthenga wabwino wa chipulumutso mophatikizirapo mphamvu yanyengo ilikudza” (1988, p. 51).

Yesu ndi Mpingo Woyamba uja analengeza za kubwera kwa Ufumu wa Mulungu. Mukutero, analengeza za kugonjetsedwa kwa ufumu wa Satana. Mwakuonjezera, anaonetsera mphamvu za dziko lirikudza. Iwo anachiritsa odwala, kuturutsa ziwanda, ndi kupereka zionetsero zina za mphamvu ya Mzimu.

Yesu anatiuza momveka bwino mmene Ufumu wa Mulungu umapitira patsogolo:

*Chilamulo ndi aneneri analipo kufikira pa Yohane; kuyambira pamenepo ulalikidwa Uthenga Wabwino wa Ufumu wa Mulungu, ndipo munthu ali yense akangamira kulowamo. (Luka 16:16)*

*Ndipo kuyambiria masiku a Yohane Mbatizi kufikira tsopano lino, Ufumu wa Kumwamba uli wokangamizidwa, ndipo okangamirawo aukwatula ndi mphamvu. (Mateyu 11:12)*

Tinayitanidwa kuti tilalike uthenga wa Yesu. Komanso tinayitanidwa kukutsanza njira ndi zionetsero za mphamvu ya Ufumu Wake. A Don Williams (1989, p.139) analemba kuti:

Ngati tingatengera maganizo a Yesu pa utumiki, tidzapempherera kutsika kwa kud zodza kwa mphamvu ya Mulungu, ndi Mzimu wa Mulungu pa ife, kufikira ndi kusodza osauka, kumasula omangika mum’nsinga, kubwezeretsa kuona kwa akhungu, kumasula ophyinjika, ndi kulengeza ku dziko, “ichi ndi chaka chosankhika cha Ambuye.” (Luka 4:18-19)

Yesu anatuma khumi ndi awiriwo “*Nawapatsa mphamvu ndi ulamuliro pa ziwanda zonse, ndi zakuchiritsa nthenda. Ndipo anawatuma kukalalikira*

*Ufumu wa Mulungu, ndi kuchiritsa anthu odwala. (Luka 9:1b-2). Kenako, Anatuma makumi asanu ndi awiri kukalengeza za kubwera kwa Ufumu wa mulungu. Anawauza kuti, “Ndipo m’udzi uliwonse mukalowamo, ndipo alandira inu idyani zomwezo akupatsani; ndipo chiritsani odwala ali momwemo nimunene nao, Ufumu wa Mulungu wayandikira kwa inu” Luka 10:8-9a).*

Kodi tikutanthauza chiyani kwenikweni tikamanena za Ufumu wa Mulungu? Ndi kulengeza za nkhani yofunikira ndi yabwino ya Yesu Khristu. Ndipo ndi kulalikira uthenga wa imfa ya Yesu, kuyikidwa m’manda, ndi kuukanso, ndi kubwera kwa Ufumu. Sityenera kulephera kulalikira uthenga uwu wa mphamvu ndi kutsatiridwa ndi zizindikiro zake. Tiyeni molimba mtima tilalikire Uthenga Wake Wabwino! Mwa iwo wokha muli mphamvu ya Mulungu yakutsogolera anthu ku chipulumutso (1 Akorinto 1:18).

## Chaputala 4

# Utumiki wa Mphamvu ndi Kulalikira Uthenga Wabwino

## Chiyambi

Kulimbana kwa mphamvu kuli gawo la kulalikira Uthenga Wabwino wa Khristu. Mu Chaputala chachitatu, tinakambirana za kulalikira Uthenga Wabwino wa Ufumu wa Mulungu. Mu chaputala ichi, tikukuza nkhanayi ndi kulongosolera mmene zimakhudzilana ndi kulimbana kwa mphamvu. Kulimbana kwa mphamvu kunali kofunikira mu utumiki wa Yesu komanso kwa iwo a Mpingo Woyamba uja. Kulimbana kwa mphamvu uku nthawi zambiri kumatsatirana (kutsogolera) ndi maulariki ao. Kulimbana kotereku unali umboni wamphamvu ku choonadi cha uthenga wao. Anthu ochuluka anatembenuka mitima potsatira kulimbana kwa mphamvuku.

## Zionetsero ndi Kulengeza

Zochitika ziwiri zofunikira pochitira umboni Uthenga Wabwino ndizo zionetsero ndi kulengeza. *Zionetsero* zimakhudzana ndi zizindikiro, zodabwitsa, ndi zozizwa zimene zimatsatirana ndi Uthenga Wabwino. *Kulengeza* kumakamba za kulalikira ndi kuphunzitsa Uthenga Wabwino wa Khristu.

Chimayamba ndi chiti: zionetsero kapena kulengeza? Chilichonse cha ziwirizi chitha kukhala koyamba. Chofunikira kwambiri ndi kuti zonse zipezeke. Pamene mphamvu ya Mulungu ikuwonetseredwa, Uthenga Wabwino umakhala ndi mphamvu yayikulu ndi kuchita koposa mu miyoyo ya anthu. Izi ndizo utumiki wa “chionetsero ndi kulongosolera” mu chiweniweni chake.

### **Zoyambilira Kukhala Zoyambilira**

Yesu anaphunzitsa kuti nthawi zonse poyamba tiyenera kuchita nkondo ya Uzimu ndipo keneko tikhonza kulalikira Uthenga Wabwino wa Khristu mwa ubwino ndi momasuka. Yesu anati:

*Koma ngati Ine nditulutsa ziwanda ndi Mphamvu yache ya Mzimu wa Mulungu, pomwepo Ufumu wa Mulungu unafika pa inu. Kapena akhoza bwanji munthu kulowa m'banja la munthu wolimba, ndi kufunkha akatundu ake, ngati iye sayamba kumanga munthu wolimbayo? (Mateyu 12:28-29).*

Yesu anadziwa kuti tiyenera kupeza “zoyambilira kukhala zoyambilira” pa kulalikira Uthenga Wabwino. Poyamba, tiyenera “kumanga munthu wolimba.” Pamenepo ndiye tikhonza “kutenga zinthu za m’nyumba yake.” Munthu wolimbayu mu Mateyu 12 akuyimira chiwanda cha mphamvu zedi. Chiwanda choterechi chimatha kulamalira munthu payekha, kapena mudzi, kapenanso dera. “Nyumba” yake ndi malo amene chimakhazikitsa ulamuliro wake. “Katundu” wake ndi miyoyo ya anthu a m’udzi kapena dera limene limasungidwa mu m’nsinga zake. Choonadi ichi chikuonetseredwa mu Chithunzi 4.1.

Yesu anati titha kulowa m’nyumba yake ndi kutenga akatundu a munthu wolimbayu. Izi zikutanthauza kuti titha kulanda miyoyo ya anthu amene akusungidwa mu ukapolo wake. Kuti tichite izi, tiyenera kulimbana naye ndi kumugonjetsa.

Ambuye wathu analonjeza kuti iwo onse amene adzakwaniritsa Lamulo Lake Lalikuru adzadzizwika ndi zochitika zapaderadera. Zizindikiro ndi zodabwitsa za utumiki zidzawatsatira iwo (Marko 16:15-18).

Chizindikiro choyamba chimene anachitchula ndicho: “*adzaturutsa ziwanda*” (Marko 16:17). Choncho, udindo wathu woyamba ndiko kugonjetsa

mphamvu ndi maukulu a ziwanda. Ndi pokhapo pamene tingakhonze kulalikira mamasulidwe ndi chipulumutso kwa iwo amene munthu wolimbayu ali kuwasunga mu ukapolo.

**Chithunzi 4.1**  
**“Munthu Wolimba” wa mu Mateyu 12:28-29**

<b>Mutu</b>	<b>Pakukhazikika mwa munthu</b>	<b>Pakulamulira mudzi kapena dera</b>
Munthu wolimba	Chiwanda cha mphamvu kulumulira munthu payekha	Chiwanda cha mphamvu kulumulira mudzi kapena dera la dziko
Nyumba ya munthu wolimba	Munthu payekha kukhala mu ukapolo wa mizimu yoyipa	Mudzi kapena dera kukhala mu ukapolo wa mizimu yoyipa
Katundu wa munthu wolimba	Moyo wamuyaya wa munthuyo	Miyoyo ya muyaya ya anthu a m'mudzimo kapena m'deramo

**Kuphatikiza Mphamvu**

Mu Chaputala choyamba, tinaonamo kuti Khristu anatipatsa zida zonse zimene timazisowa kuti titumikire nazo ndi kuchita bwino. Ziwiri za zida zimenezi ndizo Mzimu Woyera ndi Uthenga Wabwino wa Khristu. Dongosolo losalephera pa kulimbikitsa mukuchitira umboni Uthenga Wabwino wa Khristu laperekedwa mu Chithunzi 4.2.

## Chithunzi 4.2 Dongosolo la Kuphatikiza Mphamvu

Mphamvu ya            Mphamvu ya Uthenga            Zotsatira  
Mzimu Woyera + Wabwino wa Khristu    =    Zodabwitsa

Tsopano tiona mwachidule gawo lirilonse la dongosololi.

1. *Mphamvu ya Mzimu Woyera.* Yesu Khristu anatipatsa ife mphamvu ya Mzimu Woyera. Mu Machitidwe 1:8, Yesu analonjeza kuti tidzalandira mphamvu pamene Mzimu Woyera abwera pa ife. Aliyense amene agawa Uthenga Wabwino wa Khristu ayenera kudzadzidwa ndi Mzimu Woyera.<sup>4</sup> Izi ndi zofunika zedi; tiyenera kudzadzidwa ndi Mzimu Woyera. Tiyeneranso kuphunzira mmene *tingagwiritsire ntchito* mphamvuyi ya Mzimu Woyera mu utumiki.

2. *Mphamvu ya Uthenga Wabwino wa Khristu.* Khristu anatipatsanso chida china cha mphamvu chimene ndi Uthenga Wabwino wa Khristu.<sup>5</sup> Mu Aroma 1:15-16, Paulo analongosola kulimbika mtima kwake mu uthenga wabwino wa Mulungu:

*Chotero, momwe ndingakhonze ine, ndirikufuna kulalikirira Uthenga Wabwino kwa Inunso a ku Roma. Pakuti Uthenga Wabwino sundichititsa manyazi; pakuti uli mphamvu ya Mulungu yakupulumutsa munthu ali yense.*

Paulo analongosola kuti Uthenga Wabwino wa Khristu uli mphamvu ya Mulungu yakupulumutsa. Anawonjezeranso kuti Uthenga Wabwino wa Khristu uli mphamvu ya kulenga chikhulupiliro mwa iwo amene aumva.

---

<sup>4</sup> Onani mu Chaputala 6 kuti muone kulongoledwa konse kwa ubatizo wa Mzimu Woyera ndi utumiki wa mphamvu.

<sup>5</sup> Onani mu Chaputala 3 kuti musanthule tanthauzo la Uthenga Wabwino wa Khristu.

*Chomwecho chikhulupiliro chidza ndi mbiri, ndi mbiri idza mwa mau a Khristu” (Aroma 10:17). Werengani mofatsa nkhani yonse imene mukupezeke chiganizo chimenechi mu Chaputala 10. Mvetsetsani kuti amalankhula za Uthenga Wabwino. Iye ananena kuti Uthenga Wabwino wa Khristu – uli ndi mphamvu yayikulu. Uli nayo mphamvu yayikulu yakubeleka chikhulupiliro mu mitima ya anthu ochimwa!*

Yesu analankhula za chinkhulupiliro ichi – kupangitsa mphamvu mu fanizo Lake la mbeu yomera ndi kukula. Mufanizoli, anafananizira Uthenga Wabwino ndi mbeu.

*Ufumu wa Mulungu uli wotero, monga munthu akataya mbeu panthaka; nakagona ndi kuuka, usiku ndi usana, ndipo mbeu zikamera, ndi kukula, iye sadziwa umo zichitira. Nthaka ibala zipatso zake yokha. (Marko 4:26-28a)*

Monga mbeu, Uthenga Wabwino wa Khristu uli ndi mphamvu yakubereketse zokolola za uzimu. Uthenga Wabwino wa Yesu Khristu ulidi mphamvu yayikulu! Ndipo udzabereka zokolola za uzimu ngati tingaulalikire.

3. *Zotsatira zodabwitsa.* Makulidwe a mpingo wa mu Chipangano Chatsopano anali odabwitsa. Tikhonza kuona makulidwewa mu mavesi atsatana a mu buku la Machitidwe a Atumwi. Werengani ndi kuchonga mavesi amene alembedwa mu chithunzi 4.3. Pamene mukuwerenga, onetsetsani kuti mwatsatira bwino lomwe mmene mpingo unakulira. Mpingowu unayamba ndi anthu okhulupilira 120, ndipo unakula kufikira mazana mazana mu nthawi yochepa zedi. Mphamvu ya Mzimu Woyera, pamodzi ndi kulalikirira Uthenga Wabwino wa Khristu mokhulupirika, kunabweretsa kukula kodabwitsaku.

### **Chithunzi 4.3**

#### **Mavesi mu Machitidwe amene Akulongosola za Kukula kwa Mpingo Woyamba**

1:15 2:41-47 4:4 5:14	6:1-7 8:6 9:35-42 11:21-26	12:24 13:49 14:1,21 16:5	17:4 19:18-26
--------------------------------	-------------------------------------	-----------------------------------	------------------

### **Zionetsero ndi Kulengeza mu Utumiki wa Yesu**

Nthawi zambiri Yesu analalikira Uthenga Wabwino mwakuonetsera mphamvu ya Mzimu Woyera (onani Mateyu 4:23; 9:35).<sup>6</sup> Izi zinatsatiridwa ndi unyinjira wa anthu umene unabwera kwa Iye kudzamvera uthenga (Mateyu 4:24-25; 9:36).

Ambuye wathu anamaliza utumiki wao wa padziko ndi kutumiza owatsatira awo ku utumiki nthawi yao yonse. Anawauza kuti alalikire Uthenga Wabwino ku dziko lonse ndi kuonetsera mphamvu ya Mulungu (Marko 16:15-18). Yesu analonjezanso kuwapatsa mphamvu za umulungu zakuchitira izi. Mphamvuyo idzafika pa iwo mwa kudzadzidwa ndi Mzimu Woyera pa tsiku la Pantekoste (Luka 24:48-49; Yohane 20:21-22; Machitidwe 1:8).

### **Zionetsero ndi Kulengeza m’Buku la Machitidwe a Atumwi**

Mu buku lonse la Machitidwe a Atumwi, tirikuona ndondomeko yomveka bwino ya kuchitira umboni. Mpingo woyamba uja nthawi zonse unalalikira Uthenga Wabwino ndi kuonetsera machitachita a mphamvu ya

---

<sup>6</sup> Onaninso Chaputala 2, gawo II, pa kulongosola kowonjezera za mphamvu ya utumiki wa Khristu.

Mzimu Woyera. Tiyeni tione zitsanzo zinayi za kukumana kwa mphamvu mu Machitidwe a Atumwi. Izi zili: Tsiku la Pantekoste, Petro ndi Yohane pa khomo la kachisi lotchedwa Lokongola, Filipo ku Samariya, ndi Paulo ku Lustra.

### **Tsiku la Pantekoste (Machitidwe 2:1-40)**

Zochitika izi zinayamba ndi chionetsero cha mphamvu ya Mulungu. Miyanda miyanda ya opembedza a Chiyuda ochokera ku mafuko ochuluka anabwera pa tsikulo ku kachisi. Iwo sanabwere kudzamvera Petro akulalikira. Ambiri a Ayuda sanamudziwense iye ngakhale anzake ophunzira ena onse. Koma tsono anamva ophunzira 120 akulengeza za zodabwitsa za Mulungu mu zilankhulo zosiyanasiyana (Machitidwe a Atumwi 2:6-12).<sup>7</sup>

Pa nthawiyo, “kusunthika chikhulupiliro” kwakukuru kunachitika mu mitima ya Ayuda opezekawo (onani Chithunzi 4.4). Malingaliro awo onse anasinthika chifukwa cha chionetsero chimenechi cha mphamvu ndi kupezeka kwa Mulungu. Iwo anali okhudzidwa kwenikweni ndi kulimbana kwa umulungu. Iwo anali okonzekeranso kumva ndi kukhulupilira Uthenga Wabwino wa Khristu. Pamene Petro anayima ndi kulalikirira, khamulo linali ndi chidwi chachikulu ndi zimene amalankhula. Anthu okwana mazana atatu anatsimikizika pa uthenga wa Petro ndipo anavomera pakuitanidwa kukulandira Khristu.

---

<sup>7</sup> Anthu ambiri amakhulupilira kuti ophunzira anali mu chipinda chapamwamba pamene analandira Mzimu Woyera pa tsiku la Pentekoste (Machitidwe a Atumwi 1:13). Mlembi amakhulupilira kuti mwina anali mu bwalo la kachisi pamene Mzimu anatsanulidwa pa iwo (onani Luka 24:53). Ngati anali mu bwalo la kachisi, gulu la anthu ochuluka liyenera kuti linamva “mkokomo wonga ngati chimphepo champhamvu” (Machitidwe a Atumwi 2:2,6). Ndi zotheka kuti khamulo linaonadi malilime onga amoto ogawanika atakhazikika pa ophunzirawo (Machitidwe a atumwi 2:3). Mu mbiri ya Baibulo, mulibe nkhani yowonjezera apa yoti titha kuwerenga ndi kukhala otsimikizika pa nkhaninyi.



*anasamalira zonedwa ndi Filipo” (8:6a). “Koma pamene anakhulupilira Filipo wakulalikira Uthenga Wabwino ndi dzina la Yesu Khristu, (8:12a). Tsono mu Machitidwe a Atumwi akulemba kuti “panakhala chimwemwe chachikulu m’udzimo” (8:8).*

### **Paulo ku Lustra (Machitidwe a Atumwi 14:8-10)**

Paulo anatsatira machitidwe a utumiki-wamphamvu a kukhala ndi zionetsero ndi kulengeza mu Agalatiya mzinda wa Lustra.

*Ndipo pa Lustra panakhala munthu wina wopanda mphamvu ya m’mapazi mwache, wopunduka chibadwire, amene sanayenda nthawi zonse. Ameneyo anamva Paulo alikulankhula; ndipo Paulo pomuyang’anitsa, ndi kuona kuti anali ndi chikhulupiliro cholandira nacho moyo, anati ndi mau akuru, Taimirira. Ndipo iyeyu anazunzuka nayenda.*

Paulo anagwiritsa ntchito mwayi wa chozizwa ichi mukulalikira uthenga (onani 14:7, 15-17). Dongosolo ili linali lokhazikika mu utumiki wake ndipo ndilo analigwiritsa ntchito.

Tikhonza kukhala ndi chidwi chofuna kuona zotsatira ngati izi zalongosoledwa mu Chipangano Chatsopano. Tikhonza kuona izi ngati tingagwiritse ntchito dongosolo la utumiki-wa mphamvu mu utumiki wathu.

## **Zionetsero ndi Kulengeza mu Ziphunzitso za Paulo**

Taona dongosolo la zionetsero kuphatikizirapo kulengeza mu utumiki wa Yesu ndi Mpingo Woyamba. Tionanso izi zikuphunzitsidwa momveka bwino mu makalata a Paulo. Mu Akorinto woyamba, Paulo akulongosola utumiki wake pakati pa Akorinto:

*Pakuti ndinatsimikizika mtima kuti ndisadziwe kanthu mwa inu, koma Yesu Khristu, ndi Iye wopachikidwa. ...Ndipo mau anga ndi kulalikira kwanga sanakhala ndi mau okopa a nzeru, koma m’chionetsero cha*

*Mzimu ndi cha mphamvu kuti chikhulupiliro chanu chisakhale m'nzere ya anthu, koma mu mphamvu ya Mulungu. (1 Akorinto 2:2, 4-5)*

Ali ku Korinto, utumiki wa Paulo unakhazikika pa zinthu ziwiri. Choyamba chinali “uthenga wa Yesu Khristu, ndi Iye wopachikidwa” (1 Akorinto 2:2). Chachiwiri chinali “zionetsero za mphamvu ya Mzimu” (1 Akorinto 2:4). Anawakumbutsa okhulupilira a ku Akorinto kuti “Zizindikilotu za mtumwi zinachitika pakati pa inu, m'chipiliro chonse, ndi zizindikiro, ndi zozizwa, ndi zamphamvu (2 Akorinto 12:12). Mu 1 Akorinto 14:23-26, Paulo anauza mpingo kuti uyembekezere zionetsero za mphamvu ya Mzimu pamene adzalambira.

Paulo analemba kwa okhulupilira a ku Roma zokhudza utumiki wake woyambilira ku Asia. Anawauza kuti utumiki wake unali wodzala ndi zionetsero za mphamvu ya Mzimu:

*Pakuti sindingathe kulimba mtima kulankhula zinthu zimene Khristu sanazichita mwa ine zakumveretsa anthu amitundu, ndi mau ndi ntchito, mu mphamvu ya zizindikiro ndi zozizwitsa, mu mphamvu ya Mzimu Woyera; kotero kuti ine kuyambira ku Yerusalemu ndi kuzungulirako kufikira ku Iluriko, ndinakwaniritsa Uthenga Wabwino wa Khristu. (Aroma 15:18-19)*

Onetsetsani kuti Paulo akuti utumiki wake unaphatikizika ndi “mau ndi ntchito” (Aroma 15:18). Iye anachita “zizindikiro ndi zozizwitsa, mu mphamvu ya Mzimu Woyera,” pamene anakwaniritsa kulalikira konse Uthenga Wabwino wa Khristu (Aroma 15:19).

Paulo anakumbutsanso mpingo wa ku Atesalonika mmene uthenga unafikira kwa iwo. “Uthenga Wabwino wathu sunadza kwa inu m'mau mokha, komatunso mumphamvu, ndi mwa Mzimu Woyera, ndi m'kuchuruka kwakukuru (1Atesalonika 1:5). Apanso tikuona dongosolo la kulengeza kwa Uthenga Wabwino kuphatikiza zionetsero za mphamvu ya Mzimu. Kulumikizana uku kunabweretsa zotsatira zokhalitsa mu Atesalonika – mpingo weni weniwo.

## **Chimangiliro**

Umboni weniweni wa Uthenga Wabwino wa Khristu uli wokhuza magawo awiri. Loyamba ndilo la zionetsero za mphamvu ya Mulungu. Lina ndilo kulengeza Uthenga Wabwino momveka bwino. Tiyenera kuphunzira kugwiritsa ntchito njira zonse izi ziwiri. Ndi pokhapo pamene utumiki wathu ungakhale wopindula.



**Gawo II**  
**Kukonzekera Utumiki wa**  
**Mphamvu**



## Chaputala 5

# Kukonza Utumiki wa Mphavu

## Zinthu Zofunikira mu Utumiki wa Mphamvu

Tsopano tiyamba kusanthula Gawo lachiwiri: “Kukonzekera Utumiki Wamphamvu.” Onse ofuna utumiki wamphamvu ayenera kuyika nzeru zao zonse pa thandizo la iwo eni ndi pa chikonzero chao.

Kodi ndi zinthu ziti zimene ziri zofunika mu utumiki wamphamvu? Kodi ndi kukonzekera kuti kwapawekha kumene kuli kofunikira mu utumiki wopambana wamphamvu? Chaputala ichi chiyankha mafunso awa.

Zinthu zambiri zimathandiza mukutukuka kwa utumiki wamphamvu. Muchigawo chino tikambirana zinthu zofunika zisanu. Izi ndi kudzoza, chikhulupiliro, kulimba mtima, kutsogozedwa ndi umulungu, ndi kudzichepetsa.

### **Kudzoza**

Chinthu choyamba chofunikira kwambiri mu utumiki wamphamvu ndi kudzoza. Mau akuti kudzoza amatanthauza kupezeka kodziwikiratu kwa Mzimu Woyera. Kudzoza kumabwera pomwe Mzimu Woyera atsikira pa okhulupilira yemwe ali mu utumiki. Zitsanzo zina za m’Baibulo za kudzoza kotereku ziperekedwe. Kudzoza kwa Mzimu kunatsikira pa Petro pamene iye ndi Yohane anakumana ndi atsogoleri a chilamulo cha Chiyuda. Iwowa amadzudzulidwa chifukwa chochiritsa munthu wolumala ndi kulalikira Uthenga Wabwino mu bwalo la kachisi. Koma Petro anachita chiyani? *“Pomwepo Petro, wodzala ndi Mzimu Woyera anati kwa iwo . . .(Machitidwe a Atumwi 4:8).*

Onetsetsani nusu yoti “wodzala ndi Mzimu Woyera” yomwe yatengedwa pamwambapa. Nthawiyi sikanali koyamba kuti Petro adzodzedwe ndi Mzimu Woyera. Izi zinachitikanso pa Tsiku la Pentekoste pamene kupezeka kwapaderadera kwa kudzoza kwa Mzimu kunafikira pa iye nalankhula kwa atsogoleri a chilamulo cha Chiyuda. Chochitikachi kunali kukwaniritsa ulosi wa Yesu mu Luka 12:11-12. A Don Stamps (1990, p. 236) analemba kuti: “Petro analandira kudzazidwa kwatsopano kwa Mzimu Woyera komwe kunabweretsa mwadzidzi, nzeru ndi kulimba mtima kuti anene choonadi cha Mulungu.” Uku kunali kudzoza kwa Mzimu Woyera.

Kenako tsiku lomwelo, Petro ndi Yohane anabwerera ndi kukauza okhulupilira anao chochitikacho. Kudzaza kwa Mzimu kunatsikira pa okhulupilira pomwe anapemphera.

*Ndipo m'mene anapemphera iwo, panagwedezeka pamalo pamene anasonkhanirapo; ndipo anadzazidwa onse ndi Mzimu Woyera, nalankhula mau a Mulungu molimbika mtima. (Machitidwe a Atumwi 4:31)*

Onse anadzazidwanso kapena kudzozedwa ndi Mzimu Woyera. Kudzozedwaku kukufotokozedwanso m'mavesi ena awiri apatsogolo pofuna kuonetsa mphamvu yakuchitira umboni: “*Ndipo atumwi anachita umboni ndi mphamvu yayikuru za kuuka kwa Ambuye; ndipo panali chisomo chachikulu pa iwo onse*” (Machitidwe a Atumwi 4:33). “Chosomo chachikulu” chomwe chinatsikira pa iwo kunali kudzoza kwa Mzimu. Kudzozedwaku kumabweretsa mphamvu yayikulu ya uzimu.

Stefano anali munthu wodzala ndi chikhulupiliro komanso Mzimu Woyera. Mu Machitidwe a Atumwi 6 timawerenga za kudzoza kwake ndi Mzimu Woyera.

*Ndipo Stefano, wodzala ndi chisomo ndi mphamvu, anachita zozizwa ndi zizindikiro zazikuru mwa anthu ... Ndipo sanathe kuilaka nzeru ndi Mzimu amene analankhula naye. (Machitidwe a Atumwi 6:8,10)*

Ayuda anatha kuona kudzozedwaku ndi Mzimu Woyera pa nkhope ya Stefano. *Ndipo anapenyetsa onse akukhala m'bwalo la akulu, naona nkhope yake ngati nkhope ya mngelo: (Machitidwe a Atumwi 6:15).*

Kudzoza kunamufikiranso Paulo pa chilumba za Pafo. Mzimu Woyera unamuululira zakuti chiweruzo cha Mulungu chidzafikira pa wamatsenga, Elima.

*Koma Saulo, ndiye wodzadzidwa ndi Mzimu Woyera, anampenyetsa iye, nati, Wodzala ndi chinyengo chonse ndi chenjerero lonse iwe, mwana wa mdierekezi, mdani wa chilungamo chonse, kodi sudzaleka kuipsa njira zolunjika za Ambuye? Ndipo tsopano, taona, dzanja la Ambuye liri pa iwe, ndipo udzakhala wakhungu wosapenya dzuwa nthawi. Ndipo pomwepo lidamgwera khungu ndi mdima; ndipo anamukamuka nafuna wina womgwira dzanja. (Machitidwe 13:9-11)*

Masiku ano, anthu ambiri amasilira kutumikira mu mphamvu ya Mzimu Woyera monga Akhristu a mpingo woyamba aja. Kuti akwaniritse chokhumba chawo ayenera kuphunzira kuyenda mu Mzimu. Nthawi zonse ayenera kukhala okonzeka kudziyeleka ku chitsogozo ndi chitetezo cha Mzimu woyera.

### **Chikhulupiliro**

Chikhulupiliro chamatanthauzidwa mu njira zambiri. A Martin Luther anachitcha “dzanja lomwe litambasuka ndi kulandira chomwe Mulungu wapereka.” A Jeter akuti,

Chikhulupiliro mwa Yesu ndi Kusakayika mwa Yesuyo. Ndikikhulupilira kuti Iyeyo ndi amene amati ndi Iyeyo, ndipo adzapanga chomwe wanena kuti adzapanga. Chikhalidwe (chikhulupiliro cha chikhalidwe/belief) chili chosachitachita pamene chikhulupiliro pa chokha chili chochitachita nthawi zonse. (1977, p. 173).

Mlembi wina analemba kuti:

Chikhulupiliro chitanthauza kuti uli wokhutitsidwa kuti chomwe Yehova analonjeza, ndi chomwe unapempha, ndi chako ndithu, ndipo wachilandira (ngakhale usanachilandire konse, kapena kuchiona kaya kuchimva chabe). (Osborn, 1955, p. 169).

Pano tikumasulira chikhulupiliro ngati luntha lakukhoza kudalira Mulungu pa zozizwa. Chikhulupiliro choterecho chimayang’ana mwa tcheru kwa Mulungu kuti atsimikizire mau ake mwa kuonetsera zizindikirozotsarapo. Izi zikusonyezadwa mu chilakolako cha Petro pomwe anapempha chilolezo kuti nayenso ayende pamadzi.

*Ndipo Petro anayankha Iye nati, Ambuye ngati ndinutu, mudiuze ndidze kwa Inu pamadzi. Ndipo Iye anati Idza. Ndipo Petro anatsika m’ngalawa, nayenda pamadzi, kufika kwa Yesu. (Mateyu 14:28-29)*

Chikhulupiliro chinawalolo Petro ndi Yohane kuti alamulire munthu wolumala pa kachisi kuti ayende. “*Tiyang’ane ife!*” (Machitidwe a Atumwi 3:4) anamuza wolumalayo. Iwo anali ndi chomwe wolumalayo amachisowa (machiritso) ndipo anali ndi chikhumbo chakuti apereke yankho la chosowachi.

### **Kulimba Mtima**

Kulimba mtima ndi chisankho chakupanga ukaziotche wa mu uzimukapena kuti kuika moyo wako wa uzimu pa chiswe. Ukaziotche uwu ungazetse kulephera ndi mnyozo nthawi zinangati pali kulephereka. Tikuwona kulimba mtima kotereku mu utumiki wa Paulo ku Lustra. Mu uzimu wake Paulo anadziwa kuti wolumala wina anali ndi chikhulupiliro chofuna kuchiritsidwa. Izi zinali zodabwitsa popeza munthuyo anali asanayendepo chiyambire. Paulo anasenza ukaziotche ndipo anafuula.

*Taimirira. Ndipo iyeyu anazunzuka, nayenda (Machitidwe a Atumwi 14:10).*

Nanga kunakakhala kuti munthuyo sanayende? Paulo akananyozeka. Utumiki wakenso ku Lustra ukanathera pomwepo. Koma Paulo analimba mtima mu chikhulupiliro, nayika maganizo a kupephera pamalo angozi. Ndipo bamboyo anachiritsidwanthawi yomweyo. Chitsitsimutso chopambana chinabuka mumzindawo monga mwa chotsatira cha chozizwa chimenechi. Kulimba mtima kotereku kungabwere ngati munthu adzipereka kotheratu kwa Mulungu. Zimangofunika kusakayikira Mau komanso kudzoza kwa Mzimu Woyera.

Utumiki wamphamvu uli ndi ukaziotche wake. Sitikhala opambaniratu nthawi iliyonse tipempherera odwala kuti achire. Sitingapambane nthawi zonse pomwe tikulimbana ndi asilikari a Satana ngakhale kuti ndi kofunika kutero nthawi zonse. Koma onse omwe amaziritisa utumiki wao kapenanso kuchita mantha sadzakhala ndi utumiki wamphamvu ndi wopambana. Chipambano chimabwera kwa okhawa omwe asenza ukaziotche nayika moyo wao pachiswe nachita mu chikhulupiliro ndi kulimba mtima.

### **Chitsogozo cha Umulungu**

Chitsogozo cha umulungu ndi chofunika chachinayi mu utumiki wamphamvu. Kulingalira chifuniro cha Mulungu mu chinthu china chake kuyenera kudza kulimba mtima kusanafike. Yehova sadzadalitsa ntchito iliyonse yochitidwa kunja kwa chifuniro chake. Mtumiki wodzazidwa ndi Mzimu Woyera ayenera kufunafuna mayankho kosalekeza a mafunso otsatirawa:

1. Kodi chifuniro cha Mulungu ndi chiyani mu nkhaniyi?
2. Kodi Mulungu amafuna kuyenda motani?
3. Kodi Mulungu akupanga chiyani?
4. Ndingachite bwanji ndi motani kuti ndigwirizane ndi chifuniro chake?

Mafunso awa angayankhidwe ndi Mulungu wathu wakumwamba mwini wake. Mzimu wake mwa ife adzatipatsa mayankho ake.

Yesu ndi chitsanzo chathu chabwino cha utumiki wopambana. Mbuye wathu sanatumikire mwa Iye yekha, koma motsatira chifuniro cha Atate ake nthawi zonse. Ndipo amatsogozedwa ndi Mzimu Woyera womwe unamudzadza. Mosamalitsa, werengani ndi kuganizira ziganizo izi zochokera kwa Ambuye wathu:

*Pamenepo Yesu anayankha nati kwa iwo, Indetu, indetu, ndinena kwa inu, sakhonza Mwana kuchita kanthu pa yekha, koma chimene aona Atate achichita, ndicho. Pakuti zimene Iye azichita, zomwezo Mwananso azichita momwemo. Pakuti Atate akonda Mwana, namuonetsa zonse*

*azichita yekha: ndipo adzamuonetsa ntchito zoposa izi, kuti mukazizwe.*  
(Yohane 5: 19-20)

*Chifukwa chake Yesu anati, ... pomwepo mudzazindikira kuti Ine ndine,  
ndipo sindichita kanthu kwa Ine ndekha, koma monga anandiphunzitsa  
Atate, ndilankhula izi.* (Yohane 8:28)

*Pakuti sindinalankhula mwa Ine ndekha; koma Atate wondituma Ine,  
yemweyu anandipatsa Ine lamulo, limene ndikanene, ndi limene  
ndikalankhule .... monga momwe Atate wanena ndi Ine, momwemo  
ndilankhula.* (Yohane 12:49, 50b)

Yesu ananena ndi kuchita zokhazo zomwe Atate anamuza kuti akanene ndi kuchita. Nkhani ya pa Yohane 5:1-20 ikufotokoza mwatchutchutchu za zimenezi. Anthu ambiri olumala amakhala pa thamanda la Betsida tsiku ndi tsiku (Yohane 5:4). Koma Yesu anachiritsa m’modzi yekha wa iwo (Yohane 5:8). Kodi ndi chifukwa chiyani anachiza munthu m’modzi yekhayu? Iye sanachize wina osati ameneyu bwanji? Bwanji sanachize onsewo? Yesu anasankha munthuyu chifukwa amatsatira zomwe Atate anamuza. (Yohane 5:19-20). Mu uzimu, Mwana anaona zomwe Atate amachita ndipo anachita mogwirizana ndi Atate ake. Ichi chinali chinsinsi chimodzi cha utumiki wamphamvu wochiritsa wa Ambuye wathu. Ifenso tiyenera kutha kumva Mau a Atate ndikudziwa chomwe akufuna.

Wina anati, “Utumiki wamphamvu ndi wophweka. Chofunika ndi kumva Mau a Atate ndi kuwagonjera.” Ndipo ndi zoonadi – tikangozindikira chomwe Atate akuchita. Tikatero tidzachita mogwirizana ndi zolinga za Atate. Tikambirana mozama bwino za nkhanayi ya chotsogozo cha umulungu mu Chaputala 9

## **Kudzichepetsa**

Kudzichepetsa ndi chikwaniritso chodziona tokha monga momwe Mulungu amationera – monga momwe tiliri. Paulo analemba zokhudzana ndi kudzichepetsa mu Aroma 12:3: “*Ndiuza munthu ali yense wa inu, kuti asadziyese koposa kumene ayenera kudziyesa; koma aganize modziletsa yekha.*” Analimbikitsa okhulupilira kuti azikhala odzichepetsa – osakhala odzikuzi ndi kuziyesa okha kuti ndiofunikira zedi. “*Musachite kanthu monga*

*mwa chotetana, kapena monga mwa ulemelero wopanda pake, komatu ndi kudzichepetsa mtima, yense ayese anzache oposa iye mwini” (Afilipi 2:3).*

Paulo anamangiliro mkota wa chiphunzitso chake cha kudzichepetsa mu Afilipo 2:5. *Mukhale nao mtima m’kati mwanu umeneso unali mwa Khristu Yesu.”* Ndipo tsono analongosola za kudzichepetsa kwa Yesu:

*Ameneyo pokhala nao maonekedwe a Mulungu, sanachiyesa cholanda kukhala wofanana ndi Mulungu koma anadzikhunthula yekha, natenga maonekedwe a kapolo, nakhala m’mafanizidwe a anthu; ndipo popezedwa m’maonekedwe ngati munthu, anadzichepetsa yekha, nakhala womvera kufikira imfa, ndiyo imfa ya pamtanda! (Afilipi 2:6-8).*

Mu kupita kwa zaka zino, taona kugwa ndi kuonongeko kwa anthu omwe amagwiritsidwa ntchito ndi Mulungu yopambana. Iwo anagwa chifukwa cha mtima wanyada ndi kudzikuzi. Anthuwa anaiwala chenjezo lomveka bwino la Malemba. Anayamba kuganiza kuti iwo ndi opambana ndi apamwamba kwambiri. Ndipo pomaliza anthuwo anagwa ndi kulemera kwa kudzikuzi kwawo komwe. *“Kunyada kutsogolera kuonongeka; Mtima wodzikuzi ndi kutsogolera kupunthwa” (Miyambo 16:18).*

Utumiki wamphamvu uli ndi mayesero akulu akuti wina ayambe kunyada ndi kudzikuzi yekha. Mphamvu **imaledzeretsa** komanso kunyenga. Iwo omwe agwiritsidwa ntchito mwamphamvu ndi Mulungu angapezeka “oledzera” mosavuta chifukwa cha chipambano mu utumiki wao. Ndipo ena athanso kuwatsimikizira mowalimbikitsa zakufunikira kwao kwakukulu. Anthu ena sachedwa kusokonezeka ndi zozizwa zimene atumiki a Mulungu mu mphamvuyi amachita. Mwachisangalalo otsatira aluntha amawatenga atumikiwa ngati milungu. Izi zinachitikapo kwa Paulo ndi Barnaba mu Machitidwe a Atumwi 14:11-13.

Ndalama ndi cholowa zimabwera mosavuta m’mautumiki ena. Ngakhale atumiki akuluakulu, mopusa, angayambe kidzikhulupilira iwo okha osatinso Mulungu. Iwowa amakhoza kukhulupilira kuti mdalitso wa Mulungu ndi ufulu wao, osati mphatso ya chisomo ya kwa Mulungu. Oganiza moterewa ndiye kuti ali pafupifupi kugwa kwakukulu.

Mkusiyanita, atumiki ena amalephera chifukwa cha kuchepa kwa chipambano chao. Mosasamala, iwo safuna kuchitachita za Mulungu ndipo amakhumudwa ngati utumiki wao sukupambana kapena kubala chipatso.

Enanso mosalabadira amafuna angodziwika ndi anthu kuti ndi atumiki akuluakulu komanso a mphamvu. Mbali zonse ziwiri izi, atumikiwa amayamba kuzengereza pakuchita choonadi munthawi yao yakulephera. Iwowa **angabere (kuyeseza)** zozizwa kapena kuchita zinthu zosiyana ndi Malemba, munjira za iwo okha. Anthu otere amavomereza kungotsanzira zochitika m'malo mwa kukhulupilira Mulungu modzichepetsa mukufuna zenizenizo. Ngozi iyitu!

Tiyenera tisaiwale kuti Mulungu ndiye amabweretsa mphamvu zenizeni. Ulemerero onse ndi wake. Ophunzira makumi asanu ndi awiri kuwonjezeraponso mphambu ziwiri anabwerera ndi chisangalalo chachikuru pochokera ku utumiki wao. Iwo anati kwa Yesu, *“Ambuye, zingakhale ziwanda zinatigonjera ife m'dzina lanu”* Luka 10:17). Koma Yesu anawachenjeza: *“Koma musakondwere nako kuti mizimu inakugonjerani, koma kondwerani kuti maina anu alembedwa m'mwamba”* (Luka 10:20). Anawapatsa mfundo yamphamvu yokhudza utumiki wamphamvu. Musadzikuze ndi kudzitukumula chifukwa cha zomwe Mulungu wakuchitirani. Kudzichepetsa ndi chinthu chofunika kwambiri mu utumiki wamphamvu.

## **Kukonzekera Kuchita Utumiki Wamphamvu**

Tsopano tiyeni tiganizire za kukonzekera kwanu utumiki wamphamvu. Muyenera muziyese munjira zosachepera zisanu. Muyenera

- kuunika zolinga zanu
- kulimbitsa ubale wanu ndi Mulungu
- kuonjezera kumvetsetsa kwanu
- kudzipereke ku chifuniro cha Mulungu
- kudziwa mokwanira bwino

### **Unikani Zolinga Zanu**

Choyambilira kuyesa ndi zolinga zanu polakalaka kuchita nawo utumikiwu. Chifukwa chomwe mukumutumikilira Mulungu ndi chofunika zedi komanso chifukwa chochitira zimenezo ndichofunikanso kwambiri.

Muyenera mukhutire ndi zolinga zanu polakalaka kugwiritsidwa ntchito ndi Mulungu. Mu Machitidwe a Atumwi 8, Simoni wamatsenga mwa chidwi anafuna utumiki wamphamvu. Komabe zolinga zake zinali zolakwika. Iye anangofuna kuonedwa ndi anthu ngati munthu wamphamvu. Anali wokonzeka ngakhale kugula mphatso ya utumikiwo ndi ndalama. Mtumwi Petro anazindikira kuti zolinga za Simoni sizinali zenizeni za umulungu. Ndipo Petro anamdzudzula, *“Ulibe gawo kapena chalandira ndi mau awa; pakuti mtima wako suli wolunjika pamaso pa Mulungu”* (Machitidwe a Atumwi 8:21).

Ambiri lero amafunanso utumiki wamphamvu ndi zolinga zolakwika ndi zongodzikonda okha. Kodi zina mwa zolingazi ndi ziti? Zina mwa izo ndi izi:

- Kunyada
- Chilakolako cha kuzilemeretsa wekha ndi kupambana
- Kungofuna kulamulira anthu.

Zina mwa zolinga zabwino mu utumiki wamphamvu ndi izi:

- Chilakolako cholemeretsa Mulungu.
- Kukonda anthu ndi kufunafuna kuwathandiza.
- Chilakolako chotukula ufumu wa Mulungu padziko lapansi.

### **Limbitsani Ubale Wanu ndi Mulungu**

Utumiki wa umulungu umafunika ubale wamphamvu komanso waukulu ndi Mulungu. Tiyenera kuzindikira kuti tingatumikire mu choonadi ndi ubale wamphamvu woterewu basi. Utumiki wathu *kwa* Mulungu sudzakhala ndi mphamvu kuposa ubale wathu *ndi* Mulungu.

Koyambilira kwa Chaputala ichi, tinaona Yesu akutumikira mu kudzodza kupyolera mu ubale Wake ndi Atate ake. Iye anati, *“Pakuti Atate akonda mwana, namuonetse zonse azichita yakha”* (Yohane 5:20).

Chimodzimidzinsu, atumwi anatumikira kudzera mu kulimba kwa ubale ndi Yesu Khristu komanso Mulungu Atate. Ayuda *“anawazindikira kuti anakhala pamodzi ndi Yesu”* (Machitidwe a Atumwi 4:13b).

Onse omwe akufuna kugwiritsidwa ntchito mu utumiki wamphamvu ndi Mulungu ayenera kutsatira zitsanzo za m'malemba izi. Ayenera kupereka

nthawi yao yambiri polimbikitsa ubale wao ndi Mulungu. Atumiki amphamvu amapanga izi kudzera m’mapemphero apadera, kuwerenga ndi kulingalira Malemba, komanso kudzipereka kwathunthu ku chifuniro cha Ambuye.

### **Onjezerani Kumvetsetsa Kwanu**

Njira yachitatu yokonzekera utumiki wa umulungu ndi podzera mu kuwerenga ndi kuphunzira phunziro ili. Kuwerenga ndi kutsatira mfundo za m’buku lino ndi zinthu zabwino zoyambilira powonjezera kumvetsetsa kwanu. Komabe ichi ndi chiyambi chabe. Mutha kuwonjezera magawo ena awiri. Awa ndiwo kuwerenga mabuku a m’Baibulo a Uthenga Wabwino ndi buku la Machitidwe a Atumwi, komanso kuwerenga mabuku olembedwa ndi alembi odzodzedwa.

*1. Werengani mabuku a Uthenga Wabwino ndi buku la Machitidwe a Atumwi.* Kuwerenga mwachindunji, mwadongosolo ndi kubwerezanso kuwerenga Buku Lopatulika kungasithe moyo wanu mwachidziwikire. Mlembi wa bukuli akupatsani umboni pa zakusinthaku kuchokera mu chidziwitso chake. Panali mbusa wamkulu amene anakhala akugwiritsidwa ntchito ndi Mulungu pochiritsa odwala ndi kuturutsa ziwanda. Mbusa wachichepere anafunsa funso mbusayu tsiku lina: Ndithandizeni, kodi mabuku abwino ndi oyenerera pa mutu wa kuchiza mwa umulungu ndi ati? “Eya” anatero mbusa wankuluyo mwamsanga. Ndikuuza mabuku anayi opambana. Mlaliki wachichepereyo anaturutsa polembapo. “Mabuku anayiwa ndi ati?” anafunsa.. “Ndiyenera ndikhale nao.” Mlaliki uja anayankha, “Mateyu, Marko, Luka, ndi Yohane.”

Werengani ndi kuwerengabe mobwerezabwereza mabuku amenewa a Uthenga Wabwino ndi buku la Machitidwe a Atumwi. Pamene mulikuwenga, zifunseni nokha mafunso awa:

- Kodi Yesu ndi atumwi anatomukira bwanji mu mphamvu?
- Kodi anachiza bwanji anthu ndi kuturutsa ziwanda?
- Kodi chinsinsi chakupambana kwao chanali chiyani?
- Kodi ndingatsanzire bwanji moyo wao ndi utumiki wao?

*2. Werengani mabuku ena.* MUYENERA kuwerenga mabuku ena pa mutu uwu olembedwa ndi amuna ndi akazi otamandika a Mulungu. Komanso

muyenera kusamala ndi zomwe musankha kuwerenga. Simabuku onse okhazikitsidwa mu utumiki wamphamvu omwe amatsamira pa mfundo zomveka bwino za Baibulo. Komanso alembi ena siangwiro ndi otamandika.

### **Dziperekeni ku Chifuniro cha Mulungu**

Mungakonzekerenso utumiki wamphamvu podzipereka kwathunthu ku chifuniro cha Mulungu. Yesu anadzipereka ku chifuniro cha Atate ake mpaka imfa ya pa mtanda. Umu ndi momwe analandilirira madalaitso a Atate ake. Inunso muyenera kudzipereka kotheratu ku chifuniro cha Mulungu. Iyi ndi njira yokhayo yomwe mungalandilire madalitso a Mulungu. Mulungu amadzoza zolinga zake zokha. Iye analonjeza kuchitira umboni mau Ake, osati mau anu powatsatira ndi zizindikiro (Marko 16:15-20).

### **Onjezerani Kudziwa Kwanu mwa Kutengapo Gawo**

Omwe akuganizira zokhala nao mu utumikiwu ayenera adziwe mokwanira bwino mwakutengapo gawo mu utumikiwu. Kudziwa mwakutengapo gawo kuyenera kukhala mu uzimu ndi m'machitidwe.

1. *Kutengapo gawo mu uzimu.* Kutengapo gawo mu uzimu mwakuchita iwe mwini zimayamba ndi kubadwa mwatsopano (Yohane 3:3-7). Baibulo limatiuza za amuna ena omwe anayesera utumiki wamphamvu asanabadwensu mwatsopano. Kutengapo gawo kwao kuli chenjezo kwa onse amene amakhudzidwa ndi utumikiwu.

*Koma a Yuda enanso oyendayenda, otulutsa ziwanda, anadziyesa kuchula pa iwo amene anali ndi mizimu yoipa dzina la Ambuye Yesu, kuti, Ndikulumbirirani pa Yesu amene amlalika Paulo. Ndipo panali ana amuna asanu ndi awiri a Skeva, Myuda, mkulu wansembe amene anachita ichi. Ndipo unayankha mzimu woipa, nuti kwa iwo, Yesu ndimzindikira, ndi Paulo ndimdziwa, koma inu ndinu yani? Ndipo munthu, mwa iye amene munali mzimu woipa, anawalumphira nawaposa, nawalaka onse awiriwo, kotero kuri anathawa m'nyumba amariseche ndi olasidwa" (Machitidwe 19:13-16).*

Utumiki mu mphavu za uzimu ufunikanso kudzazidwa ndi Mzimu. Izi ndi zoonanso kwa ife masiku ano. Zinalinso zoona kwa ophunzira aja. Kubatizidwa mu Mzimu Woyera chinali chiyambi cha mphamvu za uzimu ku

mpingo. Ndipo kufikira lero lino zakhalabe tsinde la mphamvu za uzimu. Tidzakambirana izi mwatsatanetsatane mu Chaputala cha 6.

2. *Kutengapo gawo m'machitidwe.* Luntha la machitachita ndi lofunika kwa onse omwe amafuna akhale opambana mu utumiki wamphamvu. Mungaphunzire pogwira limodzi ntchito ndi mtumiki wodziwa zambiri komanso wa chidziwitso chokwanira chakuchita inu mwini, monga momwe ophunzira khumi ndi awiri aja anaphunzilira kwa Yesu Khristu ndi utsogoleri Wake. Muyenera kuyembekezera kukumana ndi zonse: chipambano komanso kulephera pomwe mwayamba kutumikira. Ndipo tsono mungasanthule chomwe mwadutsamocho mwakuyeza kapena kuti kuunika. Umu ndi momwe tonse timaphunzilira kutumikira Ambuye mopambana.

## **Chimangiliro**

Onse amene amafuna kutumikira mu utumiki wamphamvu ayenera ayike chidwi chao pa kukonzekera utumikiwu. Iwo ayenera asayiware kuti utumiki sumasefukira mwamphamvu zawo ndi chuma chao. M'malo mwake utumiki weniweni umasefukira mu mphamvu ndi chuma cha Mulungu.

## Chaputala 6

# Ubatizo wa Mzimu Woyera ndi Utumiki Wamphavu

## Chiyambi

Tiyenera kubatizidwa ndi Mzimu Woyera tisanalowe mu utumiki wamphamvu. Izi zinali chikhalidwe cha okhulupilira kuchokera m’masiku a Chipangano Chatsopano. Ubatizo ndi gwero lathu la mphamvu za uzimu ndi utumiki. Mu Chaputala chino tiphunzira za kutengapo gawo pa chinthu ichi chofunikira cha Chikristu. Tikambiranso mwachindule za zizindikiro zina za ubatizo mukugwirizana kwake ndi utumiki wamphamvu.

## Tanthauzo la Ubatizo wa Mzimu Woyera

Tinganene zambiri pomasulira ubatizo wa Mzimu Woyera. Komabe, tikambirana mfundo zenizeni zisanu zokha zapaphata. Ubatizo mwa Mzimu ndi:

- cholinga chenicheni cha utumiki wa Yesu Khristu pa dziko lapansi
- kumizidwa m’madzi, komanso kudzadzidwa, ndi Mzimu Woyera
- kosiyana zedi ndi kubadwanso mwatsopano
- mphatso ya mphamvu yochoka kwa Mulungu
- lonjezo la okhulupilira onse.
- Tsopano tisanthula ziganizo izi zisanu mwatsatanetsatane.

### **Cholinga Chenicheni cha Utumiki wa Yesu Khristu pa Dziko Lapansi**

A Don Stamps analemba m’buku lao kuti, “Chimodzi mwa zolinga zenizeni za Yesu Khristu mu utumiki Wake chinali kubatiza omutsatira ake ndi Mzimu Woyera” (1990, p. 228). Yesu sanangosangalatsidwa ndi khamu la anthu omwe ankamutsata, ngakhale anthuwo akanachuluka motani. Kuchokera pa chiyambi, Yesu anaganizira zokopa dziko lonse. Iye akanagwiritsa ntchito atumiki ake pokwaniritsa masomphenyawa.

Anthu omwe Mulungu amagwiritsa ntchito amayenera akhale ophunzitsidwa bwino ndi odziwa bwino. Chida chomwe anatipatsa ndi mphamvu za Mzimu Woyera. Yohane m’Batizi anauza chikhamu chimene chinali pafupi naye za momwe anthuwo angadziwire Mesiya wolonjezedwa. Yohane anati Atate anamuza: “*Amene udzaona Mzimu atsikira, nakhala pa Iye, yemweyu ndiye wakubatiza ndi Mzimu Woyera*” (Yohane 1:33b). Kuyambira pachiyambi, Yesu anafunitsitsa kubatiza otsatira ake ndi Mzimu Woyera. Ichi chinali cholinga chenicheni cha utumiki wake.

### **Kumizidwa m’Madzi, Komanso Kudzadzidwa, ndi Mzimu Woyera**

Tingaganizire za ubatizo wa Mzimu Woyera mu njira ziwiri. “**kumizidwa** ndi kudzadzidwa.” Mu Machitidwe a Atumwi 1, Yesu anatchula zochitikazi kuti ubatizo. Mau mu Chaputalachi amatiuza kuti amatanthauza kumizidwa kwathunthu.

*Anawalamulira asachoke ku Yerusalemu, komatu alandire lonjezano la Atate, limene, anati, munalimva kwa Ine; pakuti Yohane anabatizadi ndi madzi; koma inu mudzabatizidwa ndi Mzimu Woyera, asanapite masiku ambiri.* (Machitidwe 1:4b-5)

Patapita masiku khumi, pa Tsiku la Pantekoste (tsiku la kutsika kwa Mzimu Woyera) Mzimu Woyera unatsanulidwa. Baibulo limati, “*Ndipo anadzadzidwa onse ndi Mzimu Woyera, nayamba kulankhula ndi malilime ena, monga Mzimu anawalankhulitsa*” Machitidwe a Aumwi 2:4).

Kapu yopanda kanthu itha kudzadzidwa ndi madzi ndi kumizidwa m’madzi pa nthawi yomweyo. Izi zikulongosolera zomwe zinachitika kwa atumwi makumi khumi ndi awiri pa Tsiku la Pentekoste. Iwo anali omasuka, analinso zipangizo zovundukulidwa, zodzadzidwa ndi Mzimu Woyera ndi

kumizidwa mwa Iye. Chimodzimidzinso lero lino izi zingachitikire ana onse a Mulungu.

### **Losiyana Zedi ndi Kubadwanso Mwatsopano**

Ubatizo wa Mzimu Woyera sumachitika pa nthawi ya *kubadwanso mwatsopano*. Akhristu ena odziwika bwino amalimbikira kuti ubatizo wa Mzimu Woyera ndi kubadwanso mwatsopano ndi chinthu chimodzi. Koma ubatizo uli pawokha ndipo uli wosiyana ndi kubadwanso mwatsopano. Zintsanzo za m’Baibulo zikuchitira umboni motere: Ophunzira khumi ndi awiri aja anayamba kusandulika poyamba (Yohane 20:22); keneko, anabatizidwa ndi Mzimu Woyera (Machitidwe a Atumwi 2:4). A Samariya anayamba kubadwanso mwatsopano (Machitidwe a Atumwi 2:12,14); kenako, “analandira Mzimu Woyera” (Machitidwe a Atumwi 2:17). Ndichimodzimidzinso ndi ife lero lino. Ubatizo wa Mzimu Woyera ndi zosiyana ndi kubadwanso mwatsopano.

Kodi inu munabadwa mwatsopano kapena kuti kutembenuka mtima? Kodi inu ndi mwana wa Mulungu moonadi? Ngati ndi choncho, muyenera kufunafuna kudzadzidwa ndi Mzimu Woyera monga ngati okhulupilira a mu Mpingo Woyamba uja.

### **Mphatso ya Mphamvu Yochoka kwa Mulungu**

Mu Luka 24:49 Yesu anafotokozera za ubatizo wa Mzimu Woyera. Iye anati ndi “*kukutidwa*” kapena kuti “*kuvekedwa*” ndi mphamvu yochokera kumwamba. Anati, “*Ndipo onani, Ine nditumiza pa inu lonjezano la Atate wanga; koma khalani inu m’ mudzi muno, kufikira mwavekedwa ndi mphamvu yochokera Kumwamba*” (Luka 24:49).

Momveka bwino, Yesu analonjeza mphamvu yotereyi kwa okhulupilira ake Mzimu Woyera ukadzangowadzadza. “*Komatu mudzalandira mphamvu, Mzimu Woyera atadza pa inu*” (Machitidwe a Atumwi 1:8). Mau ofunikira a chiGriki (*eperchomai*) omwe agwiritsidwa ntchito mu vesi ili akutanthauza “kufikira pa.” Ndi mau okhaokha omwe anagwiritsidwa ntchito mu Luka 1:35 pofotokoza za Mzimu Woyera uli “kufikira pa” Mariya. “*Mzimu Woyera adzafika pa iwe, ndi mphamvu ya Wankulukulu idzakuphimba iwe.*”

Mavesi awa akuonetsa chithunzithunzi cha anthu atakutidwa kwathunthu ndi, kugwiridwa ndi, mphamvu ya Mulungu. Izi ndi zomwe zimachitika pamene okhulupilira abatizidwa mu Mzimu Woyera.

### **Lonjezo la Okhulupilira Onse**

Okhulupilira onse amene ndi obadwanso mwatsopano ayenera kubatizidwa mu Mzimu Woyera. Baibulo limati okhulupilira makumi khumi ndi awiri omwe anasonkhana pa Tsiku la Pentekoste, “anadzazidwa onse ndi Mzimu Woyera (Machitidwe a Atumwi 2:4). Baibulo silimati kuti 119 ndiwo anadzazidwa ndi Mzimu Woyera ndipo m’modzi sanabatizidwe, ayi. *Onse anabatizidwa.*

Chifuniro cha Mulungu ndi kuti okhulupilira onse adzazidwe ndi Mzimu Woyera. Petro anatsimikiza izi momveka bwino pa tsiku la Pentekoste. M’mau ake a ulaliki Petro ananenapo za mphatso yodabwitsayi. “*Pakuti lonjezano liri kwa inu, ndi kwa ana anu, ndi kwa onse akutali, onse amene Ambuye Mulungu wathu adzaitana*” (Machitidwe a Atumwi 2:39).

Lonjezano la ubatizo wa Mzimu Woyera ndi la “*onse amene Ambuye Mulungu wathu adzaitana.*” Lonjezano ili mulinso mphamvu yomwe Mzimu Woyera umabweretsa. Izi zikutanthauza kuti lonjezanoli ndi lanunso. Mwina ndikutheka kuti inu ndi m’modzi wa iwo amene sanalandire lonjezanoli la Atate. Ngati ndi choncho, pemphani Ambuye akudzadzeni ndi Mzimu Woyera wa mtengo wapatali. Gawo III likufotokoza momwe mungalandilire mphatsoyi.

## **Kufunika kwa Ubatizo mu Mzimu Woyera mu Utumiki Wamphamvu**

Zingaoneke ngati zodziwikiratu, komabe tibwerezanso kunena choonadichi. Munthu ayenera apatsidwe mphamvu ndi Mzimu Woyera, asanalowe mu utumiki wamphamvu.

Mphamvu ya utumiki imabwera ndi ubatizo mu Mzimu Woyera. Kudzazidwaku ndi kofunikira poyamba utumiki wamphamvu pa zifukwa ziwiri. Choyamba, ubatizo wa Mzimu Woyera ukulamulidwa m’Malemba ndipo chachiwiri, ndi gwelo lenileni la mphamvu yanu ya uzimu.

## **Ndi Lamulo Lochokera m'Malemba**

Paulo anawapatsa Akhristu a ku Aefeso malamulo awiri: “*Ndipo musaledzere naye vinyo, m'mene muli chitayiko; komatu mudzale naye Mzimu.*” (Aefeso 5:18). Tiyenera titsatire malamulo onse awiriwa.

Yesu anapereka lamulo lake lomaliza kwa ophunzira ake asanakwere kupita kumwamba. Anawauza kuti adzazidwe ndi Mzimu Woyera. (Machitidwe a Atumwi 1:4-5). Ambuye wathu anakhala masiku makumi anayi pansi pano atauka kwa akufa. Panthawiyi, anawauza omutsatira mobwerezabwereza kuti asayambe kuchitira umboni. Anafuna kuti adikire kufikira atabatizidwa ndi Mzimu Woyera (Luka 24:49; Machitidwe a Atumwi 1:4-5,8). Yesu anadziwa kuti utumiki wao adzafuna mphamvu ndi luso loposa machitidwe a umunthu chabe. Anayenera “kuvekedwa ndi mphamvu yochokera Kumwamba” (Luka 24:49).

Dongosolo ili liri loonabe kufikira lero lino. Ifenso, tiyenera kupatsidwa mphamvu ndi Mzimu Woyera tisanayambe utumiki ulionse wa uzimu. Izi ndi zoonadi makamaka mu utumiki wamphamvu. Tingakhale opuse motani ngati sitingamvera izi ndi kuchita mosiyana?

## **Ndi Gwero la Mphamvu ya Uzimu**

Mzimu Woyera ndi gwero lathu lokhalo la mphamvu ya uzimu. Izi zinali chomwechi mu:

- Utumiki wa Yesu Khristu pansi pano.
- Utumiki wa Mpingo Woyambilira uja.

1. *Utumiki wa Khristu.* Mphamvu za Khristu mu utumiki zinabwera kudzera mu kudzozedwa kwake ndi Mzimu Woyera. Kudzozedwaku kunafika mu nthawi ya ubatizo wake ku mtsinje wa Yordano (Luka 3:32). Yesu sanayambe utumiki Wake wa **umesiya** kufikira atadzozedwa ndi Mzimu Woyera. Nthawi ina Petro analalikiranso za kudzozedwaku.

*Za Yesu wa ku Nazarete, kuti Mulungu anamdzoza Iye ndi Mzimu Woyera ndi mphamvu; amene anapitapita nachita zabwino nachiritsa onse osautsidwa ndi mdierekezi, pakuti Mulungu anali pamodzi ndi Iye (Machitidwe a Atumwi 10:38).*

Timakhulupilira kwathunthu kuti Yesu anali, ali, ndipo adzakhalabe Mulungu wamuyaya. Sanayambe wasiyapo kukhala Mulungu. Komanso timakhulupilira kuti anasankha kutumikira mu mphamvu ndi mkudzoza kwa Mzimu Woyera akanali panso pano. Pakutero anakhazitsa njira ya utumiki yakuti ife titsatire.

Yesu sanayambe kutumikira mwa umulungu kugulu kufikira atabatizidwa ndi Mzimu Woyera. *Asanadzozedwe* sanachiritsa odwala, sanatulutse ziwanda ndipo sanapange chozizwa chilichonse ku gulu. *Atadzozedwa* ndi Mzimu Woyera Iye anayamba kutumikira mu mphamvu. Malemba otsatirawa ochokera mu uthenga wa Luka amatsimikizira izi (4:1-2, 14, 18-21; 5:17, 6:19). Yesu anafunika kudzoza kuti akwaniritse utumiki wake. Ifenso, tiyenera kudzozedwa ndi Mzimu Woyera . Kufikira titadzozedwa, ndi pomwe tingathe kukwaniritsa utumiki womwe Mulungu watipatsa.

**2. Utumiki wa Mpingo Woyamba.** Ubatizo wa Mzimu Woyera unalinsogwero la utumiki wa mpingo ya mu Chipangano Chatsopano. Buku la Machitidwe a Atumwi limafotokoza mobwerezabwera kuti ubatizo ndi chuma cha mphamvu cha Mulungu choperekedwa ku mpingo. Ndikudzozedwa ndi Mzimu Woyera kokha komwe kungapangitse mpingo kukwaniritsa cholinga chake chakukafikitsa Uthenga Wabwino ku malekezero a dziko (Machitidwe a Atumwi 1:8).

Buku la Machitidwe a Atumwi limalongosola mu malo okwanira asanu ndi amodzi mmene anthu anabatizidwa, kapena kudzazidwa, ndi Mzimu Woyera: Machitidwe a Atumwi 2:4; 4:31; 8:17; 9:17; 10:44-46; 19:6). Mphamvu ya Mulungu inaonekera m'malo onsewa. Nthawi iliyonse izi zinachitika, zotsatira zake zinali kholora lalikuru la anthu kulowa mu Ufumu wa Mulungu. Machitidwe a Atumwi 4:33 akufotokoza za zomwe zinachitika nthawi ina kutangotsika Mzimu Woyera: *“Ndipo atumwi anachita umboni ndi mphamvu yaikulu za kuuka kwa Ambuye Yesu; ndipo panali chisomo chachikulu pa iwo wonse.”*

Mzimu Woyera unali gwero la mphamvu ya utumiki wa Yesu komanso Mpingo Woyamba. Mphamvu yomweyi ikupezekanso kwa ife lero lino, ndipo ngati atumwi aja, tingadzazidwenso ndi Mzimu Woyera.

## M'mene Tingalandilire Mzimu Woyera<sup>8</sup>

Pa nthawi, mutha kufunsa “Kodi ndingalandire bwanji Mzimu Woyera lero lino? Tsopano tiyankha funso ili lofunika.

### **Nyengo Yolandilira Mzimu Woyera.**

Muyenera kukwaniritsa zinthu (nyengo) zitatu kuti mubatizidwe ndi Mzimu Woyera. Muyenera kubadwanso mwatsopano mwachoonadi, muyenera kukhumba kudzazidwa ndi Mzimu Woyera ndipo muyenera kumvera Mulungu.

1. *Kubadwanso Mwatsopano.* Baibulo limanena mosabisa kuti tiyenera kubadwanso mwatsopano tisanabatizidwe ndi Mzimu Woyera. Yesu anati dziko silingalandire Mzimu Wachoonadi (Mzimu Woyera). “Dziko lapansi silingathe kumlandira Iye, pakuti silimamuona Iye kapena kumzindikira Iye” (Yohane 14:17). Ndani angalandire Mzimu Woyera? Iwo okha amene abadwanso mwachoonadi mwa Mzimu wa Mulungu. Nkhani yobadwanso mwatsopanoyi imafunikira chikhulupiliro chapawekha, chochitachita ndi cholimba mwa Yesu Khristu monga Mpulumutsi. Zimafunikanso kulapa, kutembenuka ndi kusiya chilichonse chomwe chimakhumudwitsa Mulungu. Moonjezera, zimasowekanso kugonja kotheratu pakukaniza chifuniro chathu ndi kutsatira chifuniro cha Mulungu. (Munabadwapo mwatsopano mwa choonadi kodi?) Ngati sichoncho, mungatero ngati mungatembenukire kwa Yesu tsopano lino mwachikhulupiliro komanso mu kulapa machimo anu.

2. *Kukhumba kudzazidwa.* Yesu anati, “*Odala ali akumva njala ndi ludzu la chilungamo; chifukwa adzakhuta*” (Mateyu 5:6). Kudzazidwa ndi chiyani? Kudzazidwa ndi chilungamo cha Mulungu. Izi zimachitika kudzera mu mphamvu yakupatula ya Mzimu Woyera basi (Aroma 15:16; 1 Akorinto 6:11). Kukhala odzazidwa ndi Mzimu Woyera kumafunika tikhumbe (kulakalaka) Mulungu koposa china chilichonse. Yesu amatiyitanabe, “*ngati pali munthu akumva ludzu, adze kwa Ine; namwe*” (Yohane 7:37b). Kodi muli

---

<sup>8</sup> Gawo ili ndi la iwo amene sanabatizidwepo mu Mzimu Woyera. Ndi la iwonso amene akufuna kudzazidwanso ndi Mzimu. Gawolinso ndi lohandiza kwa iwo amene angatsogolere ena ku ubatizowu.

ndi njala ndi ludzu lochuluka lakufuna Mulungu? Ngati ndi choncho ndiye kuti mwafika pa mfundo yachiwiri yoti mutha kudzazidwira ndi Mzimu Woyera.

3. *Kumvera Mulungu.* Mu Machitidwe a Atumwi 5:32, Petro anati Mulungu amapereka Mzimu Woyera “kwa iwo akumvera Iye.” Munthu ayenera kukhala ndi mtima ofuna kumvera Mulungu. Ngati muli ndi mtima wotere, Mulungu adzakupatsani Mzimu wake Woyera pamene mupempha.

### **Njira Zitatu Zomwe Tingalandilire Mzimu Woyera**

Mwina ndikutheka kuti mukufunitsitsadi mutadzizidwa ndi Mzimu Woyera. Ngati ndi choncho, muyenera kuchita zinthu zitatu izi. Poyamba, muyandikireni Mulungu molimba mtima. Kachiwiri, mfunseni Mulungu kuti akudzazeni ndi Mzimu Woyera. Kachitatu, muyamikeni ndi chikhulupiliro pa mphatso yomwe akukupatsani.

1. *Yandikirani “mpando wa chisomo” molimba mtima.* Malemba amaphunzitsa izi: “*Potero tilimbike mtima poyandikira mpando wachifumu wachisomo*” (*Ahebri 4:16a*). Mungabwere pamaso pa Mulungu mopanda mantha komanso odzazidwa ndi kulimbika mtima. Chifukwa chiyani? Mukudziwa kuti mukufika molingana ndi chifuniro chake changwirowo. Fikani molimba mtima pomwe mukufunsa Mulungu kuti akudzazeni ndi Mzimu Woyera. Amakulandirani pamaso pake.

2. *Pemphani Mulungu kuti akudzazeni ndi Mzimu Woyera lero.* Yesu watipatsa lonjezano lopambana ndi lodabwitsa lokhudzana ndi kulandira Mzimu Woyera: “*Pakuti yense wakupempha alandira*” (*Luka 11:10*). Imvani mphamvu ya lonjezano lake: *yense wakupempha alandira.*

*Potero, ngati inu, okhala oipa, mudziwa kupatsa ana anu mphatso zabwino, koposa kotani nanga Atate wanu wa kumwamba adzapatsa Mzimu Woyera kwa iwo akupempha Iye?* (*Luka 11:13*)

Kodi mukufuna kuti Mulungu akudzazeni ndi Mzimu Wake. Tangomufunsani tsopano; Iye ali wokonzeka kukudzazani lero.

3. *Muyamikeni ndi chikhulupiliro chachiyembekezo.* Tsopano, yambani kutamanda Mulungu ndi mtima wanu wonse. Pakutero, yembekezerani Iye kukudzazani ndi Mzimu Woyera. Izi zimatchedwa kuti “*chikhulupiliro chachiyembekezo*” chifukwa mumayembekeza chinthu china chake kuchoka

kwa Mulungu mu chikhulupiliro. Yesu analonjeza, “*zinthu ziri zonse mukazipemphera ndi kuzipempha khulupirirani kuti mwazilandira, ndipo mudzakhala nazo*” (Marko.11:24).

Ophunzira makumi khumi ndi awiri (120) aja amatamanda Mulungu pa tsiku la Pentekoste. Baibulo limati “*iwo anakhala chikhalire m'kachisi nalikuyamika Mulungu*” (Luka 24:53). Chitani chimodzimodzi monga ophunzira oyambawa. Yembekezerani Mulungu kukudzazani ndi Mzimu Woyera. Ndiponso yembekezerani kulankhula ndi malilime ena motsogozedwa ndi Mzimuyo.

### **Zizindikiro za Kulandira Mzimu Woyera**

Simudzakhalanso chimodzimodzi mutangolandira Mzimu Woyera. Mungayembekezere zizindikiro zina kutsatira kudzazidwa kwanu.

1. *Chizindikro choyamba chenicheni.* Chizindikiro choyamba chakuti walandira Mzimu Woyera ndi kulankhula ndi malilime ena (zilankhulo zachilendo). Izi zimachitika monga momwe Mzimu amakuthandizirani (Machitidwe a Atumwi 2:4). Kulankhula ndi malilime ena pamene uli kudzazidwa ndi Mzimu Woyera chinali chinthu chodziwikiratu pakati pa okhulupilira a mu buku la Machitidwe a Atumwi. Timawerenga zambiri za izi mu Machitidwe a Atumwi 2:1-4; 10:45-47; ndi 19:1-6. Mudzazindikira kuti mwadzazidwa ndi Mzimu Woyera pamene mudzayamba kulankhula ndi malilime ena.

2. *Mavesi ena okhudzana ndi zizindikiro za utumiki wa mphamvu.* Zizindikiro zina zimatsatira pamene muphunzira kuyenda mu Mzimu. Zizindikiro zokwana zisanu ndi zitatu zukhudzana molunjika ndi utumiki wa mphamvu zina za izo ndi izi:

- Mphamvu yogwirira ntchito ya Yesu (Yohane 14:16-18; 16:14)
- Kowonjezereka kwa kutha kuzindikira kupezeka kwa Mulungu (Yohane 14:16-18)
- Kowonjezereka kwa kutha kuzindikira msanga tchimo ndi kudziwa kuti tchimo limakhumudwitsa Mzimu Woyera (Yohane 16:7-11)
- Mphamvu yakukhala mboni (Machitidwe 1:8)
- Kulimba mtima (Machitidwe a Atumwi 2:14-41; 4:31)
- Chikondi chachikulu pa Mulungu ndi kwa anthu (Aroma 5:5).

- Chikhumbo chokwanira bwino komanso kukwaniritsa kupemphera, makamaka kupempherera ena (Aroma 8:26,27)
- Kuonetsera kwa mphatso zosiyanasiyana za Mzimu Woyera (1 Akorinto 12:1-11).

## **Chimangiliro**

Mphamvu ya Mzimu Mulungu ndi yofunika zedi mu utumiki wamphamvu. Mumalandira mphamvuyi pokhapokha ngati Mzimu Woyera atsikira pa inu (Machitidwe a Atumwi 1:8). Choncho, okhulupilira aliyense amene afuna kugwiritsidwa ntchito ndi Mulungu mu utumiki wamphamvu ayenera kubatizidwa ndi Mzimu Woyera.

## Chaputala 7

# Mphatso za Mzimu Woyera ndi Utumiki Wamphamvu

## Chiyambi

Kumvetsa kwenikweni kwa mphatso za uzimu ndi kofunika zedi mu utumiki wamphamvu. Izi makamaka ndizoona pa mphatso zisanu ndi zinayi zija zomwe zalembedwa mu 1 Akorinto 12:8-10. Tingokudziwitsani pang’ono poyamba za mphatsozi, ndipo kenako tisanthula ntchito zake mu utumiki wamphamvu.

## Kutanthauzira Mphatso za Mzimu

Mphatso za uzimu izi zatanthauziridwa munjira zosiyanasiyana ndi utumiki osiyanasiyana. Mu buku lino, tigwiritsa ntchito tanthauzo ili:

Mphatso za uzimu ndi kudzoza kwa umulungu koperekedwa kwa okhulupirira odzazidwa ndi Mzimu Woyera kuti akwaniritse chifuniro cha Aate.

Tsopano tiunika gawo kapena nusu iliyonse ya chiganizochi.

Poyamba, “mphatso za uzimu” ndi mphatso zenizeni. Choncho, zimaperkedwa mwa chisomo chaulere cha Mulungu, osati potengera ubwino ndi ntchito zathu. Sizimaperekedwanso monga ngati mphoto *pa china chilichonse chomwe tachita*. Koma, mphatsozi zimaperkedwa ndi Mzimu monga pali kufunikira kwa kukwaniritsa zosowa zapaderadera.

Kachiwiri, mphatso za uzimu ndi “kudzoza kwa umulungu.” Izi zikutanthauza kuti mphatso za uzimu zimachokera kwa Mzimu, osati kuchokera mu kuthekera kwa munthu. Munjira ina, zimagwira ntchito pansi pa chitsogozo cha Mzimu Woyera.

Kachitatu, mphatso za uzimu izi ndi “zoperekedwa kwa okhulupirira odzazidwa.” Mphatsozi zimagwirira ntchito pomwe Mzimu ayenda (kutumikira kudzera) mwa okhulupilira wodzipereka. Zimagwira ntchito pomwe okhulupilirawa ayenda ndi kukhala mu uzimu. (Agalatia 5:25).

Kachinayi, mphatso za uzimu zimaperekedwa “ndi Mzimu Woyera.” Mzimu Woyera ndiye mwini ndi amene amapereka mphatsozi (I Akorinto 12:4-6). Ndiko kuti, mphatso zimagwira ntchito yake mwa chifuniro cha Mzimu (I Akorinto 12:11). Sizigwira ntchito monga mwa chifuniro cha munthu.

Kachisanu, tanthauzo lathu likuti mphatsozi zimaperekedwa kwa okhulupilira “kuti akwaniritse chifuniro cha Atate.” Zimaperekedwa kuti zipititse mtsogolo umfumu wake. Mphatso zimenezi sizimaperekedwa pofuna kukwaniritsa zolinga kapena zokhumba za munthu aliyense payekha. Simoni wamatsenga anaphunzira phunziroli mu buku la Machitidwe a Atumwi 8:20-23. Petro anamudzuzula chifukwa chofuna kugula mphamvu ya Mulungu ndi ndalama. Munthu uyu amafuna kugwiritsa ntchito mphamvu ya Mulungu pa phindu la iye mwini.

## **Kuzindikira Mphatso za Uzimu**

Tsopano tisanthula kuonekera (kutumikira) kusanu ndi kunayi kwa Mzimu mu 1 Akorinto 12:7-10.<sup>9</sup> Mphatso zisanu ndi zinayi izi zimagwira ntchito yotamandika mu usodzi wamphamvu.

*Koma kwa yense kwapatsidwa maonekedwe a Mzimu kuti apindule nawo. Pakuti kwa m’modzi kwapatsidwa mwa Mzimu mau a nzeru; koma kwa mnzache mau a chidziwitso, monga mwa mzimu yemweyo: kwa wina chikhulupiriro, mwa Mzimu yemweyo; ndi kwa wina*

---

<sup>9</sup> Malo ena atatu omwe muli mphatso za uzimu mu makalata a Paulo ndi Aroma 12:6-8; 1 Akorinto 12:28-30; ndi Aefeso 4:11.

*mphatso za machiritso, mwa mzimu m' modziyo; ndi kwa wina machitidwe a mphamvu; ndi kwa wina chinenero; ndi kwa wina chizindikiro cha mizimu; kwa wina malilime amitundumitundu; ndi kwa wina mamasulidwe a malilime. (1 Akorinto.12:7-10)*

Mphatso zisanu ndi zinayi za mu 1 Korinto 12:8-10 zimagawika m' magulu atatu mwa izo zokha a mphatso zitatu m' gulu lirilonse. Gulu loyamba muli mphatso za *mavumbulutso*. Mphatso izi zimatilola kudziwa malingaliro a Mulungu. Gulu lachiwiri muli mphatso za *uneneri* kapena kulankhula mau. Mphatso za uneneri zimatilola ife kulankhula mau a Mulungu. Gulu lachitatu muli mphatso za *mphumvu*. Izi zimatiipatsa nyonga zogwirira ntchito ya Mulungu. Tsopano tipeza ndi kutanthauzira mphatso za uzimu zitatu mu gulu lirilonse.

### **Mphatso za Mavumbulutso**

Mphatso zitatu ndi izi:

- mau a chidziwitso: vumbulutso la umulungu lokhala ndi chidziwitso cha Mulungu.
- mau a nzeru: vumbulutso la umulungu lokhala ndi nzeru ya Mulungu.
- chizindikiro cha mizimu: vumbulutso la umulungu la zimene mzimu akuonetsera kapena kutakasira kuchitapo kanthu.

### **Mphatso za Uneneri**

Mphatso zitatu za uneneri ndi izi:

- mphatso ya chinenero: kulankhula uthenga wa umulungu wochoka kwa Mulungu mu chilankhulo chodziwika ndi wolankhulayo.
- mphatso ya malilime: kulankhula mwa umulungu uthenga kapena pemphero mu chilankhulo chosadziwika ndi wolankhulayo.
- mphatso ya mamasulidwe a malilime: kulankhula mwa umulungu tanthauzo (chimasuliro) la uthenga wa m' malilime.

## **Mphatso za Mphamvu**

Mphatso za Mphamvu ndi:

- mphatso ya machiritso: kuchiritsa anthu odwala ndi mphamvu ya umulungu.
- mphatso ya chikhulupiriro: *kutumphuka* (kukurutsa) kwa chikhulupiriro cha umulungu pa kuchita ntchito yopatsidwa ndi Mulungu.
- mphatso yamachitidwe a mphamvu: kugwiritsa ntchito mphamvu ya umulungu pakugwira ntchito ya Mulungu

## **Mphatso za Uzimu mu Utumiki Wamphamvu**

Kodi mphatso zisanu ndi zinayi izi za uzimu zimagwirizana bwanji ndi utumiki wamphamvu? Tiphunzira mphatso iliyonse mogwirizana ndi funsoli.

### **Mphatso za Mavumbutso mu Utumiki Wamphamvu**

Mphatso za mavumbutso ndi zofunika mu utumiki wamphamvu. Mu Machitidwe a Atumwi, mau a chidziwitso kapena chizindikiro cha mizimu nthawi zambiri kumatsogolera kukugwira ntchito kwa mphatso za mphamvu. (zitsanzo onani Machitidwe a Atumwi 14:8-10; 16:16-18). Ndi chifukwa chiyani izi zili chonchi? Tiyenera kudziwa malingaliro a Mulungu tisanachite ntchito za Mulunguyo. Izi zikutanthauza kuti tiyenera kudziwadi chifuniro cha Mulungu mu ntchito yopatsidwayo. Yesu mwini sankangoyenda mopanda dongosolo ndi kumachiritsa anthu paliponsepo. Mu nthawi iliyonseyo anayamba wamva kuchokera kwa Atate ake a kumwamba. Ambuye wathu anuti.

*Indetu, Indetu, ndinena kwa inu, sakhoza Mwana kuchita kanthu pa yekha, koma chimene aona Atate achichita, ndicho. Pakuti zimene Iye azichita, zomwezo Mwananso azichita momwemo. (Yoh.5:19)*

Mphatso ya chizindikiritso cha mizimu imayenera kuyamba kugwira ntchito yake tisanadziwe mmene tingamuyandikire wodwalayo. Ndikofunika nthawi zonse kudziwa kaye kuti munthuyo akudwala chifukwa chiyani. Kodi kudwalako ndi kwachilengedwe kapena kochokera ku mphamvu ya ziwanda? A Smith Wigglesworth, munthu wa chikhulupiriro chozama zedi, nthawi yina anapempherera anthu osamva awiri. Kwa munthu woyamba anati “landira machiritso!” ndipo munthuyo anachiritsidwa nthawi yomweyo. Tsono anatembenukila kwa winayo ndi kulamulira, “Turuka mwa munthu uyu, iwe chiwanda cha ugonthi.” Makutu a munthuyo anatsekukanso. Kenako, a Wigglesworth anafunsidwa chifukwa chiyani anapempherera anthuwo mosiyana. Iwo anayankha, “simuchiritsa ziwanda koma kuziturutsa.”

Bambo Wigglesworth anagwiritsa ntchito mphatso ya chidziwitso cha mizimu. Popanda mphatsoyi, sakanadziwa kuti atumikila bwanji kwa anthu osamvawo. Popanda mphatsoyi “tingamayesera kuchiza ziwanda” ndi “kuturutsa matenda” – pomwe tinayenera kuchita mosiyanita mwake. Tifunika chionetsero chopambana cha mphatso za mavumbulutso kuti pakhale chigonjetso mu utumiki wathu wakugwiritsa ntchito mphatso za mphamvu.

### **Mphatso za Uneneri mu Utumiki Wamphamvu**

Mphatso ya uneneri imafunika nthawi zambiri patangotha kuchitika chionetsero cha mphamvu ya Mulungu. Zinali chomwechi pa Tsiku la Pentekoste pamene Petro analalikira “uthenga” wake wotchuka uja. Zoonza zake ndi zakuti kulankhula kwa Petro pa tsikuli suunali ulaliki konse. Chabe kungoti unali uthenga wa ulosi wolankhulidwa motsogozedwa ndi kudzoza kwa Mzimu Woyera. (Horton 1976) Ayuda omwe analipo anaona chozizwa cha Pentekoste. (chionetsero: kulimbana kwa mphamvu). Anamvanso uthenga wa ulosi wa Petro (kulengeza: kulimbana kwa choonadi). Zotsatira zake, anthu anatsutsika ku machimo awo. (Machitidwe a Atumwi 2:37). Ndipo anthu mazana atatu anapulumutsidwa ndi kubatizidwa tsiku lomwelo. (Machitidwe a Atumwi 2:41).

Paulo anaphunzitsa kuti malilime ndi chizindikiro kwa osakhulupilira. Chizindikiro ichi chimawasonyeza osakhulupirira kuti Mulungu akugwira ntchito yake mu mpingo (1Akorinto 14:22). Ndipo kupyolera mu ulosi, wochimwa amazindikira kuti ali pa maso pa Mulungu. Zotsatira zake, amatsimikiziridwa kuti ali wochimwa ndipo “*zobisika za mtima wake*

*zionetsedwa; chotero adzagwa nkhope yake pansu, nadzagwadira Mulungu” (1 Akorinto 14:25a).*

Mauthenga ena a uneneri amalosera za mtsogolo. Izinso zingakhale umboni wamphamvu wakupuzeka kwa Mulungu mumpingo. Tikuona chitsanzo cha izi mu utumiki wa m’neri Agabo (Acts 11:28; 21:10-11).

### **Mphatso za Mphamvu mu Utumiki Wamphamvu**

Mphatso za mphamvu ndi mphatso zowonekeratu pa mphatso zonse za uzimu. Anthu amachiritsidwa kudera mu mphatso zochiritsa komanso zachikhulupiriro. Anthu amachiritsidwa kupyolera mu kugwiritsa ntchito mphatso ya machiritso ndi mphatso ya chikhulupiriro. Amaona bwinobwino mphamvu ndi kupuzeka kwa Mulungu. Ochimwa amafika pokumana maso ndi maso ndi choonadi cha Mulungu wa moyo. Miyoyo yawo imakhala yokozerika kulandira uthenga wabwino. Timaona izi zikuchitika mu machiritso a Eneya:

*Koma kunali, pakupita Petroponse, anatsikiranso kwa oyera mtima akukhala ku Luda. Ndipo anapeza kumeneko munthu dzina lake Eneya, amene anagonera pa mphasa zaka zisanu ndi zitatu; amene anagwidwa manjenje. Ndipo Petro anati kwa iye, Eneya, Yesu Khristu akuchiritsa iwe; uka, yalula mphasa yako. Ndipo anauka pomwepo. Ndipo anamuona iye onse akukhala ku Luda ndi ku Sarona, natembenukira kwa Ambuye amenewa. (Machitidwe a Atumwi. 9:32-35)*

Chitsitsimutso chachikulu chinabuka kupyolera mukugwiritsa ntchito mphatso ya machiritso. Chitsitsimutso ichi chinakhudza chigawo chonse.

Mphatso ya chitatu mugululu ndi mphatso yamachitidwe a mphamvu (kuchititsa zozizwitsa). Kugwiritsa ntchito mphamvu ya umulungu kotere kumapanga machiritso ndi zozizwitsa zina (Marko 5:30; Luka 5:17; 6:19; onaninsu Luka 11:20). A Stamps (1990, t.350) akunena zotsatirazi pokhudzana ndi mphatso iyi:

Izi ndi zochitika za mphamvu ya umulungu zimene zimasintha zinthu za chilengedwe. Zimaphatikizirapo machitidwe a umulungu mmene Ufumu wa Mulungu umaonekera motsutsana ndi Satana ndi mizimu yoyipa .... kuphatikiziraponso kuturutsa ziwanda.

## Chimangiliro

Mphatso za Mzimu ndi zoyenera mu utumiki wamphamvu uliwonse. Timalandira mphamvu pamene tibatizidwa mu Mzimu Woyera. Mphamvuyi imagwira ntchito yake kupyolera mu mphatso za Mzimu mu kudalitsa ndi kumanga mpingo. Zimagwira ntchito kupyolera mwa okhulupirira amene amakhumba kugwiritsidwa ntchito ya Mulungu mu utumiki wa mphamvu. Okhulupilira otere ayenera kudziwa m'mene angamvanirane ndi Mzimu mukuyenda kwao kwa tsiku ndi tsiku ndi Mulungu. Ndi pokhapo pamene akhoza kugwiritsidwa ntchito mu mphatso za uzimu pamene kufunikira kukhalapo monga Mzimu afunira.

Mu 1 Akorinto 12:8-10 aperekamo m'ndandanda wa mphatso zisanu ndi zinayi za uzimu. Mphatso iliyonse ya mphatsozi ndiyofunika pa kutukura utumiki wa mphamvu. Mphatso zisanu ndi zinayi izi zikhoza kugawidwa m'magulu atatu okhala ndi mphatso zitatu mu gulu lirilonse. Maguluwa ndi awa:

1. Mphatso za mavumbulutso
  - mau a chidziwitso
  - mau a nzeru
  - chizindikiro cha mizimu.
  
2. Mphatso za uneneri
  - mphatso ya chinenero
  - mphatso ya malilime
  - mphatso ya kumasulira malilime
  
3. Mphatso za mphamvu  
mphatso ya machiritso
  - mphatso ya chikhulupiliro
  - mphatso ya amchitidwe a mphamvu.



## Chaputala 8

# Kusunga Mphatso za Uzimu

## Chiyambi

Mbusa wa chi Pentekoste akufuna awone mphatso za Mzimu zikugwira ntchito yake mu mpingo. Akulakalaka mphamvu ya Mulungu itamasulidwa mu nthawi ya mapempero. Mbusa wotereyu akufuna ataona Mulungu akulemekezeka ndi zosowa za anthu zikukwaniritsidwa. Kuti izi zichitike, “ayenera kuphunzira kagwiritsidwe ntchito ka mphatso za uzimu. Izi zimasowa maluso awiri. Poyamba, mbusa ayenera kukhala otha *kulimbikitsa* kagwiritsidwe ntchito ka mphatso za uzimu mu mpingo wake. Kachiniri, ayenera kutha kukwaniritsa *kuyang'anira* kagwiritsidwe ntchito ka mphatsozi, popewa kuzigwiritsa ntchito molakwika. Tsopano tikambirana maluso awa ofunikira pa ubusa:

## **Kukonza Njira Zogwiritsira Ntchito Mphatso za Uzimu**

Mbusa atha kuthandiza kukonza ndi kupititsa patsogolo kagwiritsidwe ntchito ka mphatso za uzimu pa mpingo mu njira zingapo. Zina mwa izo ndi kuvomereza udindo pa mphatsozi, kuphunzitsa, kuchita mwakupereka chitsanzo, ndi kulimbikitsa.

### **Kuvomera Udindo wa Ubusa**

Mbusa ndi mtsogoleri wosankhidwa ndi Mulungu wa pa mpingo. Iya ali ndi udindo woonetsetsa kuti mphatso za uzimu zikugwira ntchito yake mu

Chaputala 8: Kusunga Mphatso za Uzimu

mpingo wake. Kagwiritsidwe ntchito koyenera ka mphatso za uzimu kayenera kukhala chimodzi mwa zolinga zikuluzikulu za utumiki wa m’busayo. Zotsatira zakusagwiritsa ntchito ndi kugwiritsa ntchito mphatso za uzimu moyera zaperekedwa mu chithunzi 8.1.

**Figure 8.1**  
**Kufananiza kwa Kugwiritsa Ntchito ndi Kusagwiritsa Ntchito Koyenera kwa Mphatso za Uzimu**

Kuwerenga 1 Akorinto 12 mpaka 14 mosamalitsa kumaonetsa chionongeko chimene chimabwera mu mpingo chifukwa cha kugwiritsa ntchito mphatso za uzimu molakwika. Ndimezi zikuonetsanso madalitso amene amabwera chifukwa chakuzigwiritsa ntchito moyenera.

<p><b>Chionongeko chimene chimabwera ngati mbusa agwiritsa ntchito mphatso za uzimu molakwika:</b></p>	<p><b>Madalitso amene amabwera ngati mbusa agwiritsa ntchito mphatso za uzimu moyenera:</b></p>
<ol style="list-style-type: none"> <li>1. Anthu amakhalabe osadziwa (12:1; 14:38).</li> <li>2. Magawano amapangika mu thupi la Khristu (12:25).</li> <li>3. Chisokonezo chimakura (14:33).</li> <li>4. Mphatso imodzi yokha ndi imene imagwiritsidwa ntchito nthawi zosne momangoibe-wereza-bwereza, zina zonse ndi zimayiwaliika (14:17, 28).</li> </ol>	<ol style="list-style-type: none"> <li>1. Mpingo udzaphunzitsidwa ndi kulimbikitsidwa (12:7; 14:4, 5, 6, 19, 26).</li> <li>2. Mpingo udzayangika pamodzi, kulimbi-kitsidwa, ndi kutonthzedwa (12:12; 14:3,31).</li> <li>3. Mtendere umatsatira (14:33,40).</li> <li>4. Mphatso zonse zimapatsidwa gawo ndipo zimagwira ntchito yake (12:7-11, 25, 27-31; 14:26).</li> </ol>

## Chaputala 8: Kusunga Mphatso za Uzimu

<p>5. Utumiki wochitira umboni ku dziko umakhala “belu longosokosa” chabe (13:1).</p> <p>6. Alendo amatha kunena kuti “muli osongonekera mitu” (14:24).</p> <p>7. Otayika amakanika kufika pafupi (14:23,33).</p>	<p>5. Mpingo umakonzekera kumenya nkondo (14:8).</p> <p>6. Alendo amatha kunena kuti, “Ameni! Zoonadi, Mulungu ali pakati panu” (14:8).</p> <p>7. Miyoyo umapindulidwira kwa Khristu (14:24-25).</p>
---	--

### Kuphunzitsa Okhulupilira

Mbusa angalimbikitse kugwiritsa ntchito mphatso za uzimu mu mpingo pa kuphunzitsa. Ayenera kuphunzitsa anthu ake za mphatso za uzimu. Kuphunzitsa kwake kuyenera kuphatikizirapo mitu iyi yofunikira:

- chimene mphatso ziri
- kufunikira kwa mphatsozi
- mene mphatsozi zingagwiritsidwire ntchito moyenera mumpingo
- mmene mphatsozi zingamasulidwire kupyolera mu mamembala a mumpingo.

Kodi mbusa angaphunzitse bwanji mu mpingo mwake za mphatso za uzimu? Atha kuyamba ndi kuphunzitsa choonadi chopezeka m’buku lino. Mbusa athanso kuphunzitsa maphunziro otsatana a mphatso za uzimu. Mowonjezera, angaphunzitse kalasi ya Sande sukulu kapena maphunziro a padera opezeka mu nkhaniyi. Njira zophunzitsira zilipo zosiyanasiyana. Komabe, chiphunzitsosho chiyenera kuchokera ndi kukhazikika m’Baibulo. Mbusa ayenera kuphunzitsa zomwe Baibulo likunena za mphatso za uzimu ndi mmene zigwirira ntchito mu mpingo.

### Kupereka Chitsanzo cha Kagwiritsidwe Ntchito ka Mphatso za Uzimu

Mbusa ayenera kuchita zoposa *kungolankhula* ndi anthu ake za mphatso za uzimu. Ayeneranso kuwonetsa okhulupilirawo momwe mphatso zimagwirira ntchito kupyolera m’moyo wa iye mwini. Uwu ndi udindo waukulu. Iye

mwini ayenera “kukhumba zedi” mphatso za uzimu (Onani 1 Akorinto 12:31). Izi zikutanthauza kuti ayenera kufunafuna Mulungu kufikira Mzimu Woyera utamugwiritsa ntchito mu utumiki wa mphatso za uzimu. Ndi kupyolera mu njira yokhayi pomwe iye angathe kukhala chitsanzo cha machitidwe a mphatso.

Abusa, kodi mphatso za uzimu zimagwira ntchito yake momasuka ndi motsatira dongosolo la Baibulo mu mpingo mwanu? Ngati sichoncho, Mulungu akufuna ayambe ndi *inu*. Kudzera mwa inu, Mulungu akukhumba kukugwiritsani ntchito mu mphatso za uzimu mu mpingo mwanu.

### **Kulimbikitsa Okhulupirira Kukugwiritsa Ntchito Mphatso za Uzimu**

Mbusa ayeneranso kulimbikitsa anthu ake ku kukhumba mphatso za uzimu. Angawaphunzitse kuti madalitso amatsikira pa iwo pamene akutumikira mu mphatsozi. Choyamba, okhulupirira adzadalitsidwa pamene adzazipereka okha kwa Mulungu. Tsono, mpingo udzalimbikitsidwa kupyolera mukugwiritsa ntchito mphatso zosiyasiyana. Pomaliza, anthu ozungulira dera lanu adzadalitsika pomwe mpingo udzakhala ukuonetsera mphemvu ndi chifundo cha Mulungu. Odwala adzachiritsidwa. Maukwati opasuka adzamangikanso. Odzazidwa ndi omangidwa ndi ziwanda adzamasulidwa. Ndipo anthu adzapulumutsidwa pamene Mulungu agwiritsa ntchito mpingo wake mu utumiki wa uzimu. Madalitso awa ali umboni woonekeratu kwa anthu adera lozungulira mpingowo.

Mphatso za uzimu zimagwira ntchito yake bwino pamalo *omwe palibe kuopyeza*. Anthu sayenera kuopa kudzudzulidwa kapenanso kuchongedwa nthawi zonse pamene atumikira mphatso za uzimu. Ngati akuchongedwa nthawi zonse, adzayamba kunyalanyaza kapena kukana kumene kutumikira mu Mzimu. Mbusa ayenera kupereka nthawi kwa anthu ake ndi mwayi wophunzilirira kugwiritsa ntchito mphatso za uzimu. Anthu adzalakwitsa nthawi zina. Mbusa wao ayenera kuyembekezera izi; kulakwitsa ndi gawo limodzi la kuphunzira. M’busa ayenera kukonza anthu ake bwinobwino ndi modekha. Iye ayenera kuwakonza modekha ndi mwachikondi. Mbusa awakumbutse zomwe Baibulo limanena za kugwiritsa ntchito mphatso za uzimu moyenera. Chofunikira kwambiri ndi kuti mbusa alimbikitsebe anthu ake mukupitiriza kuyesayesa kutumikira mu mphatsozi.

Mphatso za uzimu zimagwira ntchito bwino pamalo pomwe pali kupezeka kwa Mulungu komvekeratu mwamphemvu. Tingapange malo oterewa kudzera

m’mapemphero ndi m’kulambira. Ndipo tiyenera kumakhala wotsegukira ku Mzimu wa Mulungu nthawi zonse pamene tiri m’mapemphero ku mipingo yathu.

### **Kukhala Ndi Nthawi Yokwanira Mu Mapemphero a Mu Mpingo**

Abusa ena samaona mphatso za uzimu zikugwira ntchito mu mipingo yao. Samamupatsa mwayi Mzimu Woyera kuti awonetsere kupezeka kwake kudzera mu mphatso za uzimu. Abusa oterewa amatanganidwa ndi kulankhula, kuyimba, kuvina ndi kunena zolengeza. Samapereka mpata ku mpingo wakudikira pa Mulungu pomwe akupemphera. Abusa a chiPentekoste ayenera kupereka nthawi ndi mwayi wakulora mphatso za uzimu kutumikira pakati pao.

## **Kupewa Kagwiritsidwe Ntchito Kolakwika ka Mphatso za Uzimu**

Mbusa ali ndi udindo woletsa kugwiritsa ntchito mphatso za uzimu molakwika. Mukutero, amatumikiradi anthu ake monga mbusa ndi kuwatsogolera mu kukula mu uzimu.

### **Kuyang’aniridwa ndi Mbusa**

Mbusa wa chiPentekoste ayenera nthawi zonse kulimbikitsa kugwiritsa ntchito mphatso za uzimu. Kamanso ayenera kuyang’anira kagwiritsidwe ntchito kwa mphatsozi. Mphatso izi siziyenera kugwiritsidwa ntchito molakwika ndi mosoyenera. Mmalo mwake, ziyenera kudalitsa mpingo ndi anthu a m’dera lozungulira mpingowo. Mphatsozi zimakhala temberero m’malo mwa m’dalitso ngati zitagwiritsidwa ntchito molakwika. Chionengeko chachikuru chimachitika ku mpingo ngati mbusa alora kugwiritsa ntchito mphatso za uzimu mosatsata dongosolo la Baibulo.

Mapemphero mu mpingo sayenera kukhala msonkhano wosowa mwambo wa anthu omwe ali mu makanda ndi odzala ndi umunthu chabe. M’mpingo ina, munthu aliyense amaloledwa kuchita chomwe akuwona kuti ndi cholondola kwa iye mwini. Mipingo yotereyi siyipereka ulemmerero kwa Khristu. Paulo akulemba kuti mphatso za uzimu “zonse zichitike koyenera ndi

kolongosoka” (1 Akorinto 14:40). Mbusa ali ndi udindo woonetsetsa kuti dongosolo la m’Malemba likutsatilidwa. Akhristu ena amatha kuwanena abusa awo kuti “siauzimu” pamene atsatira dongosolo loyenera mu mpingo. Iwo sayenera kuwaopa Akhristu oterewa. Abusa enieni amayika chidwi chawo chachikuru pa kulandira chivomerezo cha Mulungu koposa kumangotsutsidwa ndi anthu.

### **Ndondomeko Zoyenera Kutsata Pogwiritsa Ntchito Mphatso**

Baibulo limatipatsa njira za kagwiritsidwe ntchito ka mphatso za uzimu moyenera. Ndondomeko zitatu zingapezeke mu Chipangano Chatsopano.

1. *Tiyenera kukhumba mphatso za mzimu (1 Akorinto 12:31, 14:1, 39).*

Tiyenera kukhumba mphatso za uzimu chifukwa tili ndi ntchito yayikulu yoti tiyigwire. Mphatso za uzimu ndi zida zoperekedwa ndi Mzimu Woyera kuti tigwire nazo ntchito.

2. *Tiyenera kumvetsa zolinga za mphatso za uzimu.* Tanthauzo lathu la mphatso za uzimu<sup>10</sup> likuti ndi zoperekedwa kuti “tikwaniritse chifuniro cha Mulungu Atate.” Paulo anati mphatso za uzimu zinaperekedwa pofuna “kukumangilira mpingo” (1Akorinto 14:26b). Choncho, cholinga cha mphatso ndi kudalitsa thupi lonse la Khristu. Siziyenera kugwiritsidwa ntchito pakungozitamandira kapena kubweretsa ulemmero kwa munthu payekha.

3. *Tiyenera kudziwa kugwiritsa ntchito mphatso moyenera.* Okhulupilira a ku Akorinto sanali osadziwa za mphatso za uzimu (1 Akorinto 12:1). Iwo anali odziwa za mphatso. Kunena moona iwo samasowa mphatso iliyonse ya uzimu (1 Akorinto 1:7). Koma anali osadziwa *kugwiritsa ntchito* mphatsozo moyenera. Amagwiritsa ntchito mphatso za uzimuzi molakwika, makamaka mphatso ya malilime. Tiyenera kumvetsa ndi kutsata ndondomeko za m’Baibulo pogwiritsa ntchito mphatso za uzimu moyenera.

### **Ndondomeko Zoyenera mu Utumiki wa Uneneri**

Kulimbikitsa komanso akuyang’anira mphatso za uneneri kapena mphatso zogwiritsa ntchito mau<sup>11</sup> mu mpingo ndi chinthu cholimba zedi. 1 Akorinto 14

---

<sup>10</sup> Werenganinso Chaputala 7.

<sup>11</sup> Izi ndi mphatso za malilime, kumasulira malilime ndi uneneri: onani gawo III.B ya Chaputala 7.

## Chaputala 8: Kusunga Mphatso za Uzimu

amatiuza momwe mpingo ungasungire mwambo pogwiritsa ntchito mphatso za uzimu muchipembedzo.

1. *Onetsetsani kuti malilime akumasuliridwa nthawi zonse* (1 Akorinto 14:5, 13, 16).

2. *Dikilirani kumasulira* (1 Akorinto 14:27-28). Kodi chiyenera kuchitika ndi chiyani uthenga wa m'malilime ukaperekedwa? Mbusa awuze mpingo kuti udikire chimasuliro cha uthengawo. Alimbikitse anthuwo kulankhula mwachikhulupiliro pamene Mzimu uwafulumizitsa kuti amasulire. Komabe udindo waukulu wakumasulira uthenga umakhala kwenikweni m'manja mwa wopereka uthengawo (1 Akorinto 14:13).

3. *Sungani dongosolo loyenera*. Mphatso ziyenera kutumikiridwa mu dongosolo loyenera (1 Akorinto 14:27). Abusa sayenera kuloleza kuti mapemphero asokonezeke mu njira ina iliyonseyo. Ayenera kuwonetsetsa kuti ndondomeko ya Baibulo ikutsatiridwa nthawi zonse.

4. *Weruzani (Unikani) ziganizo za uneneri*. Kuweruza uthenga ndi kofunika, ndipo kuchitike potsatira chidziwitso. Mphatso za uneneri ziyenera kulandiridwa ndi chidziwitso nthawi zonse. Baibulo limati, “*Ndipo aneneri alankhule awiri kapena atatu, ndi ena azindikire*” (1 Akorinto 14:29). Abusa ndi atsogoleri ena odzazidwa ndi Mzimu ali ndi udindo woweruza mau a uneneri operekedwa mu thupi la Khristu. “Mneneri” yemwe safuna mau ake kuti aweruzidwe sayenera kuloledwa kulankhula (kunenera) mu mpingo.

Kodi atsogoleri odzazidwa ndi Mzimu angadziwe bwanji kuti uthenga wa m'malilimewo ukuchokeradi kwa Mulungu? Apa, mphatso ya chidziwitso cha mizimu ingagwiritsidwe ntchito. Mphatsoyi imaloleza atsogoleri kudziwa kuti ndi mzimu wanji ukumutsogolera m'neneriyo.

Mafunso atatu ayenera kuyankhidwa pamene tiweruza mphatso ya uneneri.

- Kodi uthengawo unagwirizana ndi Malemba a m'Baibulo?
- Kodi uthengawo unagwirizana ndi chitsongozo cha Mzimu mu mapempherowo?
- Kodi uthengawo unamangilira ndi kulimbikitsa mpingo?

Yankho la funso lililonse la mafunso awa liyenera kukhala “Inde.” Ngati sichoncho, ndiye kuti uneneriwo suli mundondomeko yoyenera ndipo tiyenera kulongsola izi motsata Baibulo.

## Chaputala 8: Kusunga Mphatso za Uzimu

5. *Yang'ananitsitani pa chilimbikitso.* Utenga wa Malilime ndi kumafulira kuyenera kumanga ndi kulimbitsa thupi. (Akorinto 14:1-5,12,17). Paulo adafotokoza mfundoyi mwatsatanetsatane: “*Ali nalo lilime, ali nacho chimasuliro. Muchite zonse kumangirira*” (1 Akorinto 14:26). Mbusa ayenera kuonetsetsa kuti mpingo ukumangiliridwa kupyolera mu mphatso ya unereri. Ayenera kumvetsera mwa tcheru nthawi zonse pomwe wina anenera kapena kupereka uthenga m'malilime ndi kumasulira kwake.

6. *Gwiritsani ntchito ulemu woyenera.* Mphatso ziyenera kutumikiridwa mu ulemu ndi mwambo woyenera wodziwikiratu. Kudzoza kwa Mzimu Woyera sichinthu chotipangitsa ife kuti tichite mwano ndi kudzikuzika. Nthawi zonse tiyenera kulingalira kukhuzika kwa anthu ena m'moyo wao. Paulo akuti:

*Koma ngati kanthu kavumbulutsidwa kwa wina wakukhalapo, akhale chete woyambayo. Pakuti mukhoza nonse kunenera mmodzi mmodzi, kuti onse aphunzire, ndi onse afulumidwe.* (1 Akorinto 14:30-31)

7. *Chepetsani chiwerengero cha mauthenga.* Mapemphero a mipingo ina amangopitilirabe osafika pamapeto ndi mauthenga a m'malilime omwe amabwera motsatana. Mbusa asalole izi kuchitika motere. Ayenera kuyika malire a anthu awiri kapena atatu mu mapemphero alionse (1 Akorinto 14:27).

8. *Yang'anirani (kudziletsa) mphatso.* Amene anenera ayeneranso kutengapo gawo lakuyang'anira mphatso yake. Paulo anaonapo kuti “*Ndipo mizimu ya aneneri imvera aneneri*” (Akorinto 14:32). Palibe amene angawiringule, “*Ndinalephera kudziletsa chifukwa choti ndanali pansu pa ulamuliro wa Mzimu Woyera.*” M'neneri woonadi amakhala ndi mphamvu yakuyang'anira (yakuletsa) mzimu wa iye mwini.

9. *Musaletse malilime.* Malilime sayenera kuletsedwa kapena kuyimitsidwa m'mapemphero. (1 Akorinto 14:39). Mulungu akufuna mphatso ya malilime—mu choonadi chake, mphatso zonse – zisaletsedwe kuti zigwire ntchito mu chipembedzo. Izi zikuvomerezidwa motero ndi chiyembekezo chakuti mphatsoyi ikugwiritsidwa ntchito moyenera ndipo ikulimbitsadi mpingo.

10. *Lolani okhawo amene ndi odziwika ndi mpingo kunenera.* Mphatso ziyenera kutumikiridwa ndi mamembala okhawo amene ndi okhulupirika ndi a ulemu wao mumpingomo kapena atsogoleri ena odalirika. Baibulo

limatilangiza ife kuti “dziwani iwo akugwiritsa ntchito mwa inu (ife)” (1 Atesalonika 5:12). Sitiyenera kulola mlendo kapena munthu wosayeretsedwa (moyo wokaikitsa) kutumikira mu mphatso ya uzimuyi pagulu.

*11. Tsogolerani kuchitapo kanthu ku uthenga wa uneneri.* Mbusa ayenera kutsogolera mpingo ku kuchitapo kanthu (kuyankha) moyenera ku mphatso ya uzimu. Ndikutheka kuti uthenga wa uneneri wangoperekedwa kumene mu mpingo. Kenako, abusa angatsongolere mpingo mu nthawi yakupemphera kapena kupembedzera. Angakhosenso kuyitanira anthu ena kutsogolo kuti awapempherere. Abusa ayenera kusamalitsa komanso kugwiritsa ntchito nzeru potsogolera ku kuchitapo kanthu kwa mpingo wonse.

### **Kulangiza Amene Akugwiritsa Ntchito Mphatso za Uzimu Molakwika**

Kodi m’busa angachite chiyani ngati wina ayamba kugwiritsa ntchito mphatso za Mzimu molakwika? Poyamba, mbusa ayenera kulankhula ndi munthuyo payekha komanso mwachinsinsi. Ayenera kumupatsa malangizo a uzimu a momwe angagwiritsire ntchito mphatsozi moyenera. Ndichiyembekezo, kuti munthuyo adzaphunzitsika ndipo adzamvera abusawo. Kenako mpingo udzadalitsika ndipo munthuyo adzakula mu uzimu.

Komabe, nthawi zina munthuyo angapandukire malangizo a abusa ake ndi kupitiriza kutumikira molakwika kapenanso kugwiritsa ntchito mphatso molakwika. Izi zikatero, mbusa ayenera kumudzudzula munthuyo pamaso pa mpingo wonse. Ndi chanzeru kukambirana ndi atsogoleri ena akulu mu uzimu, chigamulo chomaliza chisanaperekedwa kwa munthuyo.

Mutha kufusa, “Kodi ndikoyenera kuletsa wina kulankhula malilime mumpingo?” Yankho ndi “Inde, ndipo izi nthawi zina ndizofunikira. Izi ndizofunikira makamaka pomwe:

- mowonekeratu, mphatso za uzimu zikugwiritsidwa ntchito molakwika,
- wolankhulayo akungopitirizabe kulankhula, koma mpingo siukulimbikitsidwa,
- wolankhulayo akusokoneza bata ndi kudzetsa chisokonezo mu mpingo (1 Akorinto 14:33).

## Chimangiliro

Mbusa ali ndi udindo wolimbikitsa kutumikira momasuka kwa mphatso za uzimu mu chipembedzo. Njira zapaderadera zomwe angalimbikitsire nazo mphatsozi izi ndi monga:

- kuphunzitsa okhulupirira kudziwa komanso kugwiritsa ntchito mphatso za uzimu.
- kukhala chitsanzo cha kutumikira mphatso za uzimu.
- kulimbikitsa okhulupilira kuti azigwiritsa ntchito mphatso za uzimu.
- kulola kukhala ndi nthawi mu mapemhero yakuti mphatso za uzimu zitumikire.

Mbusa alinso ndi udindo woletsa kugwiritsa ntchito mphatso za uzimu molakwika. Iye ayenera aziyang'anitsitsa katumikiridwe ka mphatsozi. Malemba amapereka ndondomeko yoyenera yogwiritsira ntchito mphatso za uzimu:

- khumbani mphatso za uzimu.
- mvetsetsani zolinga za mphatsozi.
- Dziwani mmene mungagwiritsire ntchito mphatsozi moyenera.

Kutumikira mphatso za uneneri ndi ntchito yolimba. Mutha kupeza ndondomeko khumi zofunika kutsata pogwiritsa ntchito mphatso za mau mu 1 Akorinto:

- malilime amasuliridwe nthawi zonse.
- dikirani kumasulira kwa uthenga wa m'malilime.
- sungani dongosolo loyenera.
- weruzani ziganizo zonse za uneneri.
- yang'anilirani pa kumangilirana.
- ikani malire a mauthenga.
- tchinjiridzani mphatso.
- musaletsa mauthenga a m'malilime.
- lolezani okhawo ali odziwika ku mpingo kunerera.

## Chaputala 8: Kusunga Mphatso za Uzimu

- tsogolerani kukuchitapo kanthu ku uthenga wa uneneri.

Mu nthawi zina, iwo a mu mpingo ayenera kukonzedwa mwachinsinsi kapenanso pakati pa mpingo wonse ngati mphatso zikugwiritsidwa ntchito molakwika. Mwachikondi, mbusa ayenera kudzudzula kapena kapena kupereka chilango, atapeza upangiri kuchokera kwa atsogoleri ena akulu mu uzimu.



## Chaputala 9

# Chitsogozo Cha Umulungu Ndi Utumiki Wamphamvu

## Kufunika kwa Chitsogozo cha Umulungu mu Utumiki wa Mphamvu

### Chitsogozo cha Umulungu mu Utumiki wa Yesu

Chilichonse chomwe Yesu anachita chimayang'aniridwa ndi Atate ake. Iye ankachita zokhazo zomwe Atate amamuuza.<sup>12</sup> Werengani mosamala mau otsatirawa omwe Yesu analankhula mu Yohane 5:19-20. (onaninso Yohane 8:28-29; 12:49):

*Indetu, indetu, ndinena kwa inu, sakhoza Mwana kuchita kanthu pa yekha, Koma chimene aona Atate achichita ndicho. Pakuti zimene Iye azichita, zomwezo Mwananso azichita momwemo. Pakuti Atate akonda Mwana namuonetsa zonse azichita yekha: ndipo adzamuonetsa ntchito zoposa izi, kuti mukazizwe.*

Munthu wina amagwiritsidwa ntchito ndi Mulungu pochiritsa odwala. Koma tsiku lina munthuyu anabetcheredwa ndi munthu wosakhulupilira. Iye anati “Ngati ulidi ndi mphatso yamachiritso, chifukwa chiyani supita kuchipatala ndi kukachiritsa wodwala aliyense kumeneko.” Mtumikiyo anayankha nati, “Pamene Yesu anapita kuchipatala, sanachize odwala aliyense

---

<sup>12</sup> Onani Chaputala 5

kumeneko.” Koma wosakhulupilirayo anafunsanso nati, “Ndi liti pomwe Yesu anapita ku chipatala?” “Tsiku lina Iye anapita ku chipatala cha ku Betesda,” mtumikiyo anayankha. “Pita ukadziwerengere wekha mu Yohane 5:1-15.” Ngakhale panali anthu ochuluka ... olumala, akhungu komanso akhate. Yesu adangochiritsapo m’modzi wa iwo.

Nthawi zina Yesu amachiritsa odwala onse omwe amawapeza pamalo. (onani Mateyu 4:23-24, 8:16). Nthawi zina, amatha kungochiritsa m’modzi, monga momwe anachitira pa thamanda la Betesda. Ndi chifukwa chiyani Yesu anangochiritsa munthu m’modzi yekha ku Betesda? Yesu mwini anayankha funso limeneli: “*Sakhoza mwana kuchita kanthu pa yekha, koma chimene aona Atate achita, ndicho*” (Yohane 5:19). Yesu anangochiritsa munthu m’modzi chifukwa ichi chinali chifuniro cha Atate ake.

Ichi ndi chifungulo chofunika kwambiri mu utumiki wopambana wamphamvu. Yesu anatumikira m’mau ndi muntchito pansu pa utsogoleri wa Mulungu. Ifenso, tiyenera kufunafuna chitsogozo cha Atate wathu wakumwamba. Tiyenera kukwaniritsa kumva ndi kudziwa kulankhula kwake. Kupanda kuthekera uku, khama lonse ndi luntha lonse lakufuna kukhazikitsa utumiki wa mphamvu zidzalepherekeratu.

### **Chitsogozo cha Umulungu mu Mpingo Woyamba**

Atumwi anaphunzira kutumikira pakuonera ndi **kutsanzira** utumiki wa Yesu. Monga Yesu, nthawi zonse anafunafuna (ndi kulandira) chitsogozo cha umulungu pamene amatumikira.

A John Wimber anapeza kuti Yesu ndi atumwi aja anachitira umboni nthawi zonse “ndi chitsogozo cha umulungu.” (Wimber & Springer 1986). Mukunena kwina tingati, nthawi zambiri Mulungu anawatsogolera mu utumiki wakuchitira umboni. Tikambirana zitsanzo zitatu pankhaniyi zopezeka mu Chipangano Chatsopano. Chitsanzo choyamba chikukhudza Yesu, chachiwiri Filipino, ndi chachitatu Petro

1. *Yesu ndi mkazi wa ku Samariya.* Mu Yohane 4:4-42 timawerenga za chitsitsimutso chopambana mu Samariya, m’modzi wotchedwa Sukari. Kuyenda kwa Mulungu uku kunatsatira nthawi ya kufalitsa uthenga komwe Yesu anachita. Iye anamchitira umboni, namupindulira kwa Iye mwini, mkazi wochimwa yemwe anamupeza pa chitsime cha m’modzimomo. Poyambilira titi, kodi ndi chifukwa chiyani Yesu anapita ku Samariya? Anapita kumeneko chifukwa Atate ake a kumwamba anamutuma kumeneko. Mu Yohane 4:4,

Yohane akulongosola kuti Yesu, “anayenera kupita pakati pa Samariya.” Kodi kunali kofunika bwanji kuti Iye adutsire mu Samariya? Atate anamukonzera utumiki kumeneko woti akauchite. Mkazi wa ku Sukari amafunitsitsa mpulumutsi. Ndipo Mudziwo unali uli wokonzeka kulandira chipulumutso.

2. *Filipo ndi m’Kalasidindo wa ku Aitiopiya.* Mpingo woyambirira unachitiranso umboni kupyolera mu chitsogozo cha umulungu. Tikuona izi mu nkhani ya Filipo ndi mdindo wa ku Aitiopiya. Machitidwe a Atumwi 8:26 akuti, “*Koma mngelo wa Ambuye analankhula ndi Filipo, nanena, Nyamuka nupite mbali ya kumwera, kutsata njira yotsika kuchokera ku Yerusalemu kunka ku Gaza, ndiyo ya chipululu.*” Mulungu anakonzera Filipo chilinganizo chakukumana ndi munthu wa ku Africa. Munthuyo anali ndi njala yofuna kudziwa Mulungu wa Moyo. Filipo anampeza munthuyu atakwera pa gareta lake, akuwerenga mau mu Yesaya 53:7-8. Mzimu wa Ambuye unalakhula kwa Filipo, “*Yandikira, nudziphatike ku gareta uyu (8:29b).*” Filipo anachita monga anauzidwira, ndipo anamva munthuyo akuwerenga mokweza. Filipo anayamba kulankhula ndi mu Aitiyopiyay; zokambirana zao zinapangitsa kuti munthuyo atembenuke mtima. Chitsanzo ichi chikungosonyeza kuti kunali kofunika kuti Filipo amvere mau a Mzimu.

3. *Petro ku Nyumba ya Korneliyo.* Chitsanzo chachitatu chakutumikira mu chitsogozo cha umulungu chikupezeka mu Machitidwe a Atumwi 10:1-48. Mulungu mwini anakonzera chilinganizo cha kukumana pakati pa mtumwi Petro ndi Korneliyo (kenturiyo wa Chiroma). Kenako Mulungu anayamba kulankhula kwa amuna awiriwa kudzera m’masomphenya. Mulungu analankhulanso mwa chindunji ndi Petro mwa Mzimu Wake (10:19). Nkhani iyi yosangalatsayi ikuwonetsanso kufunikira kwa kumvetsera – ndi kumvera - mau a Mzimu.

Zitsanzo izi zitatu za m’Baibulo zikutiphunzitsa phunziro lamphamvu. Tiyenera kumva ndi kudziwa kulankhula kwa Mulungu kuti titumikire mu mphamvu, pansu pa chitsogozo cha umulungu. Phunziro ili likutitsogolera ife kufunsa: “Kodi munthu angamve bwanji kulankhula kwa Mulungu?” Tiyankha funsoli mu chigawo chotsatirachi mu chaputala chomwechino.

## **Kumva Mau a Mulungu**

Njira zisanu ndi imodzi zakuyankhira funso, “Ndingamve bwanji mau a Mulungu?” Mungaphunzire kudziwa mau Ake pakumvetsetsa ndi kugwiritsa ntchito njira izi.

### **Zindikirani Kuti Mulungu Akulankhula**

Poyamba, tiyenera kudziwa kuti Mulungu amalankhula kua ana ake. Ndi khalidwe lake kulankhulana ndi ife. Monga Atate wokonda, Mulungu amalankhula kwa ana ake mosalekeza.

Mwina simukumva kulankhula kwa Mulungu panopa. Mwina mukungomva bata la umulungu. Chete ameneyu sichifukwa kuti Mulunguyo akukana kulankhula nanu. Kawirikawiri, izi zimachitika chifukwa simudziwa momwe mungamvere kulankhula kwa Mulungu.

Tsiku lina mwini munda amathilira munda wake. Koma anasautsika chifukwa madzi samatuluka mu fafa lake lothilira madziwo. Iye anakalipira m’nzake chifukwa cha kusatuluka kwa madziwo nati, “Palibe madzi akuturuka kudzera mu payipi iyi. Ndinakuuza kuti utsekule mpopiwo!” Mzakeyo adayankha nati. “M’nzanga mpopi ndi wotsekula kuno.” Payipi yako yapindika ku mapetoko ndi chifukwa chake madzi sakutuluka.” Umu ndi momwenso ziliri ife ndi Mulungu. Mulungu akulankhula kwa ife koma sitikumvetsera. Tiri ndi payipi yathu ya uzimu koma yopilingizana.

### **Mvetsetsani Monga Momwe Mulungu Amalankhulira**

Tiyenera kudziwanso momwe Mulungu amalankhulira ndi ife. Yohane anati, “*Nkhosa zimva mau ake (mbusa).... Zimadziwa mau ake (Yoh.10:3b, 4b)*”. Mulungu amalankhula nafe lero lino mu njira zinayi. Tingazitchule njirazi kuti:

- njira yoyambilira ndi yodziwika bwino
- njira ya zisudzo (masewero)
- njira ya chilendo yosapezeka pezeka
- njira yongotsimikizira

Tisanthula njira iliyonse yomwe Mulungu alankhulira nafe lero lino.

1. *Njira yoyambilira ndi yodziwika bwino.* Njira yoyambilira ndi yodziwika bwino ya kulankhula kwa Mulungu kwa munthu lero lino ndi kupyolera mu mau Ake. Tingathe kudziwa zomwe Mulungu akutiiza pongowerenga Baibulo. Iyi ndi njira yokhayo *yodalirika* kwambiri yomwe tingamvere zolankhula za Mulungu. Njira zina zomwe tingamvere mau Ake zimaunikidwa kapena kuweruzidwa kudzera m' mau Ake olembedwa.

2. *Njira ya zisudzo (masewero).* Nthawi zina Mulungu amalankhula kwa ana ake mu zisudzo kapena kuti m' masewero. Zitsanzo za m' Baibulo zina mwa izo ndi maloto, maso mphenya ndi kuchezeredwa ndi angelo. Nthawi zina, Mulungu amalankhula kwa anthu Ake m' mau omvekeratu. Komanso, masiku a lero lino athabe kugwiritsa ntchito njira za zisudzozi polankhula nafe. Komabe, chenjezo ndi lofunika apa. Nthawi zina anthu opanda uzimu amafuna kuwoneka ngati a uzimu pakati pa anthu ena. Anthuwa amati Mulungu walankhula nawo kudzera mu imodzi mwa njirazi. Chisokonezo ndi kukhumudwitsana kumadza chifukwa cha bodza loyipali. Choncho, anthu ambiri odzozedwa amaopa njira ngati zimenezi monga maloto ndi masomphenya.

Nanga, kodi malingaliro athu akhale otani pa njira izi? Tiyenera kuzindikira kuti maloto, masomphenya ndi kuchezeredwa ndi angelo sizinali njira zokhazo zodziwika bwino zomwe Mulungu amalankhulira. Nthawi zambiri amalankhula kudzera mwa Mzimu Wake ku mzimu wa anthu Ake. Komabe, nthawi zina Mulungu amagwiritsa ntchito njira za *zisudzo*. Koma ife siti yenera kuyembekezera Mulungu kuti atilankhule mu njirayi. Komanso siti yenera kukana kukhulupilira ngati Mulungu alankhula nafe mu njira yosayembekezekayi. Mulungu ndi *wopambana* ndipo akhoza kusankha njira ina iliyonse mwa njirazi yotilankhulira ngati afuna kutero.

3. *Njira ya Chilendo Yosapezeka Pezeka.* Njira ya Mulungu yodziwika bwino polankhula nafe ndi kudzera mwa Mzimu Woyera ku mizimu yathu. Zitsanzo ziwiri za mu Chipangano Chakale zikutsimikizira izi. Choyamba ndi cha mneneri Eliya. Iye sanamve kulankhula kwa Mulungu mu mphepo yamphamvu, mu chivomerezi kapena mu moto. Mmalo mwake, Eliya anamva kulankhula kwa Mulungu monga mkunong'ona kwa pang'onopang'ono (1 Mafumu 19:12). Chitsanzo china ndi umboni wa mneneri Yesaya. Iye analongosola Mulungu akulankhula motere: “*ndipo makutu ako adzamva mau kumbuyo kwa iwe akuti, njira ndi iyi yendani inu m' menemo.*” (Yesaya 30:21).

Kulankhulana kwa Mzimu ku mzimu kuli kowonekeratu mu Chipangano Chatsopanonso. Aroma 8:14 akuti “*Pakuti onse amene atsogozedwa ndi Mzimu wa Mulungu, amenewo ali ana a Mulungu.*” Ndipo ndime ya 16 ikufotokoza kuti “*Mzimu yekha achita umboni pamodzi ndi mzimu wathu, kuti tiri ana a Mulungu.* Mavesi awa akutiphunzitsa kuti Mzimu amalankhula mwa chindunji ndi mizimu ya Akhristu obadwanso mwatsopano.

Mtumwi Paulo akutsendera choonadichi polongosolera izi mu 1 Akorinto 2:9-13. Mavesiwa akutivumbulutsira zinsinsi zitatu za momwe Mulungu amalankhulira mizimu yathu.

1. *Mulungu amavumbulutsa choonadi kwa ife kudzera mwa Mzimu wake:*

*Koma monga kulembedwa:  
Zimene diso silinazona, ndi  
Khutu silinazimva,  
Nisizinalowa mu mtima mwa munthu,  
Zimene ziri zonse Mulungu anakonzereratu iwo akumkonda Iye . . .  
Koma kwa ife Mulungu anationetsera izi mwa Mzimu;  
pakuti Mzimu asanthula zonse, zakuya za Mulungu zomwe.  
(1 Akor. 2:9-10)*

2. *Mzimu wa Mulungu umadziwa maganizo a Mulungu.* Paulo anafananiza Mzimu wa Mulungu ndi mzimu wa munthu. Mzimu wa munthu mkati mwa iye mwini umadziwa malingaliro ake. Chimodzimodzinsu, Mulungu amadziwa malingaliro Ake.

*Pakuti ndani wa anthu adziwa za munthu, koma mzimu wa munthuyu uli mwa iye? Momwemonso za Mulungu palibe wina azidziwa, koma Mzimu wa Mulungu. (1 Akorinto 2:11)*

3. *Popeza tinalandira Mzimu wa Mulungu, titha kudziwa malingaliro a Mulungu.* Mzimu wake udzatiululira malingaliro ake mkati mwa mzimu wathu.

*Koma sitinalandira ife mzimu wa dziko lapansi, koma Mzimu wa kwa Mulungu, kuti tikadziwe zimene zipatsidwa kwa ife ndi Mulungu kwaufulu. Zimenenso tilankhula, si ndi mau ophunzitsidwa ndi nzeru za*

*munthu, koma ophunzitsidwa ndi Mzimu.* (1 Akorinto 2:12-13a; onaninso 12:16)

4. *Njira yongotsimikizira.* Pomalizira, titha kumva kulankhula kwa Mulungu kudzera mu njira yongotipatsa chitsimikizo. Njira iyi ndi yosiyana ndi zina zija zitatu talongosola m’mbuyomu. Njira izi Mulungu samalankhula nafe mwachindunji ngati zina zija. Nthawi zina amangogwiritsa ntchito *zochitika* zina ndi zina kapena anthu ena polankhula nafe. Chitsanzo chimodzi cha izi ndi nyengo *yakungokwaniritsa*. Izi ndi nyengo za m’*moyo* wathu zomwe Mulungu amakonza kuti atitsogolere ndi kutionetsa chifuniro chake.

Mulungu amagwiritsanso ntchito okhulupilira ena odzazidwa ndi Mzimu Woyera kuti alankhule nafe. Nthawi zina munthuyo amadziwa kuti uthenga akuperekawo ndi wochokera kwa Mulungu. Nthawi zina, okhulupilirayo amalankhula mau oti iye mwini samawamvetsetsa. Koma Mulungu amapanga uthenga wake kukhala weniweni m’mitima mwathu kudzera m’mauwo.

Nthawi zina Mulungu amalankhula nafe kudzera mu mauthenga a uneneri operekedwa mu nthawi yamapemphero. Mauthengawa amakhoza kukhala a m’malirime ndi kumasulira kwake komanso maulosi.<sup>13</sup> Tiyeneranso kupereka chenjezo pano. Ambiri a ife taonapo njirayi ikugwiritsidwa ntchito molakwika ndi okhulupilira osakhwima (makanda) ndi okhulupilira ochita zinthu mwa phuma. Okhulupirira ena asocheretsedwa ndi kuvulazidwa ndi aneneri abodzawa.

Pali mfundo ziwiri zomwe tingagwiritse ntchito pamene tizindikira kuti Mulungu akulankhula nafe kudzera mwa anthu ena. Poyamba, uthengawo uyenera ugwirizane kwathunthu ndi Mau a Mulungu. Ngati siukugwirizana, tiyenera tiwukane nthawi yomweyo – umenewo siunachokere kwa Mulungu! Kachiwiri, uthengawo ungotsimikizira zomwe Mulungu analankhula kale nafe kudzera mwa Mzimu ku mzimu. Musalore wina aliyense kukuuzani zomwe Mulungu akulankhula nanu popanda kuziganizira mozama. Nthawi zonse funani Mulungu pa inu nokha. Iye adzalankhula ndi mzimu wanu molunjika kupyolera mu Mzimu Wake.

---

<sup>13</sup> Onani gawo III.B mu Chaputala 7

## **Konzekerani Kumva Kulankhula kwa Mulungu**

Nthawi zina timalephera kumva mau a Mulungu akamalankhula nafe. Chimodzi mwa zifukwa zake ndi kuti mitima yathu imakhala yosakonzekera kumva kulankhula kwa Mulungu. Wailesi imayenera kukwaniritsa zinthu ziwiri isanalandire mau ochokera ku malo owulutsira mau a wailesi. Iyenera kulumikizidwa ku magetsi kapena kuyikidwa mabatile, komanso ichunidwe ku malo owulutsira mau oyenera. Ifenso, tiyenera kulumikizidwa ndi “kuchunidwa” moyenera ku Mzimu Woyera. Tikatero, tidzamva kulankhula kwa Mulungu.

1. *Kulumikizidwa.* Kubadwanso mwatsopano kumalumikiza mizimu yathu ku gwelo la mphamvu ya Mulungu: Mzimu Woyera. Paulo analemba “*koma iye wophatikizidwa ndi Ambuye ali Mzimu umodzi*” (1 Akor.6:17). Mzimu Woyera amalowa mwa ife pamene tiri “*obadwa mwa ...Mzimu*” (Yohane 3:5) Tsono timakhala “olengedwa atsopano” mwa Khristu (2 Akorinto 5:17). Ichi ndi chifukwa chake Yesu anati munthu wobadwa mwatsopano akhonza “kuona” ufumu wa Mulungu (Yohane 3:3). Mu choonadi chake “*Munthu wopanda Mzimu ...sangathe kumvetsa ... (zinthu za Mzimu), pakuti ziri za uzimu*” (1 Akorinto 2:14).

Kulumikizidwa ku gwero la mphamvu ya Mulungu kumakhudzanso kubatizidwa mu Mzimu Woyera. Ubatizowu, uli ngati kuonjezera mphamvu ku wailesi kapena kugwiritsa ntchito mlongoti (nthambo) wautali pa wailesi yathu. Tikatero timalandira mphamvu yambiri komanso kumva msanga kulankhula kwa Mzimu Woyera.

2. *Kuchuna.* Timadzichuna tokha ku mau a Mulungu podzipereka kwa Mulunguyo komanso ku chifuniro chake changwiro. Baibulo limatichenjeza ife: “*Momwemo, monga anena Mzimu Woyera, Lero ngati mudzamva mau ake musaumitse mitima yanu*” (Ahebri 3:7-8:a). Tiyenera kusunga mitima yathu yotsekuka ndi yofewa pamaso pa Mulungu. Tcheru lotereli kwa Mzimu Woyera limafunikira kudzichepetsa ndi kumvera. Ichi chimasowa moyo wodzipereka, wokhala ndi nthawi yochuluka mu pemphero ndi kulingalira Mau a Mulungu.

## **Zindikirani Mau a Mulungu**

Iwo onse amene akutumikira Ambuye ayenera kukhala otha kuzindikira kulankhula kwa Mulungu pamene Iye alankhula nafe. Yesu anati, “*Nkhosa zimva mau ake (mbusa)... ndi nkhosa zimtsata Iye chifukwa zimva mau ake*

(Yohane 10:3b-4). Kodi tingalimbikitse bwanji luso lakudziwa kulankhula kwa Mulungu? Zimachitika izi mwa kukhala okhudzidwa muzochita-chita nthawi zonse. (onani Ahebri 5:14). Tiyenera kuphunzira kumva ndi kugonjera kukulankhula kwa Mzimu. Ndipokhapo tingaphunzire kuzindikira kulankhula kwake momveka bwino pamene alankhula.

### **Yesani “Mauwo”**

Mau a *chilimbikitso* ndi ofunika pano. Ndikofunika kwambiri kuphunzira kuyesa “mau” amene timawamva. Umu ndi momwe timadziwira kuti mauwo ndi kulankhuladi kwa Mulungu. Mulungu amalankhula kwa ana ake. Komanso “mau” ena amalankhulidwanso ndipo mokweza kwambiri. Baibulo limatiuzanso kuti pali “mitundu ya mau ochuluka pa dziko lapansi” (1 Akorinto 14:10). Mau omwe timamva atha kungokhala a anthu chabe. Athanso kukhala maganizo athu kapena mau a anthu ena. Titha kumvanso mau a uzimu-maganizo ochokera kwa mizimu yoyipa.

Tiyenera kudziwa kuyesa zomwe timamva. Ndipokhapo pomwe tingadziwe kuti ndi Mulungu akulankhula. Mau onse omwe sagwirizana ndi Malemba a Baibulo ayenera kukanidwa.

Mfundo yomaliza ndi yakumvera (kugonjera). Mwachikhulupiliro, tiyenera kumvera Mau a Mulungu pamene tiwamva. Tiri ndi chifukwa chimodzi chokha chomwe tiyenera kumvetserera kulankhula kwa Mulungu. Timamvetsera ndi cholinga chofuna kumvera ndi kugonjera Iye.

Tiyenera kuyembekezera kulankhulidwa ndi Mulungu. Ndipo tiyenera kumugonjera akatilankhula. Pamene timvera ndi kutsata Mulungu, timakhala ndi luso lakuya mukuzindikira mau ake a Mulungu.

Kudziwa ndi kumvera kulankhula kwa Mulungu ndi zinthu zofunika mu utumiki wa mphamvu. Cholinga chathu chiyenera kukhala kuphunzira kuchita zonse moyenera ndi mopambana.



## Chaputala 10

# Zida za Nkhondo Yathu

## Chiyambi

Mu Chaputala 3, tinaphunzira kuti Yesu anabwera kudzakhazikitsa Ufumu wa Mulungu pansi pano. Akupitirizabe kuchita izi kudzera mu mpingo wake wodzadzidwa ndi Mzimu Woyera. Satana amatsutsana ndi Ufumu wa Mulungu, kupangitsa nkhondo ya uzimu. Sitingazikonde izi. Mwinanso sitingadziwe kuti izi zikuchitika. Koma zoonadi zake ndi zakuti mpingo uli pankhondo yosalekeza ndi ufumu wa m'dima wa Satana (Aefeso 6:12). Ndipo Khristu watipatsa ife mphamvu ndi ulamuliro zomenyera nkhondo ndi m'dani wathu.

*Ndinaona Satana alikugwa ngati mphezi wochokera kumwamba. Taonani ndakupatsani ulamuliro wakuponda pa njoka ndi zinkhanira, ndi pa mphamvu ili yonse ya mdaniyo; ndipo kulibe kanthu kadzakuipsani konse. (Lk.10:18-19)*

Asilikari mu nkhondo iliyonseyo amafunika zida. Ife ndife asilikari mu gulu la nkhondo ya uzimu la Khristu. Tili ndi zida zonse za uzimu zomwe tizisowa kuti tigonjetsere Satana. Paulo anafotokozera mphamvu ya zida za uzimu zimenezi: *“Pakuti zida za nkhondo yathu siziri za thupi, koma zamphamvu mwa Mulungu za kupasula malinga (2 Akorinto 10:4).*

Mu chaputala ichi, tiyamba taona zida zauzimuzi. Kenako, tikambirana momwe tingazigwiritsire ntchito kuti tipambane nkhondo ya uzimuyi polimbana ndi Satana ndi ziwanda zake.

## **Zida Zankhondo Zonse za Mulungu**

Ku Aefeso 6:11, tinauzidwa kuti “Tavalani zida zonse za Mulungu.” Tiyenera kutenga zida za nkhondo za Mulungu kuti tichilimike ndi kulimbana ndi kugonjetsa Satana. Nanga, kodi, zida zankhondo za Mulungu ndi chiyani? Tingazigwiritse ntchito bwanji kuti tigonjetse Satana? Tiyankha funsoli mu chigawo chino ndi chigawo chachitatu.

### **Gwero la Mphamvu Zathu Zomenyera Nkhondo**

Tiyenera kukumbukira kuti Mulungu ndiye gwero la mphamvu yathu yomenyera nkhondo. “*Tadzilimbikani mwa Ambuye, ndi m'kulimbika kwa mphamvu yake (Aefeso 6:10)*. Sitiyenera kudalira pa mphamvu zathu, luso kapena zida zathu pakumenya nkhondoyi. M'malo mwake, Mulungu watipatsa mphamvu ndi thandizo lake. Chimene tiyenera kuchita ndi “*Tavalani zida zonse za Mulungu, kuti (Ife) mudzakhoze kuchirimika pokana machenjerero a mdierekezi (Aefeso 6:11)*.”

### **Zolinga za Zida Zonse za Mulungu.**

Paulo anafokoza zolinga ziwiri za zida za nkhondo yauzimuyi mu Aefeso 6:11-13. Poyamba, zimatiteteza ku chinyengo cha Satana chomwe chimabwera ndi “machenjerero” ake (Aefeso 6:11). Mau oti “machenjerero” amachokera ku mau a chiHelena oti *methodeia*. Mau awa angamasuliridwe mu njira zingapo: msampha, mayendedwe, machitidwe, ukamberembere, ndi chipangizo. Tiyenera kukhala okonzekera ku chiwembu ndi machitidwe ake a m'daniyo. Kachiwiri, tigwiritse ntchito zida izi za uzimu pakuchilimika motsutsana ndi mphamvu za m'daniyo. (Aefeso 6:13).

## **Zida Zankhondo Zisanu ndi Ziwiri mu Zida Zankhondo Zonse za Mulungu (Aefeso 6:14-18)**

Paulo anagwiritsa ntchito monga chitsanzo msilikali wa Chiroma popereka chithunzi cha zida zankhondo zopezeka kwa Akhristu.

*Chifukwa chake chirimikani, mutadzimangira m'chiuno mwanu choonadi, mutavalanso chapachifuwa cha chilungamo; ndipo mutadziveka mapazi anu ndi makonzedwe a Uthenga Wabwino wa mtendere; koposa zose mutadzitengeranso chikopa cha chikhulupiriro, chimene mudzakhoza kuzima nacho mivi yonse yoyaka moto ya woyipayo. Mutengenso chisoti cha chipulumutso; ndi lupanga la Mzimu, ndilo mau a Mulungu, mwa pemphero lonse ndi pembedzero mupemphere nthawi zonse mwa Mzimu, ndipo pochezera pamenepo chichezerere ndi kupembedzera oyera mtima onse. (Aefeso 6:14-18)*

Ndime iyi ili ndi mau ofunikira zedi asanu ndi anayi. Awa akulongosola zida zamphamvu mu gulu la nkhondo loopysa la Akhristu. Tsono tisanthula mwachidule chida chilichonse pachokha pachokha.

### **Choonadi**

Ankhondo a Chikhristu ayenera kuvala chida cha choonadi. “Lamba wa choonadi” atha kuyimira zinthu ziwiri. Akutanthauza Mau a Mulungu, amene ndi choonadi (Yohane 17:17). Timadzaza mitima ndi malingaliro athu ndi Mau a Mulungu. Komanso zikutanthauza kuti tikukhala mu choonadi ndi mu ungwiro.

Kodi ndi machenjerero ati a Satana omwe chida ichi cha choonadi chingagonjetse? Chidachi chitha kugonjetsa bodza lake. Bodza ndi chimodzi mwa zida zamphamvu za m'dyerekezi. Kumbukirani, iye ndi wa bodza ndipo ndi atate wa amabodza onse (Yohane 8:44). Timagonjetsa bodza lake polalikira choonadi cha Mau a Mulungu kuchokera mu mtima woona ndi wokhulupirika.

### **Chilungamo**

Kugonjetsa Satana kumasowekanso kuti tivale chida cha chilungamo. *Chilungamo* chimatanthauzidwa monga chiyanjano chabwino komanso kukhalirana koyenera. Tingakhale a chilungamo chenicheni *ngati* tili mu chiyanjano chenicheni ndi Mulungu kudzera mwa Khristu Yesu. Chiyanjano chenicheni chimatipangitsa kukhala moyenera – kukhala mopanda zilema komanso kukhala moyo wachiyero. Tiyenera “ *kuziphunzitsa ife kuti, pokana chisapembedzo ndi zilakolako za dziko lapansi, tikhale ndi moyo m'dziko lino odziletsa, ndi olungama ndi opembedza*” (Tito 2:12). Mayesero a Satana ofuna

kulondola moyo wokana chilungamo (zinthu osati za umulungu) ndi kulondola zokhumba za pansi pano kwagwetsa Akhristu ambiri amene sanavale zida za nkhoodoyi. Koma kuvala chapachifuwa cha chilungamo kumatithandiza kuchirimika ku mayesero ake.

### **Chikonzekero**

Tiyenera kuvalanso kumapazi kwathu ndi “makonzedwe a Uthenga Wabwino wa mtendere” (Aefeso 6:15). Mu mau ena, tiyenera kukhala atcheru nthawi zonse ku ziwembu za mdani. Petro akuchenjeza kuti, “*khalani odzisungira, dikirani, m’dani wanu mdierekezi monga mkango wobuma, ayendayenda ndi kufunafuna wina akamulikwire.*” (1 Pet.5:8). Tiyenera tikhale ndi zida zonse komanso okonzekera ku chiwembu chilichonsecho cha mdani.

Paulo anati kukonzekera kwathu ku chiwembu cha m’dani kumachokera mu Uthenga Wabwino. Uthenga Wabwino umatipanga ife kukhala atcheru ndi kutikonzekeretisa ku machenjerero a m’dani.<sup>14</sup>

### **Chikhulupiliro**

Chida china chimene tiyenera “kunyamula” pankhondo yathu yolimbana ndi Satana ndi chishango cha chikhulupiliro. Ichi chikuphatikizapo chikhulupiriro cha kupulumutsa – kudalira kwenikweni mwa Mulungu ndi chipulumutso Chake mwa Khristu Yesu. Komabe, chikhulupiliro cha mtundu uwu chiri choposa chikhulupiliro cha kupulumutsa chabe. Ichi chimaphatikiraponso chikhulupiliro chakulandilira mwachangu zomwe Mulungu analonjeza.

Chishango cha chikhulupiliro chimazima mivi yonse yoyaka moto ya woipayo (Aefeso 6:16). Mivi ya Satanayi ndi monga malingaliro osalungama, chilakolako chosafuna kumvera, kuukira, kusilira ndi mantha. Ndi chishango ichi, tingadziteteze ku chiwembu chilichonse cha m’daniyu.

Chikhulupiliro ndi chishango chodalirika chimene ndi *chodzitetezera* nacho. Komabe, sikuti chimangoteteza kokha ai, chingathenso kumugonjetsa m’dani. Pezani nthawi ndi kuwerenga Ahebri 11 – chaputala cha ngwazi za chikhulupiriro chozama. Onani mu Chipangano Chakale ndi kuona mmene amuna ndi akazi amagwiritsira ntchito chida cha chikhulupiliro monga ngati

---

<sup>14</sup> Onani Chaputala 14.

chida *chomenyera* nkhondo. Kupyolera mu chikhulupiro anagonjetsa maufumu, nakhazikitsa chilungamo ndi kulandira zomwe zinalonjezedwa (Ahebri 11:33). Ndipo kupyolera mu chikhulupiro anakhala amphamvu ku nkhondo ndipo anagonjetsa adani achilendo onse (Ahebri 11:34). Baibulo ladzadza ndi nkhani zoterezi. Iwo anagwiritsa ntchito chikhulupiro ngati chida chopambana pakupititsira ufumu wa Mulungu patsogolo m'dziko la pansi pano. Ifenso tiyenera kuphunzira kugwiritsa ntchito chida champhamvuchi cha uzimu moyenerera ndi mopindulitsa.

### **Chipulumutso/Kuomboledwa**

Chipulumutso ndi chida chachisanu mu zida za nkhondo ya Chikhristu yolimbana ndi mdyerekezi. Zoonadi zake ndi zakuti chidachi chimakhudzanso chipulumutso ku tchimo ndi ku gehena. Komanso chimakhudzanso chipulumutso china chilichonse kapena chiombolo chimene chimachokera kwa Mulungu. Izinsu zimaphatikiza kumasulidwa ku ziwanda, matenda, zowawa ndi imfa. Kuomboledwa kuchoka kwa Satana ndi misampha yake kapena machenjerero ake kumapambanidwanso kupyolera mu chidachi.

Kuomboledwa kuchoka kwa Satana kumadza kuchokera kwa Mulungu basi. Chokhacho chomwe tifunika kuchita ndi kungoyitanira pa dzina la Ambuye (Aroma 10:13). Nthawi zina titha kuona ngati tazunguliridwa ndi kumva kukanikizidwa ndi mdaniyo. Komabe, sikuti zonse zathera pamene. Titha kuyitanira pa mpulumutsi wathu wamphamvu yonse, ndipo adzatilanditsa!

### **Mau A Mulungu**

Chimodzi mwa zida za uzimu zamphamvu kwambiri ndi Mau a Mulungu. Paulo adachitcha chidachi lupanga la Mzimu Woyera. (Aefeso 6:17). Lamulo loti titenge lupangali – Mau a Mulungu – lili ndi matanthauzo awiri. Poyamba limatauthauza kuti tiyenera tikhale ndi Buku loyera ngati chida chathu cha nkhondo. Chidachi chimafuna kuwerenga, kuloweza, kuphunzira ndi kulalikirira Mau Ake.

Kachiwiri, titha kukhala ndi Mau a Mulungu wotilankhula ife patokha ngati chida chathuchathu. Anthu ena osanthula Buku Loyera amatchula chidachi kuti mau a “rhema”. Rhema ndi mau a chiGiriki ndipo amatanthauza “mau.” Mau oterewa amakumana ndi chosowa chapaderadera pa nthawi yake.

Atha kukhala mau a luntha kapena a nzeru pamene ali mwa mphatso ya Mzimu Woyera.

Chidachi chitha kugwiritsidwa ntchito pomugonjetsera m'dani kapena kudzitetezera kwa m'daniyo munkhondo ya uzimu. Mau ndi chida champhamvu ngati akuphunzitsidwa ndi kulalikidwa ndi kudzoza kwa Mzimu Woyera. Athanso kutiteteza ku ziwembu za m'dyerekezi. Satana adzatiponyera nkhondo pogwiritsa ntchito bodza ndi mayesero ake. Titha kuchitapo kanthu pogwiritsa ntchito malonjezano a Mulungu. Mdyerekezi atha kubwerera pambuyo ndi mphamvu ya chidachi.

### **Pemphero mwa Mzimu Woyera**

Chida chazimu chomaliza chomwe chikupezeka mu Aefeso 6:18, ndi pemphero mwa Mzimu Woyera. Ili ndi pemphero lina lililonse lodzozedwa ndi Mzimu Woyera kapena lotsogozedwa ndi Mzimuyo. Pemphelori limaphatikizanso kulankhula m'malilime (Aroma 8:26, 1 Akorinto 14:14). Kupemphera mwa Mzimu Woyera ndi chida chazimu chopambana kwambiri. Paulo anati tiyenera kumapemphera mwa Mzimu nthawi zonse. (Aefeso 6:18). Izi ndi zofunika kwambiri makamaka mu nthawinso ya mazunzo ndi masautso.

Madalitso ambiri amatsatira pomwe msilikari wauzimu apemphera mwa Mzimu. Mwachitsanzo:

- Pemphero lathu limatsogozedwa ndi Mzimu Woyera kolingana ndi chifuniro cha Mulungu (Aroma 8:27),
- Malingaliro/maganizo amakhalanso atsopano (Aroma 12:2),
- Moyo wa uzimu umalimbitsidwa (1 Akorinto 14:4),
- Chikhulupiliro chimamangidwa ndi kulimbitsidwa (Yuda 20).

Tatchula pemphero mwa Mzimu monga ngati chida cha uzimu. Onaninso zomwe Paulo adanena ku Aefeso 6:18. Ndipo pempherani... “mwa pemphero lonse ndi pembedzero mupemphere nthawi yonse mwa Mzimu ndipo pochezera pamenepo chichezerere ndi kupembedzera oyera mtima wonse.” Paulo anatipempha kuti tiyenera tidzipempherera oyera mtima onse. Paulo anatipemphanso kuti tiyenera tidzipemphera mosalekeza. Ndipo tipemphere “mwa pemphero lonse ndi pembedzero.” Sitiyenera kulephera kugwiritsa ntchito chida champhamvu ichi cha uzimu.

## Zida za Uzimu Zowonjezera Zisanu ndi Ziwiri

Tsopano tiwona zida za uzimu zina zowonjezera zisanu ndi ziwiri zopezeka kwa okhulupirira. Zina mwa zidazi zakambidwa mwa tsatanetsatane m'machaputala ena m'buku lomwe lino. Komabe zikhala zothandiza kuti tizitchulebe zonse pamodzi mu chaputala chino. Kenako titha kunena mosavuta za zida zopezeka kwa ife mu nkhondo yolimbana ndi Satana.

### Chida Chosala Kudya

Kusala kudya kumagwiritsidwa ntchito pamodzi ndi chida chakupemphera. Marko 9 amatiuza za ka m'nyamata kodzazidwa ndi ziwanda. Ophunzira ena a Yesu anayesera kutulutsa ziwanda mwa m'nyamatayo. Iwo analephera. Bambo wa Mwanayo anagwidwa ndi chisoni chachikulu ndipo kenako anaona Yesu akubwera poteropo. Bamboyo anadandaulira Ambuye kuti atulutse ziwandazo. Mukuyankha kwake Yesu ku pempho la bamboyo, analamulira ziwandazo kuti zituluke mwa m'nyamatayo. Ndipo m'nyamatayo anamasulidwa.

Kenako ophunzira a Yesu anamufunsa Iye “*Nanga bwanji sitinakhoza ife kutulutsa?*” Ndi Iye anati kwa iwo, “*mtundu uwu sukhoza kutuluka ndi kanthu kena konse koma ndi kupemphera* (Marko 9:29). Ndikukhulupirira kuti ziwanda za mtundu uwu zikanalipobe pa dziko. Pemphero ndi kusala kudya ndi njira yokhayo yopezera chipambano pa ziwanda zoterezi.

Malemba akuonetsa zifukwa zinayi zomwe tiyenerera kugwiritsira ntchito chida chazimu chakusala kudya:

- kutithandiza kupeza chisomo pamaso pa Mulungu (Ezra 8:23).
- kumasula omangika mu nsinga (Yesaya 58:6)
- kupeza nzeru ndi chidziwitso chapaderadera (Danieli 9:2-3, 21-22).
- kupeza chifuniro cha Mulungu pa chomwe tikufuna kuchita (Machitidwe a Atumwi 13:2)

Werengani ndi kulingalira mavesi awa. Mavesiwa akuthandizani kumvetsa tanthanzo lenileni la chida ichi cha mphamvu cha kusala kudya.

### **Chida cha Matamando**

Nthawi zambiri matamando samaganiziridwa ngati chida cha nkhondo ya uzimu. Koma, mphamvu yochuluka ya uzimu imapezeka mu nthawi ya kutamanda kokutidwa ndi kudzodza kwa Mzimu Woyera. Makoma a mzinda anagwa pomwe ana a Israyeli anafuula mu matamando (Yoswa 6:16-20). Mu 2 Mbiri 20, timawerenga za oyimbira a mfumu Yehosofati. Iwo anaimbira ndi kutamanda Mulungu muukoma wa kukongola kwa chiyero chake. Iyi inali nzeru ya nkhondo ya Yehosofati. Mulungu anatsikira ku malo ankhondowo ndi kumenya nkhondo mwachibisilirano ku adani a Israyeli. Adaniwo anaonongedwa ndipo a Israyeli anapulumutsidwa (2 Mbiri 20:1-26). Pomaliza, Paulo ndi Sila anapemphera ndi kuyimba motamanda Mulungu mkati mwa usiku ali mundende ya Chiroma. Matamando awo anatsitsira mphamvu ya Mulungu mu ndendemo.

*Ndipo mwadzidzidzi panali chivomezi chachikulu, chotero kuti maziko andende anagwedezeka! Pomwepo pa makomoponse panatseguka; ndi maunyolo a onse anamasuka. (Machitidwe a Atumwi 16:26)*

Pomwe tikutamanda Mulungu, mphamvu yake imatsikira pa malopo, M’dani wathu m’dyerekezi amasokonezeka ndipo amabwerera pa mbuyo. Ichi ndi chifukwa chake matamando ndi chida china cha mphamvu chopezeka kwa okhulupirira.

### **Chida cha Chikondi**

Chikondi chenicheni chili ndi mphamvu yodabwitsa zedi. Chikondi chitha kutsogolera anthu otayika kwa Khristu. Sitingathe kutembenuza mitima ya anthu ena ndi mikangano yathu chabe kapena ziwonetsero za mphamvu. Enawa atha kutembenuka mtima kudzera mu chikondi chenicheni cha Chikhristu.

Saulo wa ku Tariso ndi m’modzi wa omwe anatembenuka mtima chifukwa cha chikondi. Saulo anachitira umboni za chikondi chopambana pomwe ankamuponya miyala Stefano. Miyala imagwa pa thupi la Stefano ndi mphamvu. Komabe, Stefano anapemphera “Ambuye musawaikire iwo chimo ili (Machitidwe a Atumwi 7:60). Izi zikuonetsa zomwe chikondi ndi chikhululuko zinachita pakumukonzekeretsa kukumana kwake ndi Yesu

wouka kwa a kufa pa njira yopita ku Damasiko. Paulo akufokoza momwe tingawiritsire ntchito chidachi.

*Musabwezere munthu ali yense choipa chosinthana ndi choipa. Ganiziranitu zinthu za ulemu pamaso pa anthu onse. ... Koma ngati m'dani wako akumva njala, umdyetse, ngati akumva ludzu, um'mwetse; pakuti pakutero udzaunjika makala amoto pa mutu pake. Musagonje kwa choipa koma ndi chabwino gonjetsani choipa. (Aroma 12:17, 20-21)*

Choipa (chidetso) chitha kugonjetsedwa ndi chabwino. Anthu otayika atha kubwezeretsedwanso kwa Yesu Khristu pogwiritsa ntchito chida cha chikondi.

### **Ubatizo mwa Mzimu Woyera**

Mu Machitidwe a Atumwi 1:8, Yesu anati kuti omutsatira Iye adzalandira mphamvu Mzimu Woyera akadzafika pa iwo. Amalankhula za ubatizo wa m'tsogolo wa Mzimu Woyera. Ubatizowu ndi chida chofunika zedi pa nkhondo ya uzimu.

### **Mphatso za Mzimu Woyera**

Mzimu Woyera amapereka mphatso za uzimu ku mpingo. Chifukwa chimodzi mwa zifukwa zikuluzikulu za mphatsoyi ndi kupereka mphamvu ku mpingo yakumenyera nkhondo ya uzimu. Izi zikutsimikiziridwa ndi mphatso zisanu ndi zinayi za Mzimu Woyera zomwe zikupezeka mu 1 Akorinto 12:2-10. Kudzera mu mphatsozi, mpingo

- umalandira chitsogozo cha kwa Mulungu (mphatso za mavumbulutso),
- umalankhula mau amphamvu ochokera kumwamba (mphatso za uneneri),
- umaonetsera mphamvu ya Mulungu yakugonjetsera m'dani. (mphatso za mphamvu).

### **Chida cha Dzina la Yesu**

Yesu anapereka dzina lake ngati chida chazimu polimbana ndi mphamvu za Satana. Ulamuliro wonse wa umulungu umatithandizira kugwiritsa ntchito dzina la Yesu. Tikagwiritsa ntchito dzina lake monga

momwe anatilangizira, timalankhula ndi ulamuliro wa kumwamba. Mphamvu za ku gehena zimagonja pa dzina lopambana mayina onse. (Afilipo 2:9-11). Yesu anati:

*Indetu, indetu ndinena kwainu, wokhulupirira ine, ntchito zimene ndichita ine adzachitanso, iyeyo; ndipo adzachita zoposa izi; chifukwa ndipita ine kwa Atate. Ndipo chimene chirichonse mukafunse mu dzina langa, ndidzachichita, kuti Atate akalemekezedwe mwa mwana. Ngati mudzapempha kanthu mdzina langa, ndidzachita. (Yohane 14:12-14)*

*Ndipo tsiku limenelo simudzandifunsa kanthu. Indetu, indetu, ndinena kwa inu ngati mudzapempha Atate kanthu, adzakupatsani inu mdzina langa. Kufikira tsopano simunapempha kanthu mdzina langa; pemphani ndipo mudzalandira, kuti chimwemwe chanu chikwaniridwe. (Yohane 16:23-24)*

Atumwi anagwiritsa ntchito dzina la Yesu mu utumiki nthawi zonse. Mu dzina Lake anachiritsa odwala, anatulutsa ziwanda, ndi kugwira ntchito zawo za uzimu. ( onani Machitidwe a Atumwi 3:6,16). Chida champhamvu ichi chazimu chikugwirabe ntchito mpaka lero lino mu chipambano chazimu.

### **Chida cha Uthenga Wabwino**

Mu Aroma 1:16 Paulo anatchula Uthenga Wabwino wa Khristu kuti “*mphamvu ya Mulungu yakupulumutsa munthu aliyense wakukhulupirira.*” Mu Aroma 10:17 ananena kuti Uthenga Wabwino wa Khristu uli ndi mphamvu yobzala chikhulupiriro mu mtima mwa omvetsera uthengawo. Mphamvu ya Mulungu imaonekera poyera pomwe uthenga wa imfa ya Yesu, kuikidwa m’manda ndi kuuka kwa akufa kwake zilalikidwa. Ichi ndi chida cha mphamvu kwambiri.<sup>15</sup>

---

<sup>15</sup>

## Chimangiliro

Mpingo uli pankhondo yaikulu ya uzimu yolimbana ndi Satana, ndi maukulu komanso zimphamvu zake. Mulungu anapereka ku mpingo wake zida za mphamvu zogonjetsera mphamvu za Satana. Zisanu ndi ziwiri mwa zidazi zatchulidwa mu Aefeso 6:14-18. Zina mwa izo ndi izi:

1. Choonadi
2. Chilungamo
3. Chikonzekero
4. Chikhulupiriro
5. Chipulumutso/Chiombolo
6. Mau a Mulungu
7. Pemphero mu Mzimu

Zida zinanso zisanu ndi ziwiri zowonjezera zomwe zikupezeka mu chipangano chatsopano ndi izi:

1. Chida cha kusala
2. Chida cha kuyamika
3. Chida cha Chikondi
4. Ubatizo mu Mzimu Woyera
5. Mphatso za Mzimu Woyera
6. Chida cha dzina la Yesu.
7. Chida cha Uthenga Wabwino.

Iwo omwe akufunitsitsa kupititsa patsogolo utumiki wamphamvu ayenera kukhala “ankhondo” a uzimu aluso. Izi zimafunika luso pogwiritsa ntchito zida khumi ndi zinayi zomwe zatchulidwa mu chaputala chino.



**Gawo III**  
**Kuchitachita Utumiki**  
**Wamphamvu**



## Chaputala 11

# Kuchiritsa Odwala

## Chiyambi

Chaputala ichi chikuonetsa chitsanzo (dongosolo) cha momwe tingatumikirire pakuchiritsa odwala kukhala. Chitsanzochi ndi cha m'Malemba komanso cha mu utumiki. Chitsanzochi ndi cha m'Malemba chifukwa chikutsamira pa ntchito za Yesu ndi atumwi. Chili cha mu utumiki chifukwa timakambirana za kuchiritsa monga atumiki ngati abusa.

Kawirikawiri mlaliki pa msonkhano wa chitsitsimutso amapempherera odwala *en masse* (monga gulu).<sup>16</sup> Posiyanita, m'busa amapempherera odwala m'modzi m'modzi. Odwalayo amakhala yemwe mbusayo amamudziwa ndipo amamukonda.

M'busa weniweni amakhudzidwa kwambiri ndi zofuna komanso zosowa za odwalayo. M'busayo samakakamiza kapena kulepheretsa zotsatira za kupemphera kwao pamodzi. Cholinga cha m'busayo ndi cha umunthu komanso cha uzimu. Iyeyo amafuna wodwalayo achiritsidwe. M'busayo amafunanso kuti munthuyo awone chikondi cha Mulungu m'moyo mwake ndi chikondi cha mpingo pa iye. M'busa sayenera kumuopseza odwalayo kapena kumudzudzula kuti alibe chikhulupiriro posapemphera payekha. M'malo mwake m'busayo (monga ngati Yesu Khristu) ayenera kutumikira mokhudzika ndi mwa chikondi ku zofuna za munthu wodwalayo.

---

<sup>16</sup>Nkhaniyi tiyikambirana bwino lomwe mu Chaputala 15 pokamba za misonkhano ya usodzi.

## Zinthu Zofunika

Mu chaputala chino tikambirana mwatsatanetsatane momwe tingachiritsire odwala. Komabe, tisanayambe kukambirana, tikambirana za malo kaye kapena kuti nyengo ya machiritso. Tiwonanso momwe mtumiki kapena m’busa angakonzekerere payekha utumikiwu.

### Malo a Machiritso

Mau oti “malo amachiritso” amathanthauza nyengo ya kupezeka kwa Mzimu Woyera mu nthawi ya utumikiwu. M’busa amayenera kuyika chidwi chake chonse ku malo amachiritsowa pomwe akutumikira mu utumiki wamachiritso. Luka ananenapo za malo oterewa mu utumiki wa machiritso wa Yesu Khristu.

*Ndipo mipingo yambiri ya anthu inasonkhana kudzamvera, ndi kudzachiritsidwa nthenda zao, ... Ndipo mphamvu ya Ambuye inali ndi Iye yakuwachiritsa. (Luka 5:15b,17b)*

Yesu anachiritsa m’ malo omwe anali odzazidwa ndi kupezeka kwa Mulungu. Yesu amakhudzidwa ndi malo opezeka mphamvu ya umulungu potumikira. Kumbukirani pomwe anapita kukadzutsa mwana wa mkazi wa Yairo kwa akufa. Marko analembapo za nkhanayi:

*Ndipo anafika ku nyumba kwake kwa mkuru wa sunagoge; ndipo anaona chipiringu, ndi ochita maliro, ndi akukuwa ambiri. Ndipo m’mene atalowa, ananena nao, mubuma ndi kulira bwanji? Mwana sanafe, koma ali m’tulo. Ndipo anamseka Iye pwepwete. Koma Iye anawaturutsa onse, natenga atate wa mwana, ndi amache, ajawo anali naye, nalowa m’mene munali mwanayo. Ndipo anagwira dzanja lake la mwana, nanena kwa iye, Talita koumi; ndiko kunena kuti, Buthu ndinena ndi iwe, Uka. Ndipo pomwepo linauka, niliyenda. (Marko 5:38-42a)*

Onani zomwe Yesu anachita asanaonetsere chozizwachi. Iye anatulutsa anthu onse mchipindamo omwe samakhulupirira. Anthu osakhulupirirawa amatsutsana ndi utumiki wake ndipo amalepheretsa zomwe Iye ankafuna

kuchita. Pakuwatulutsa anthuwo Yesu amateteza malo akupezeka kwa Mzimu wamachiritso.<sup>17</sup> Nthawi ina, utumiki wa kuchiritsa wa Ambuye wathu unalepheretsedwa chifukwa cha malo osoweka chikhulupiriro. Izi zinachitika monga kwao ku Nazareti. Marko 5:5-6 akuti:

*Ndipo kumeneko sanakhoza Iye kuchita zamphamvu konse, koma kuti anaika manja ake pa anthu odwala owerengeka, nawachiritsa. Ndipo anazizwa chifukwa cha kusakhulupilira kwao. (Onaninso Mateyu 13:58)*

Zochitika ziwiri izi zikutisonyeza nyengo ziwiri zofunika momwe tikuonetsedwa malo amachiritso. Chionetsero cha kupezeka kwa Mulungu ndi chiyembekezo m'chikhulupiriro zinalipo pamalopo.

1. *Chionetsero cha kupezeka kwa Mulungu.* Kukamba za chionetsero cha kupezeka kwa Mulungu sizitanthauza mkhalidwe *wachilengedwe* chake cha Mulungu *wopezeka paliponse*. Ndi zoonadi kuti Mulungu amapezeka paliponse nthawi zonse. Koma chionetsero cha kupezeka kwa Mulungu zimatanthauza kupezeka kwa Mulungu kokhudzika kapena kuti kowonekeratu. Kupezeka kwa Mulungu kotereku kunatchulidwapo mu Luka 5:17, vesi imene tayilemba m'mbuyomu: “Ndipo mphamvu ya Ambuye inalipo yakuchiritsa odwala.”<sup>18</sup>

2. *Chiyembekezo m'chikhulupiriro.* Chiyembekezo m'chikhulupiriro chinasonyezedwapo ndi m'mayi wina wodwala mu Marko 5:28. Iye anati kwa iye mwini “*ngati ndikhudza chovala chake ... ndidzachira.*” Chikhulupiriro choterechi chimapezeka pomwe anthu akuyembekezera kapena kudikirira chozizwa kuchokera kwa Mulungu. Kukula kwa chiyembekezo m'chikhulupiriro kungathandizidwe ndi kuperekedwa kwa Uthenga Wabwino mwatsatanetsatane (onani Aroma 10:17). Kuperekedwa uthenga kotereku kuyenera kutsindika pa chikhulupiriro ndi pa machiritso. M'busa wanzeru poterepa amayesetsa kukhazikitsa chiyembekezo m'chikhulupiriro chokhazikika m'mitima ya anthu ake.

---

<sup>17</sup>Werenganinso Machitidwe 9:40. Onani kuti Petro anachita chimodzimidzi pamene anaukitsa Dorika kwa akufa.

<sup>18</sup>Baibulo ndilodzala ndi zitsanzo zosangalatsa za zionetsero zakupezeka kwa Mulungu. Onani Eksodo 3:1-6; 2 Mbiri 7:1-3; Luka 2:8-9; Machitidwe 2: 1-13; ndi 1 Akorinto 14:22-25.

### **Kudzikonzekeretsa kwa Mtumiki**

Mu chaputala 5 tinafotokoza za kukonzekera utumiki wamphamvu m’magawo akuluakulu. Pano, tisanthula kukonzekera kukumana ndi machiritso. Magawo asanu ndi limodzi adzakukonzekereetsani kulandira machiritso pa odwala.

Pemphani kuti mudzadzidwenso kwatsopano ndi Mzimu Woyera. Pempherani kufikira mutamva kudzoza kwake.

- Zikumbutseni kuti kodi Yesu ndi ndani, zimene amachita ndipo anakuuzani kupanga chiyani. Kumbukirani kuti chigonjetso chimabwera kudzera m’chikhulupiriro mwa Yesu Khristu.
- Zikhutureni inu mwini mu “undekha.” Simungapange chilichonse cha uzimu mu mphamvu za inu nokha (Yohane 15:5).
- Osayerekeza kukakamiza chozizwa kuti chichitike. Osayesera kuyerekeza momwe Mulungu angachiritsire kapena momwe kuombedwa kungabwerere. M’Baibulo, palibe anthu awiri omwe anachiritsidwa munjira zofanana kwenikweni.
- Funsani Mulungu “Mukufuna kuchita chiyani?” (Onani Yohane 5:19-20). Pezani chifuniro cha Mulungu pa nkhanayi. Kenako dziiperekeni ku chifuniro Chakecho ndi kutumikira molimbika mtima.
- Pempherani kawirikawiri mu Mzimu. Mvetserani mwatcheru ku mau ake kuti akutsogolereni.

### **Mmene Kudzoza kwa Utumiki Kumabwerera**

Mu Chaputala 7, tinanena kuti mphatso za Mzimu zimabwera monga ngati “kudzoza” kwa Mzimu Woyera. Izi zikuphatikizanso mphatso za mphamvu zitanu zija.<sup>19</sup> Kodi, tsono, kudzozaku kumabwera bwanji pa munthu kuti atumikire? Atumiki ena amachitira umboni za kumva kuchuluka kwa “mphamvu” mkati mwao mwadzidzi. Iwowa amafotokozeranso izi pogwiritsa ntchito mau ngati “kutentha” kapena “kutakasa.” Enanso amanena za kumva chifundo chachikuru ndi munthu wovulazikayo. Komanso ena mwadzidzi amangomva kufulumizidwa mwa chikhulupiriro choyembekezera kuti ntchitoyo igwirikadi. Yesu nthawi zonse “amadzazidwa ndi chifundo”

---

<sup>19</sup>Izi ndi mphatso za machiritso, mphatso ya chikhulupiriro, ndi mphatso ya kuchita zamphamvu.

asanachiritse odwala (Marko 1:41). Mu njira iliyonseyo yomwe kudzoza kungabwerere, mudzamva mkati mwa moyo wanu kuti machiritso a Mulungu achitikadi. Mudzadziwa kuti Mzimu wa Mulungu ali pa ntchito yake.

## **Chitsanzo cha Magawo–Atatu Pochiritsa Odwala.**

Chitsanzo cha magawo-atatu chomwe chikufotokozedwa pano ndi machitidwe a m’chikhalidwe cha umunthu potumikira mu utumiki wa mphamvu. Chitsanzochi chikuchokera pa utumiki wochiritsa anthu wa Yesu ndi atumwi. Chitsanzochi chimayankha mafunso atatu ofunikira mu kukumanizana ndi machiritso.

1. Kodi chosowa chenicheni cha munthuyo ndi chiyani?
2. Kodi ndingapitirire bwanji ndi utumiki pa chosowachi?
3. Kodi ndimulangiza bwanji munthuyo utumiki wa kulimbana ndi machiritso ukatha?

### **Gawo Loyamba: Kufunsa Mafunso Achidziwitso**

Gawo loyambirira mukukumana ndi machiritso ndilolunjika pakupeza chosowa chenicheni cha munthuyo. Kawirikawiri timangoyamba kum’pemphepera munthu osamufunsitsa chosowa chake ndi chiyambi cha chosowacho. Nthawi zina timachita izi ngakhale tisanadziwe choti tipemphepere. Izi ndiko kuchepekedwa chidziwitso komanso ngozi yayikuru chifukwa timapemphepera chinthu cholakwika. Ndipo munthuyo timasiyana naye asanakumane ndi yankho la chosowa chake. Choncho, tiyenera kuyamba kulimbana ndi utumiki wa machiritso pakufunsa mafunso angapo.

Funso loyambilira labwino ndi: Kodi mukufuna Mulungu akuchitireni chiyani lero? Tiyenera “kumvetsera” yankho mwa chidwi munjira zinayi. Ndi *makutu* athu, timamvetsera mwa chidwi ku zimene munthuyo akulankhula. Ndi *maso* athu, timayang’anitsitsa munthuyo kuti tione momwe akuchitira mukupezeke kwa Ambuye. Ndi *mtima* wathu, timamva ululu wa munthuyo ndi kumvetsera chikhulupiriro chake. Ndi *mzimu* wathu, timamvetsera mwatcheru ku zomwe Mzimu wa Mulungu akulankhula nafe.

Tiyenera kupanga zisankho ziwiri zofunika zedi tisanapemphere. Poyamba, tiyenera kupanga chisankho cha *kafufuza* matenda. Kenako, tipange chisankho cha *utumiki*.

1. *Chisankho cha kafufuza*. Adokotala asanamuthandize munthu wodwala amayenera apange chisankho chakufuza matenda. Izi zikutanthauza kuti poyamba ayenera kupeza chomwe chikumuvuta wodwalayo. Ayeneranso azindikire chiyambi cha matendawo. Mayankho operekedwawo amamuthandiza dokotalayo kupeza njira yomwe angamuthandizire wodwalayo. Izi ziri chimodzimodzinso kwa iwo omwe atumikira mu mphamvu ya Mzimu. Tiyenera kudziwa:

- pomwe munthuyo akumva kupweteka,
- chifukwa chiyani ali ndi vuto lotere,
- ngati chiyambi cha matendawo ndi monga mwa chilengedwe kapena ndi ziwanda.

Mayankho ku mafunsowa adzatithandiza kupeza njira ya momwe tingatumikilire kwa munthuyo.

2. *Chisankho cha utumiki*. Nzeru ya chithandizo cha Dokotala yimatsamira pa mfundo yake “yakuyesa” ya zachipatala. Momwemonso mfundo yathu ya Utumiki yimatsamira pa mfundo ya kuyesa ya Mzimu Woyera. Tizidzifunsa tokha, kodi ndi koyenera kuti nditulutse ziwanda kapena ndingopemphera pemphero la chikhulupiriro. Kodi ndigwiritse ntchito njira iti ya Mubaibulo, mu nthawi yakuchiritsayi. Apa timayenera kumvetsera mwatcheru zomwe Mzimu Woyera akutiiza panthawiyi.

### **Gawo Lachiwiri: Utumiki wa Kulimbana**

Gawo lachiwiri mu kukumana ndi machiritso tikulitchula kuti *utumiki wa kulimbana*. Mu gawo ili timachitapo kanthu potsatira zimene tapeza mu nthawi yakufunsa mafunso achidziwitso. Timapempha Mzimu Woyera kuti atsike ndi kuwonetsera mphamvu zake pamene tikutumikira. Timachita izi potsatira njira zina za izi kapenanso zonsezi:

- kukhudza munthuyo,
- kugwiritsa ntchito mau a chikhulupiriro,

- kugwiritsa ntchito ulamuliro wa chikhulupiriro,
- kulengezera zotsatira za ntchito yogwirikayo,
- kuphunzitsa
- kuonetsera mphamvu ya Mulungu,
- kupemphera pemphero la mgwirizano,
- kumanga ndi kumasula,
- kugwiritsa ntchito njira zina za m’Baibulo.

Tikambirana zina mwa njirazi kutsogolo kwa chaputalachi.

Mulungu amafuna ife tikhalebe atcheru ku zimene Iye akuchita. Tiyenera kuyang’anitsitsa zizindikiro za ntchito ya Mzimu pakudzifunsa tokha funso lachifungulo ili: “Kodi Mulungu akuchita chiyani mu nthawi ino?” Popitiriza, titha kumufunsa munthuyo mafunso ena othandiza ngati awa:

1. Mukumva chiyani mthupi mwanu?
2. Kodi ululu wachoka?
3. Kodi mukumva kuti china chake chikuchitika mthupi mwanu?

Munjira iyi, timapeza chomwe Mulungu akuchita mwa munthuyo. Ndipo timapitirira kutumikira mwa chikhulupiliro ndi motsatira chitsogozo cha Mzimu.

Ndikofunika zedi kuti tisasiye msanga kupemphera pa kupempherera machiritso. Nthawi zina, machiritso amabwera mu magawo magawo, amatenga nthawi yochulukirapo (Marko 8:22-25). Tiyenera kupitiriza kupemphera mpaka munthuyo atachiritsidwa kapena Mzimu atatilamulira kuti tisiye.

### **Gawo Lachitatu: Uphungu Wachitsogozo Atatha Mapemphero**

Utumiki wathu wa machiritso umakhudzanso kupereka uphungu kwa anthu amene tapemphera nawo. Nthawi zonse Yesu amapereka *uphungu-wachitsogozo* kwa anthu omwe anawapempherera.<sup>20</sup> Mwina munthuyo walandira kale machiritso ake. Tiyenera kumulimbikitsa kuti akhale mu chikhulupiriro ndi kumvera kwa Yesu Khristu. Nthawi zinanso, munthuyo

---

<sup>20</sup>Onaninso Marko 5:19; Yohane 5:14; 9:35-39.

sangachiritsidwiretu kotheratu. Apa tiyeneranso kumulimbikitsa pa kukhulupirira Mulungu kuti amuchiritsa kotheratu.

Tipange chiyani ngati munthuyo sakuchiritsidwa titamupempherera? Tiyenera timutsimikizire za chikondi cha Mulungu chosalekeza ndi za mphamvu ya Khristu yakuchiritsa. Ndipo tiyenera kulonjeza kupitiriza kukhulupirira Mulungu mpaka munthuyo atachiritsidwa kotheratu ngati nkotheke. Tithanso kumpempha munthuyo kudzakhala nafenso pa mapemphero ena a machiritso.

## **Njira za m’Baibulo Zochiritsira Odwala**

Kodi Yesu amachiritsa bwanji odwala? Ili ndi funso lofunika chifukwa Yesu ndiye chitsanzo chathu chachikulu mu utumikiwu. Utumiki wamachiritso wa Yesu uyenera kukhala chitsanzo chomwe tingamagwiritse ntchito mu utumiki wathu wa machiritso.

A Jim Miller anazindikira izi pokhudzana ndi utumiki wa Yesu:

Chinthu chofunika chimodzi chidzazivumbulutsa chokha pamene mukusanthula njira za Khristu mu utumiki Wake wochiritsa odwala. Iye sanachiritse odwala mu nthawi ziwiri koma munjira yofanana. Komabe, ndi kofunika kumvetsa kuti Iye anagwiritsa ntchito njira zoposera khumi mu njira yopanda malire komanso mukuphatikiza njirazo ina ndi inzake. (n.d., p. 3)

A Miller analembanso mfundo zopambana mu chithunzi: “Utumiki Wamachilitso wa Khristu mu Uthenga Wabwino” ndi “Njira zomwe Anagwiritsira Atchito Yesu Khristu Pochiritsa.” Mu izi, a Miller anaonetsera kuti mu mabuku a Uthenga Wabwino mwalembedwa nkhani zakuchiritsidwa anthu zokwana makumi anayi ndi imodzi zomwe Yesu anatumikiramo. Zolembedwa zotsatirazi zambiri zake zatengedwa mu mfundo za a Miller.

## **Kulankhula Mau**

Njira yodziwika kwambiri yomwe Yesu anagwiritsa ntchito pochiritsira odwala ndiyo kulankhula mau kwa odwala. Nthawi zina amalamulira odwalayo kuti achite china chake.

- Tambasula dzanja lako. (Marko 3:6),
- *Mnyamata iwe, ndinena ndi iwe, Tauka.* (Luka 7:14),
- *Tauka, yalula mphasa yako, nuyende.* (Yohane 5:8).

Nthawi zinanso Yesu amalamula ziwanda kuti zituluke.

- *Khala uli chete, nuturuke mwa iye.* (Marko 1:25),
- *Turuka iwe, mzimu wonyasa, kwa munthuyu!* (Marko 5:8),
- *Mzimu wasalankhula ndi wogontha iwe, Ine ndikulamulira iwe, turuka mwa iye, ndipo usalowenso mwa iye.* (Marko 9:25).

Nthawi zinanso Ambuye wathu amalankhula ndi chiwalo cha munthuyo, nthendayo kapenanso maonekedwa a matendawo.

- *Takonzedwa! (Yeretsewa).* (Mateyu 8:3, 41),
- *Tatseguka!* (Marko 7:34),
- *Penyanso!* (Luka 18:42).

Nthawi zocheperapo, Yesu amangozindikira chikhulupiro cha munthu.

- *Chikhulupiro chako chakuchiritsa.* (Mateyu 9:22, Luka 18:42b),
- *Mkaziwe, kudwala kwako.* (Luka 13:12),
- *Muka, mwana wako ali ndi moyo.* (Yohane 4:50).

## **Kukhudza: Kukhudza (Kusanjika) ndi Manja**

Njira ina yomwe Yesu ankagwiritsa ntchito pochiritsa odwala ndi kusanjika manja (kukhudza) pa odwalayo.

- *Ndipo anamkhudza dzanja lake, ndipo malungo anamleka mkaziyo.* (Mateyu 8:15).

- *Yesu, ... nakhudza maso ao. Ndipo pomwepo anapenyanso.* (Mateyu 20:34).
- *(Yesu) nalonga zala zake m'makutu mwake ... nakhudza lilime lake. Ndipo makutu ake anatseguka, ndi chomangira lilime lake chinamasulidwa.* (Marko 7:33, 35).
- *Ndipo Iye anaika manja ake pa munthu aliyense wa iwo, nawachiritsa.* (Luka 4:40).

### **Kuchitapo Kanthu pa Chikhulupiriro**

Nthawi zina yesu amangozindikira ndi kuyankha chikhulupiriro. Chikhulupilirochi chimabweretsa machiritso. Nthawi zambiri amayankha chikhulupiriro cha munthu wolandira machiritsoyo.

- *Mkaziwe, chikhulupiliro chako ndi chachikuru; chikhale kwa iwe monga momwe wafunira* (Mateyo 15:28).
- *Muka, chikhulupiliro chako chakupulumutsa iwe* (Marko 10:52).

Nthawi zinanso Yesu amayankha chikhulupiriro cha anthu ena. Abale ake a munthu wina wolumala anabwera naye kwa Yesu kuti amuchiritse. Yesu anawona chikhulupiriro cha anzake a wolumalayo ndipo anamuchiritsa (Marko 2:5).

### **Chifundo**

Mu Uthenga Wabwino alembamonso kuti nthawi zina Yesu amangokhala ndi chifundo zedi chomufulumizitsira ku kuchiritsa odwala.

- *Nachitira iwo chifundo, nachiritsa akudwala ao* (Mateyu 14:14).
- *Ndipo Yesu anagwidwa chifundo, natasa dzanja namkhudza iye ... Ndipo pomwepo kate linamchoka.* (Marko 1:41-42).
- *Ndipo pamene Ambuye anamuona, anagwidwa ndi chifundo chifukwa cha iye, Usalire.*
- *Ndipo anayandikira nakhudza chitatha; Ndipo wakufayo anakhala tsonga, nayamba kulankhula* (Luka 7:13-15).

### **Kutulutsidwa kwa Mphamvu**

Yesu anagwira ntchito yake yonse mu mphamvu komanso mukudzoza kwa Mzimu Woyera. Baibulo limafotokoza mwa chindunji za choonadi ichi. (Luka 5:17, Machitidwe a Atumwi 10:38). Zambiri mwa zozizwa zake zimachitika monga mwa zotsatira za kutulutsidwa kwa mphamvu imene imayendelera kuchoka mwa Iye ndi kulowa m' matupi mwa odwala. Mphamvu iyi imadzetsa machiritso pa odwala.

- *Munaturuka mphamvu mwa Iye, nichiritsa onsewa* (Luka 6:19).
- *Wina wandikhudza Ine; pakuti ndizindikira Ine kuti mphamvu yaturuka mwa Ine* (Luka 8:46).

### **Kupemphera mu Dzina la Yesu**

Kawirikawiri, ophunzira a Yesu mu buku la Machitidwe a Atumwi anachiritsa odwala. Iwowa amachita izi potsanzira momwe Yesu Khristu amachitira. Komabe, iwo anaonjezerapo chinthu chimodzi chofunika kwambiri. Anatumikira mu “dzina la Yesu”. (Marko 16:17-18; Machitidwe a Atumwi 4:10). Ifenso, tiyenera titsanzire njira za Yesu zochiritsira odwala. Tiyenera kuchita izi mu dzina Lake la mphamvu zonse!.

### **Kudzoza ndi Mafuta**

Buku la Marko 6:13 limati ophunzira a Yesu amachiritsa odwala pakuwadzoza ndi mafuta. “*Ndipo anaturutsa mizimu yoipa yambiri, nadzoza mafuta anthu ambiri akudwala, nawachiritsa.*” Buku la Yakabo 5:14-15 likutiuzza momwe tingapempherere odwala mwakuwadzoza ndi mafuta:

*Pali wina kodi adwala mwa inu? Adziitanire akuru a Mpingo, ndipo apemphere pa iye, atamdzoza ndi mafuta m'dzina la Ambuye: ndipo pemphero la chikhulupiliro lidzapulumutsa wodwalayo, ndipo Ambuye adzamuukitsa; ndipo ngati adachita machimo adzakhululukidwa kwa iye.*

Mu ndime iyi, taphunzira maphunziro atatu ofunika okhudza kupempherera odwala powadzoza ndi mafuta. Poyamba tikuwona kuti uwu ndi utumiki wa “akulu a mpingo” iwo omwe ali okhwima mu uzimu ndipo ndi

atsogoleri pa mpingo. Akulu a mpingo amayenera kuphunzitsidwa momwe angapempherere odwala.

Taonanso kuti kudzoza ndi mafuta kuyenera kulumikizana ndi pemphero la chikhulupiriro. Simafuta omwe amachiritsa.. Mafutawo ndi chizindikiro chabe cha Mzimu Woyera. Pemphero la chikhulupiriro ndi lomwe limachiritsa munthuyo.

Pomaliza, taphunziranso kuti tiyenera tizikhudzidwanso ndi moyo wa uzimu wa munthu wodwalayo. Tchimo litha kulepheretsa machiritso a umulungu. Kawirikawiri akulu a mpingo ayenera kutsogolera wodwalayo m'mapemphero akulapa ndi kutembenuka mtima. Ngati nkotheke akulu a mpingowo ayenera kuchita izi asanapempherere machiritso a munthuyo.

## **Chimangiliro**

Chitsanzo cha ndondomeko zitatu chimatitsogolera ife kudziwa momwe tingapempherere odwala. Ndondomeko zitatuzi ndi:

1. Kufunsa mafunso achidziwitso.
2. Kukumanizana ndi utumiki.
3. Uphungu wachitsogozo atatha mapemphero.

Yesu ndi atumwi akutipatsa ife zitsanzo za m'Baibulo m'mene tingapempherere odwala. Tasanthula njira zisanu ndi ziwiri za kupempherera ndi kukhulupirira machiritso.

Njira zake ndi izi:

1. Kulankhula mau
2. Kukhudza: kukhudza (kusanjika) ndi manja
3. Kuchitapo kanthu pa chikhulupiriro
4. Chifundo
5. Kutulutsidwa kwa mphamvu
6. Kupemphera mu dzina la Yesu
7. Kudzoza ndi mafuta

Ife ndife atumiki Akhristu ndipo tinalandira lamulo lake lakutumikira. Tiyenera kulalikira Uthenga Wabwino wa Mulungu ndi kuchiza odwala. Ambuye wathu anatipatsa ife chitsanzo chodabwitsa kuti titsatire. Ntchito yathu ndi kutumikira mwa chikhulupiliro ndi momvera. Tiyenera kutsanza njira zake, kupemphera mu dzina Lake, ndi kuyembekezera Iye kuchita mbali yake yakuchiritsa.



## Chaputala 12

# Kutulutsa Ziwanda

## Chiyambi

Mpingo unatumizidwa ku dziko ndi Uthenga Wabwino . Imodzi mwa ntchito zake zofunika kwambiri ndi kugonjetsa mphamvu za m'dima. Mpingo umapanga izi kudzera mu dzina la Yesu. Timadziwa kuti chozizwa choyamba kulembedwa m'buku la Marko ndi chokhudzana ndi Yesu kutulutsa chiwanda (Marko 1:21-27). Kenako Yesu anati ichi chidzakhala chizindikiro choyamba kutsatira okhulupirira, monga momwe zalembedwera mu lamulo lalikuru la kutumiza “*m'dzina langa adzatulutsa ziwanda*” (Marko 16:17b). Izi zikusonyeza kufunika kwa kutha kutulutsa ziwanda.

Mu chaputala chachitatu, taphunzira momwe kubwera kwa ufumu wa Mulungu kumatsitiridwa ndi kulimbana ndi mphamvu za Satana. Ziwanda za Satana zimayesetsa kulimbana ndi kuletsa ufumu wa Mulungu kupita patsogolo. Chocho, atumiki a Uthenga Wabwino ayenera kulimbana ndi kutulutsa ziwanda paliponse pomwe akumana nazo.

Chaputala chino chikupereka njira zotulutsira ziwanda zomwe zingapezeka ziri mwa munthu. Poyamba, tiona kuti kodi ziwanda ndi chiyani ndi momwe zimalowera ndi kukhalira mwa munthu.

## Kuzindikira Adani Athu

### Kupezeka kwa Ziwanda

Baibulo (makamaka mabuku anayi oyambilira otchedwa a Uthenga Wabwino) limanenetsa kuti ziwanda zilipodi. Limafotokoza mwachindunji kuyipa kwa mkhalidwe wa ntchito zao. Zina mwa ntchitozi ndi kupereka

“mphamvu kwa anthu ochimwa (monga mfiti) omwe amafuna mphamvu zodabwitsa pakati pa anthu. (O’Donovan 1992, p. 235). Kawirikawiri Yesu amakumana ndi ziwanda ndipo amazitutsa. Komanso analamulira mpingo Wake kuti ukhale ndi utumiki onga omwewu (Marko 16:17, Luka 9:1-2).

### **Maonekedwe Odziwika Nawo a Ziwanda.**

Kodi ziwanda zili ngati chiyani? Baibulo limatiphunzitsa izi pokhudza chilengedwe ndi mkhalidwe wao:

1. *Ziwanda ndi zolengedwa zamoyo zenizeni* (Luka 4:33-35, Machitidwe a Atumwi 16:16-17, Yakobo 2:19). Ziwanda siziri zinthu chabe zopanda moyo zongokhala chimphamvu chabe cha m’aganizo. Ziwanda ndi zamoyo zenizeni zokhala ndi maganizo awoawo, zifuniro komanso ziri ndi machitidwe a umunthu.

2. *Ziwanda ndi mizimu* (Genesis 3:1; Chivumbulutso 16:13-14). Ziwanda ndi mizimu yopanda matupi awoawo. Izo zimafuna nthawi zonse kukhala m’matupi a anthu.

3. *Ziwanda ndi zamphamvu*. Ziwanda zili ndi nzeru komanso mphamvu (Luka 8:29; Machitidwe a Atumwi 16:16-17). Komabe, sizili ngati Mulungu yemwe ali wamphamvu yonse ndi wosalengedwa. Ziwandazi ndi zolengedwa komanso zili ndi mphamvu zokhala ndi malire. Izo sizingathe kulimbana ndi kugonjetsa mphamvu zazikulu za Mulungu.

4. *Ziwanda ndi za chikhalidwe chonyasa choonongeka* (Marko 1:23; Aefeso 6:12). Ziwanda zinaperekedwa kotheratu ku tchimo ndi kuchikhalidwe choukira. Choncho, izo zili zonyasa mchikhalidwe, zankhanza komanso zoipa kwa munthu.

### **Zolinga ndi Ntchito za Ziwanda**

Angelo amakhumba kungokwaniritsa chifuniro cha Mulungu. Mu njira ngati yomweyi, ziwanda zimakhumba kukwaniritsa chifuniro cha Satana. Cholinga chenicheni cha Satana ndi kumenyana nkondo ndi Mulungu ndi kuyesetsa kumuvulaza. Ziwanda zimagawana cholinga ichi ngakhale kuti zimadziwa kuti sizingalimbane ndi mphamvu ya Mulungu kapena kumuvulaza. Choncho, ziwandazi zimayesetsa kuvulaza Mulungu mosamulunjika. Zimachita izi pakugwera ndi kulusira omwe amakonda Mulunguyo: mtundu wa anthu. Ziwanda zimavulaza anthu maka mu njira zitatu. Njirazi ndi:

- Kupangitsa anthu kuzipembedza.
- Kumangilira anthu m'nsinga za ukapolo.
- Kupangitsa anthu khungu ku choonadi.

1. *Kupangitsa anthu kuzipembedza* (1 Akorinto 10:19-21). Ziwanda zimafuna anthu kuti azizipembedza (chimodzimodzinsu Satana). Mu njira iyi, zimalanda mapembedzero ochoka kwa anthu ndi kupita kwa Mulungu wao omwe ali akeake a Mulungu.

2. *Kumangilira anthu m'nsinga za ukapolo* (Luka 13:11; Ahebri 2:14). Ziwanda zimafuna kumamangilira anthu m'nsinga za mantha, matenda ndi khalidwe lonyasa. Mu njira iyi, zimaononga chifaniziro cha Mulungu mwa munthu.

3. *Kupangitsa anthu khungu ku choonadi* (Machitidwe a Atumwi 10:38; 2 Akorinto 4:4; 2 Timoteyo 2:25). Ziwanda zimayesetsa kulepheretsa anthu kukhulupirira choonadi cha Mulungu. Izo sizimafuna kuti anthu azisangalala ndi ubale wangwiro ndi Mulungu wao. Ziwanda zimafunanso kumalepheretsa anthu ku kukalowa kumwamba.

A O'Donovan (1992) anatchula mitundu ingapo ya machitidwe a ziwanda. Zotsatirazi ndi njira zisanu ndi ziwiri momwe ziwanda zimayeserera kutivulazira:

1. *Chinyengo*. Ziwanda zimagwiritsa ntchito mabodza pakulimbikitsa maudani, zipembedzo zonyenga, ngakhalenso ziphunzitso zachinyengo mu mpingo (Yohane 8:44; I Timoteo 4:1; 2 Petro 2:21).

2. *Kupha ndi kupanga chiwawa*. Ziwanda zimabweretsa chiwawa, ululu ngakhalenso imfa kwa omwe zikuwalamulira, ngati sizinathamangitsidwe mwansanga (Yohane 8:44).

3. *Kuzunza*. Ziwanda zimazunza anthu mu njira izi:

- Matenda m'thupi la munthu (Yobu 2:7, Machitidwe a Atumwi 10:38)
- Khungu ndi kusalankhula (Mateyu 12:22)
- Misala (Luka 8:27-29)
- Kulumala (Luka 13:11-16)

4. *Kulimbikitsa khalidwe lonyasa la chiwerewere*. Baibulo limatiuza mobwerezabwereza za “mizimu yonyasa.” Mauwa amakamba za mkhalidwe wonyasa wa ziwandazo. Komanso amatanthauza maganizo onyasa,

zikhumbokhumbo ndi zitchito zomwe ziwanda zimalimbikitsa anthu kuchita (Mateyo 10:1; Marko 1:23, 3:11).

5. *Kutchinga ntchito ya Uthenga Wabwino*. Taona kale kuti ziwanda zimasokoneza ntchito yakulalikira Uthengo Wabwino. (Aefeso 6:12; 1 Atesalonika 2:18).

6. *Kusautsa ana a Mulungu* (Luka 22:31; 2 Akorinto 12:7). Ziwanda zimavutitsa, kukhumudwitsa ndi kufooketsa okhulupirira nthawi ina iliyonse yomwe izo zafuna kutero.

7. *Kulimbikitsa kupembedza mafano ndi machitachita aumfiti* (Deuteronomo 32:16-17; 1 Samueli 15:23; 1 Akorinto 10:19-20). Ziwanda zimalimbikitsa ndi kupatsa mphamvu mfiti, kupembedza mafano komanso kupembedza mizimu ya anthu akufa.

### **Kulowedwa Ziwanda**

Ziwanda zimazunza ndi kulamalira omwe zakhala mwa iwo munjira zingapo. Njira yosautsa kwambiri imatchedwa “kulowedwa ziwanda.” Ziwanda zimakhala mwa munthu pakulowa mwa iye ndi kumalamulira moyo wake. Ziwandazo zimalamalira moyo wake wonse kapena gawo chabe la moyo wamunthuyo. Ulamuliro wa ziwandazi pa moyo wa munthu umakhala wokhazikika komanso nthawi zina umakhala wa kanthawi chabe. Kulowedwa ziwanda kumakhudza anthu odzazidwawo mu njira zingapo. Zina mwa izo ndi:

1. Mavuto owoneka ndi maso mthupi lao (Marko 1:26), monga ngati kugontha mkhutu, kusalankhula komanso khungu. (Mateyo 9:32-33, 12:22);
2. Chilakolako chofuna kudzipha kapena kudzivulaza mwini. (Marko 5:5, 9:22);
3. Kudzimbuka, komanso mantha pa kutchulidwa kwa dzina la Khristu (Marko 1:24);
4. Kusinthika kwa umunthu, kapenanso kusoweka kwa chikumbumtima. (Marko 9:26);
5. Umunthu wachilendo umalankhula kudzera mwa munthuyo (Luka 8:28);
6. Kuchuluka moposera kwa mphamvu za umunthu.

7. Nzeru yovuta kuyilongosola kwake komanso mphamvu za matsenga. (Machitidwe a Atumwi 16:16-17)

Kodi m’Khristu angadzazidwa ndi ziwanda? Yankho ndi “Ayi!” M’Khristu obadwanso mwatsopano atha kuyesedwa, kunyengedwa, kuchitidwa chiwembu, ngakhalenso kuzunzidwa kumene ndi ziwanda zongobwera. Ngakhalebe izi ziri chomwechi ndi zosatheka kwa m’Khristu kulowedwa ziwanda. Chiwanda sichingalowe ndi kulumulira mwana wa Mulungu.

Mfundo zitatu zikuperekera umboni pa chikhulupiriro ichi. Poyamba, Chipangano Chatsopano sichinatchulepo za okhulupirira kapenanso kuti obadwa mwatsopano kukhala odzazidwa ndi ziwanda. Sichinaperekenso ngakhale chitsanzo cha chiwanda chitatulutsidwa mwa mwana wa Mulungu. Kachiwiri, kumasulidwa ku ziwanda kumachitika nthawi ya chipulumutso, ya kutembenuka mtima.<sup>21</sup> Kachitatu, palibe kalata ya Atumwi imene inafotokozapo za kudzazidwa ndi ziwanda monga chenjezo kwa Akhristu.

Mfundo zitatu zafotokozedwa pamwambazi zikutsimikizira chikhulupiriro choti Akhristu sangalowedwe ziwanda. Komabe, izi zingathe kuchitika kwa *munthu wobwerera m’mbuyo* m’moyo wa Chikhristu kapenanso kuti *m’Khristu wakugwa* (Mateyu 12:43-45; 2 Petro 2:20-21). Anthu ena amanena kuti anatulutsapo ziwanda mwa “M’Khristu odzazidwa ndi ziwanda.” Ndikukhulupirira kuti M’Khristu wotere anali wotayika amene anali kuyenda mu uchimo.

### **Satana ndi m’Dani Wogonjetsedwa**

Tikamadzudzula ndi kuturutsa ziwanda tiyenera kusunga m’maganizo athu mfundo zoonadi ziwiri izi: Poyamba, mphamvu za Satana m’nyengo ino inapatsidwa malire ndi mphamvu ya Mzimu Woyera (2 Atesalonika 2:7). Kudzera mwa Mzimu, tili ndi mphamvu yoposa yakulamulira ziwanda. Kachiwiri, mphamvu za Satana ndi ziwanda zake zinagonjetsedwa pa mtanda wa Kalvari (Yohane 12:31). Akolose 2:15 akuti: *Atavula maukulu ndi maulamuliro, anawaonetsera poyera, nawagonjetsera nako.*”

---

<sup>21</sup>Onaninso maka mu nthawi ya Filipo ku chitsitsimutso cha ku Samariya mu Machitidwe a Atumwi 8:5-8.

Satana ndi ziwanda ndi adani ogonjetsedwa tsopano. Ndi zoonza kuti Satana ndi ziwanda zake akumenyabe nkhondo ndi anthu. Komabe Satanayu sangalepheretse kukula kwa mpingo chifukwa cha ntchito yopambana yomwe Khristu anayichita pa mtanda paja.

## **Mmene Tingatulutsire Ziwanda**

Tsopano tisanthula za nkhani ya kuturutsa ziwanda kapenanso kuti kumasula a m'nsinga za Satana. Poyambilira tikambirana za mtumiki wotulutsa ziwandayo.

### **Mtumiki Womasula a m'Nsinga (Kulanditsa)**

Msilikali wabwino amadzikonzekeeretsa yekha kukamenya nkhondo. Chomwechonso aliyense amene akufuna kukhala mtumiki wotulutsa ziwanda ayenera kudzikonzekeeretsa yekha. Mmusimu muli m'ndandanda wa zinthu zisanu zofunika mu nkhondo ya uzimu.

1. Mtumiki ayenera kuzindikira kuti kutulutsa ziwanda ndi nkhondo yeniyeni. Azindikirenso kuti akukumana ndi m'dani weniweni komanso woopsa ndipo sayenera kuyitengera nkhondoyi chibwana.
2. Mtumiki ayenera kudzazidwa ndi Mzimu Woyera chifukwa nkhondoyi ndi ya uzimu.
3. Mtumiki afunika kudzipereka kwathunthu ku chifuniro cha Mulungu (Yakobo 4:7).
4. Mtumiki ayenera kudziwa bwino momwe zida zake za uzimu zimagwirira ntchito (Aefeso 6:10-18). Ndipo ayeneranso kudziwa kugwiritsa ntchito zidazi moyenera mu nkhondoyi.
5. Mtumiki ayenera kukhala ndi chikhulupiro champhamvu mu chigonjetso cha mtanda ndi m'mwanzi wa Khristu. Mwa iye payekha ayenera kukhala ndi ulamuliro wa Yesu Khristu m'moyo wake.

### **Utumiki Womasula a m'Nsinga**

Otsatira a Yesu Khristu anapatsidwa mphamvu ndi zida zomasulira anthu omwe ali omangidwa ndi ziwanda. Yesu ndi chitsanzo chatu ndi chitsogozo pa nkondo ya uzimu (Luka 4:18-19; 31-37). Watiyitana ife kuti timutsatire ku nkondoyi. (Marko 16:15-18).

Yesu watipatsa mphamvu zomwe timazisowa pomasula omangidwa ndi ziwanda. Kudzazidwa ndi Mzimu Woyera komanso mphatso za Mzimu Woyera zimatithandiza kubweretsa ziwanda poyera ndi kuzivumbulutsa.<sup>22</sup> Mzimu Woyera amatipatsanso mphamvu ndi ulamuliro wotulutsira ziwandazi (Luka 9:1-2; 10:17-19).

### **Ndondomeko Yakumasulilira**

Kutulutsa ziwanda ndi kuphwasula nsinga za ziwandazo ndiyo ntchito ya Mulungu. Ntchito iyi imachitika kudzera mwa Mzimu Woyera yekha basi. Kugonjetsa ziwanda ndi chizindikiro cha kupezeka kwa Ufumu wa Mulungu pamalo. Izi zimasonyezanso mphamvu ndi umulungu wa Khristu mu dziko lake lino.

Mfundo zitatu zotsatirazi ziyenera zikhalepo potulutsa ziwanda, monganso muja takambira pochiritsa odwala. Mfundozi ndi kufunsa mafunso achidziwitso, utumiki wakulimbana komanso uphungu wachitsogozo kwa omasulidwa ku ziwanda.

*1. Kufunsa mafunso achidziwitso (Kufufuza).* Nthawi zina kufunsa mafunso munthu wodzazidwa kapena womangidwa ndi ziwanda kumakhala kosatheko. Koma ngati zili zotheka, kufunsa mafunso achidziwitso ndi mfundo yoyambilira mu ndondomeko yotulutsa ziwanda. Mfundoyi imatipangitsa kuzindikira kupezeka kwa ziwanda mwa munthuyo. Timachita izi kudzera mu mphatso ya chizindikiro cha mizimu yonyasa. Komanso mizimu imasautsika ndi kupezeka kwa Mulungu pamalopo. Nthawi zina zimadzivumbulutsa zokha. Nthawi zambiri zinachita izi mu utumiki wa Yesu Khristu (Marko 1:23; 5:6-7).

Ngati zili zotheka, timulimbikitse munthu amene akufuna kumasulidwa ku ziwanda kukudzipereka kwa Ambuye. Izi ziyenera kuchitika kutulutsa ziwanda kusanachitike. Tiyenera kumutsogolera ku pemphero la kulapa ndi

---

<sup>22</sup>Mphatso za mavumbulutso ndizo zimagwira ntchito apa, maka za chizindikiro cha mizimu.

kuvomereza kuchimwa kwake. Tiyenera titsindike pa machimo omwe akukhudzana kwambiri ndi mphamvu komanso nsinga za mizimu yonyasa. Munthuyo ayenera kunena molimba mtima kuti wasiya kutsatira zinthu zonse za ziwanda komanso zokonda za umunthu.

2. *Utumiki wakulimbana.* Timayamba utumiki weniweniwo wa kulimbana ndi mphamvu mu dzina la Yesu, kufunsa Mzimu Woyera kuti ufike. Tiyenera kutengapo nthawi kufikira titamva kupezeka kwa mphamvu ya Mulungu. Apa tsono titha kupitiriza utumiki wathu wa kutulutsa ziwandazo. Chimodzi kapena zingapo mwa zinthu izi zingagwiritsidwe ntchito:

- Kukhazika chete chiwanda mu dzina la Yesu (Mateyu 16:19; 18:18),
- Kulamula chiwanda kutuluka ndikusamuka, kapenanso kumumasula munthuyo kukumangidwako (Luka 4:35),
- Kulamula chiwanda kuti chisadzalowenso mwa munthuyo (Marko 9:25).

Nthawi zina, chiwandacho chimalimbalinga kapena kukakamira (Marko 1:24-26; Luka 8:28). Zikatero mtumikiyo ayenera apitirizebe utumiki wake ndi chikhulupiriro mpaka chigonjetso chitaonekera. Kawirikawiri, kutulutsa ziwanda kumapangitsanso ziwanda kupanga zionetsero zosiyanasiyana zina mwa izo zomuvulaza munthuyo (Luka 4:33-35; 9:39,42). Mtumiki sayenera kunyengelera kapena kuopa machenjerero oterewa. M'malo mwake, ayenera kulamulira ziwandazo kukhala chete (Marko 1:25, 34). Kenaka, mu ulamuliro wa Khristu, atha kulamulira ziwandazo kuti zituluke ndi kuti zisakhalenso mwa munthuyo (Marko 9:25).

Baibulo la “Full Life Study”(1990 tsamba 81) pali nkhani mutu wake “Mphamvu pa Satana ndi Ziwanda.” Nkhaniyi yimasanthula mfundo zisanu ndi ziwiri zomasulira anthu ku nsinga za ziwanda.

1. Zindikirani kuti sitili mu nkondo yolimbana ndi thupi kapena mwazi koma ndi maukulu a uzimu ndi maulamuliro komanso zimphamvu za woyipayo (Aefeso 6:12).
2. Khalani pamaso pa Mulungu, odzipereka kwathunthu ku choonadi Chake ndi chilungamo (Aroma 12:1-2; Aefeso 6:14).

3. Khalani ndi chikhulupiriro kuti mphamvu za Satana zitha kuononedwa mu dera lililonse la ulamuliro wake (Machitidwe a Atumwi 26:11; Aefeso 6:16; 1 Atesalonika 5:8), ndi kuzindikira kuti okhulupilira ali yense ali ndi zida za mphamvu zauzimu zoperekedwa ndi Mulungu pakugonjetsera malinga a Satana (2 Akorinto 10:4-5).
4. Lalikirani Uthenga Wabwino wa ufumu wa Mulungu kupyolera mukudzazidwa ndi Mzimu Woyera (Mateyu 4:23; Luka 1:15-17; Machitidwe a Atumwi 1:8; 2:4; 8:12; Aroma 1:16; Aefeso 6:15).
5. Limbanani ndi Satana ndi mphamvu zake maso ndi maso pakukhulupirira m'dzina la Yesu (Atumwi 16:16-18), pakugwiritsa ntchito Mau a Mulungu (Aefeso 6:17), pakupemphera mwa Mzimu (Machitidwe a Atumwi 6:4, Aefeso 6:18), pakusala kudya (onani Mateyu 6:16) ndi pakutulutsa ziwanda (Mateyu 10:1; 12:28; 17:17-21; Marko 16:17; Luka 10:17; Machitidwe a Atumwi 5:16; 8:7; 16:18; 19:12).
6. Pempherani maka kwa Mzimu Woyera kuti atsutse otayika pokhudzana ndi machimo ao, chilungamo ndi chiweruzo chomwe chikubwera (Yohane 16:7-11).
7. Pempherani ndi kukhumba mwachidwi zionetsero za Mzimu Woyera kudzera mu mphatso za machiritso, malilime, zozizwa, zizindikiro ndi zodabwitsa (Machitidwe a Atumwi 4:9-33; 10:38; 1 Akorinto 12:7-11).

3. *Uphungu wachitsogozo kwa omasulidwa ku ziwanda.* Gawo lomaliza pa nthawi yakumasula omangika mu m'nsinga ndi kutsogolera anthu omwe tawapempherera komanso kuwalangiza Munthu amene wakhala pansu pa ulamuliro kapena chitsogozo cha ziwanda amafuna chithandizo chokwanira. Uphungu wotsatirapo, thandizo la m'moyo komanso mapemphero amasoweka kwambiri kwa otulutsidwa ziwandayo. Iyi sinthawi yomusiya yekha munthu wotereyu. Tiyenera kumuonetsa chikondi chenicheni komanso chithandizo cha muuzimu.

Mtumiki ayenera kukhala ndi chidziwitso cha moyo wa uzimu mwa munthuyo. Ngati kuli kofunikira, m'tumiki ayenera kumutsogolera ku chipulumutso komanso ku mtendere ndi Mulungu. Komanso mtumikiyo

ayenera kupemphera ndi munthuyo kuti alandire ubatizo wa Mzimu Woyera. Yesu anatichenjeza za zinthu izi molunjika:

*Koma mzimu wonyasa, utaturuka mwa munthu, umapitirira malo opanda madzi kufunafuna mpumulo osaupeza. Pomwepo unena, ndidzabwerera kunka kunyumba kwanga, konkuja ndinaturukako; ndipo pakufikako uipeza yopanda wokhalamo, yosessedwa ndi yokonzedwa. Pomwepo upita, nutenga pamodzi ndi uwu mizimu yina inzake isanu ndi iwiri yoipa yoposa mwini yekhayo, ndipo ilowa, nikhalamo. Ndipo matsirizidwe ake a munthu uyo akhala oyipa oposa mayambidwe ake (Mateyu 12:43-45a)*

Munthuyo adzafunabe thandizo polimbana ndi mavuto atsalira mkati mwake a umunthu kapenanso a uzimu. Tiyenera kulimbikitsabe kukumana kwathu ndi munthuyo mpaka atamasulidwa kwathunthu ku m'nsingazo. Tiyenera kusonyeza chikondi nthawi zonse pofuna kudzisungira ulemu kwa anthu omwe tikuwatumikira.

## Chimangiliro

Okhulupirira Yesu alamuliridwa kutulutsa ziwanda (Marko 16:17). Ndi zoonadi kuti Satana ndi m'dani wogonjetsedwa. Ngakhale zili choncho, iye akanalibe ndi mphamvu. Titha kumudzudzula kudzera mu mphamvu ya Mzimu Woyera ndi m'kudzoza kwa Mzimuyo basi.

Ziwanda ndi zamoyo zenizeni zomwe zimafunafuna kuvulaza anthu. Izo zimatsutsana ndi kukula kwa ufumu wa Mulungu kudzera mu mpingo. Zina mwa njira zawo ndi izi:

- Chinyengo
- Kupha ndi kuchita chiwawa
- Kuzunza
- Kulimbikitsa khalidwe lonyasa la chiwerewere
- Kutsekereza ntchito ya Uthenga Wabwino
- Kusautsa ana a Mulungu
- Kulimbikitsa kupembedza mafano ndi machitachita aumfiti.

Ndondomeko ya kutulutsa ziwanda imatsatiranso chitsanzo cha mfundo zitatu cha machiritso—Mfundozi ndi izi:

- Kufunsa mafunso achidziwitso
- Utumiki wakulimbana
- Uphungu wachitsogozo kwa omasulidwa ku ziwanda.



### Chaputala 13

# Kugonjetsa Mizimu ya m'Madera

## Mizimu ya m'Madera ndi Chiyani?

Mizimu ya *m'madera* ndi dzina lina la ziwanda, monga momwe taphunzilira mu chaputala 12. Komabe, ziwanda izi ziri ndi ntchito ina yapaderadera. Ziwanda zina zimazunza anthu okha basi. Mizimu ya m'madera imalamulira dera lapaderadera, gulu la anthu, fuko, mtundu ngakhalenso mudzi.

### Ziwanda ndi Zadongosolo Lokhazikika

Baibulo limaphunzitsa kuti mizimu yoyipa ili ndi maudindo ndi ntchito zosiyanasiyana.

*Chifukwa chake kulimbana kwathu sitirimbana nawo mwazi ndi thupi, komatu nawo maukulu ndi maulamuliro ndi akuchita zolimbika adziko lapansi a mdima uno ndi auzimu a choipa m'zakumwamba. (Aefeso 6:12; onaninso Akolose 2:16)*

Malemba amanena kuti mizimu yolamulira iri ndi madera akeake, midzi, mafuko, ndi mitundu ya anthu pa dziko lapansi. Kolingana ndi a Peter Wagner

Satana amayika ziwanda zomwe zili ndi maudindo akuluakulu kolingana ndi ndondomeko ya maudindo a mizimu yoyipa mukulamulira mayiko,

zigawo, mizinda, mafuko, ngakhalenso mabugwe ena padziko lonse lapansi. (1990 tsamba 77).

A Wesley Deuwel analongosolera m'malo mwake maudindowa a ziwanda (1986, tsamba 104-105). Iwo analemba kuti:

Sitidziwa bwino lomwe momwe Satana anagawira maudio a ziwanda mu ufumu wake. Malemba amagwiritsa ntchito mayina angapo pofotokoza za mizimuyi ndipo nthawi zambiri mu njira yosonyeza kuti zili pansu pa ufumu wa Satana. Mayina ena a chi Herene (Griki) ndi malo omwe atha kupezeka zalembedwa m'munsimu:

<i>archai</i>	olamulira	1 Akor. 15:24; Aef. 1:21; 3:10; 6:12; Akol. 1:16; 2:10, 15)
<i>exousiai</i>	maulamuliro	(1 Akor. 15:24; Aef.1:21; 3:10; 6:12; Akol. 1:16)
<i>dunameis</i>	mphamvu	(Aroma 8:38; 1 Akor. 15:24; Aef. 1:21)
<i>kuriotes</i>	maufumu	(Aef. 1:21; Akol. 1:16)
<i>throni</i>	mpando wachifumu	(Akol. 1:16)
<i>archontes</i>	atsogoleri, akalonga	(1 Akor. 2:6)
<i>kosmokrantes</i>	olamulira a dziko lapansi	(Aef. 6:12)

Mayina amaudindo ali pamwambapa angatanthauze maudio a ulamuliro, mbiri zosiyanasiyana kapenanso ntchito zosiyanasiyana pansu pa ulamuliro wa Satana. Chofunika kudziwa ndi chakuti zolengedwa zonse izi zili ndi malire mu mphamvu zao, nzeru komanso zochita zawo. Ziwanda zonse zinagonjetsedwa ndi Khristu pa mtanda. Ndipo izo zonse zimadziwa kuti zikugodikira chiweruzo, chomwe chidzatsatiridwa ndi chilango chamuyaya (Mateyu 8:29).

### **Satana Ndiye Wamkulu Wao**

Mizimu ya ulamuliroyi ili pansu pa utsogoleri ndi ulamuliro wa Satana. Baibulo limati, “*Tidziwa... Ndipo dziko lonse lapansi ligona mwa oipayo.*” (1 Yoh. 5:19). “Dziko lonse” (mu Griki, *kosmos*) kulankhula za chilichonse

chokhudzana ndi umoyo wa munthu pa dziko la pansi. Zina mwa izo ndi munga ndale, zipembezo maphunziro, magulu osiyanasiyana komanso nkhanu za chuma. A George Otis analemba kuti,

Zolinga za Satana ... ndikupeza ulamuliro pa miyoyo ya anthu pakukhazikitsa ulumuliro wake - mu za ndale, chuma, chipembedzo - zimene iwo analenga (1991, tsamba 88).

Satana amakhazikitsa ulamuliro wakewu kudzera mu m'gwirizano wa mphamvu ya ulamuliro wa ziwanda maukulu, zimphamvu ndi mizimu yonyasa (Aefeso 6:12). Otis (1991 tsamba 94) analongosola m'gwirizanowu motere:

Lero, maudindo a mizimu yonyasa *amazungulira* pansuponse ndi kuyendetsa (kuyang'anira) madera ndi anthu omwe ali kale mu ufumu wa satana komanso kumenya nkondo ndi onse omwe sali mu ufumu wake. M'malemba, anthu ena "auzimu amphamvu" (mizimu ya maudindo akuluakulu) imadziwika bwino ndi maina a m'madera omwe ikulamulira. Izi ndi munga kalonga (mwana wa mfumu) wa ku Perisiya (Daneil 10:13), kalonga wa ku Helene (Greece) (Daniel 10:20). Kalonga wa ku Turo (Ezekieli 28:12) ndi mizimu ya ku Babulo (Chivumbulutso 17:3-6). Nthawi zinanso, mphamvu zotsogolera za usatana zimadzionetsera munga a milungu ya m'madera, munga Beli ku Babulo (Yeremiya 51:44), Baala Zebubu wa ku Ekroni (2 Mafumu 1:2-3 komanso Apoliyoni wolamulira dziko la kuphompho (Chivumbulutso 9:11).

Mwachidule, mizimu ya m'madera ndi ziwanda zokhala ndi maudindo akuluakulu. Izozizimalamulira kapena kufunafuna kulamulira madera kapena magulu momwe zimakhala.

## **Kodi Ntchito ndi Njira za Mizimu ya m'Madera ndi Ziti?**

### **Ntchito za Mizimu ya m'Madera**

Ntchito yoyambilira ya ziwanda za m'madera ndi kusunga mabungwe, madera kapenanso magulu a anthu mu ukapolo. Zimayesetsa kulepheretsanso anthu kukhulupirira Uthenga Wabwino ndi kutembenuka mtima napulumutsidwa (2 Akorinto 4:4). Imodzi mwa njira zomwe mizimuyi imagwiritsa ntchito ndi kulimbikitsa atsogoleri osiyanasiyana ngakhalenso oyendetsa maboma kuchita monga mwanzeru za mizimuyo (onani Chivumbulutso 16:14). A Douglas Pennoyer (1990) anakhulupirira kuti ziwanda zimalamulira m'madera pogwiritsa ntchito anthu ofunikira m'deralo. Iwo analongosola izi “Ukapolo wa gulu” umalimbikitsidwa pa anthu ndi mizimu iyi ya maudindo akuluakulu:

Ziwanda zomwe zimatumikira mwa anthu zithanso kulamulira madera mwakulepheretsa anthu kulandira Uthenga Wabwino m'miyoyo yao. Cholinga cha ziwanda ndi kusunga anthu mu ukapolo wa m'dima wa Satana, mwa njira ya ukapolo wa gulu kapenanso kuti mudzi wonse. Izi zimalepheretsa munthu payekha kuukira ndi kulowa mu ufumu wa kuwala (1990, tsamba 250).

### **Njira za Mizimu ya m'Madera.**

Kodi mizimu ya m'madera imalepheretsa bwanji anthu kukulandira kuwala kwa Uthenga Wabwino? Imodzi mwa njira zake ndi kupangitsa khungu anthu ku choonadi:<sup>23</sup>

*Koma ngatinso Uthenga Wabwino wathu uphimbika, uphimbika mwa iwo akutayika; mwa amene mulungu wa nthawi yino ya pansi pano unachititsa khungu maganizo awo a osakhulupirira, kuti chiwalitsiro cha Uthenga Wabwino wa ulemerero wa Khristu amene ali chithunzithunzi cha Mulungu, chisawawalire (2Akolinto 4:3-4).*

---

<sup>23</sup>Onaninso gawo II.C mu chaputala 12.

Kodi Satana angapangitse bwanji khungu malingaliro a miyandamiyanda ya anthu pa dziko lonse lapansi? Ndizachidziwikire kuti sangakwaniritse kuchita izi yekha, popeza iye ali ndi malire a utumiki wake komanso siali wamphamvuyonse. Iye amadalira maulamuliro apamwamba a makono omwe anakhazikitsidwa kale komanso mizimu ya ulamuliro.

Satana amalamuliranso madera ndi mabungwe podzera mu zokhumba za thupi za anthu. Popanda Mulungu, anthu onse amakhala ndi chikhalidwe choyipitsitsa mu umunthu ndi mu uzimu momwe. Ziphuphu ndi moyo wa katangale zimakula pakati pao ndipo amakhala mu goli lalikuru la ukapolo wa m'dyerekezi. Ichi ndi chikonzero cha mizimu yonyasa ya m'madera ya Satana.

## **Momwe Tingagonjetsere Mizimu ya m'Madera**

Tiyenera kulimbana ndi kugonjetsa mizimu ya m'madera pogwiritsa ntchito mphamvu ndi ulamuliro wa dzina la Yesu Khristu. Titha kulimbana ndi kugonjetsaku mu njira zitatu zamphamvu izi:

1. kudzera mu nkondo ya pemphero,
2. kudzera mukumanga munthu wolimba,
3. kudzera mukufalitsa Uthenga Wabwino mu mphamvu ya Mzimu.

Ndipokhapo pamene tidzatha kufalitsa Uthenga Wabwino ngakhale kumadera amene sikunafikiridwe.

### **Nkhondo mu Pemphero**

Nkhondo ya mumapemphero imakhudza kulimbana ndi kugonjetsa mizimu yonyasa yamaulamuliro kupyolera mu dzina la Yesu. Kugwiritsa ntchito mphamvu ya Mzimu Woyera ndi yofunika zedi pankhondoyi ya uzimu kotero kuti titha kulamulira kuti ituruke mizimu yomwe yalowa mwa munthu. Mu njira yomweyi, tithanso kulamula mizimu ya m'madera kuti ichotse maukulu ake mu dera lomwe ili kulamulira.

Nkhondo yomenyedwa mu pemphero imakhudzanso kuyitana Mzimu Woyera kuti ubweretse chitsitsimitso m'deramo. Kupezeka kwa Mzimu Woyera kumakhala choletsa ku mphamvu za ziwanda (2 Atesalonika 2:7). Zotsatira za nkondo mu pemphero ndi “zitseko kutseguka” zomwe

zimatchulidwa kawirikawiri m'Malemba. (1 Akorinto 16:9; 2 Akorinto 2:12; Akolose 4:3; Chivumbulutso 3:8). Ndi chanzeru kupeza nthawi yomenya nk'hondo ya pempheroyi. Tiyenera tichite izi tisanalowe m'dziko, chigawo, mzinda, kapena mudzi kukalalikira Uthenga Wabwino.

### **Kumanga Munthu Wolimba,**

Njira yachiwiri yogonjetsera mizimu ya m'madera ndi kulanda mphamvu za “munthu wolimbayo.” Yesu analankhulapo zogwiritsa ntchito chidachi:

*Koma ngati Ine ndimatulutsa ziwanda ndi mphamvu yake ya Mzimu wa Mulungu, pomwepo ufumu wa Mulungu unafika pa inu. Kapena akhoza bwanji munthu kulowa m'banja la munthu wolimba, ndi kufunkha akatundu ake ngati iye sayamba kumanga munthu wolimbayo? Ndipo pamenepo adzafunkha za m'banja lake. (Mateyu 12:28-29)*

*Pamene paliponse mwini mphamvu alonda pabwalo pake zinthu zake ziri mumtendere; koma pamene pali ponse amdzera wakumposa mphamvu, nakamlaka, am'chotsera zida zake zonse zimene anazitama nagawa zofunkha zake. (Luka 11:21-22)*

Kodi “munthu wolimbayo” ndi ndani? Uyu ndi chiwanda champhamvu chomwe chimalamulira munthu, mabungwe kapena madera osiyanasiyana. Mu Luka 4:21 akufotokoza kuti chiwandachi chimakhala ndi zida zonse. Nyumba ya munthu wolimbayo itha kukhala thupi la munthu yemwe walowedwa ziwada. Ithanso kukhalo dera lomwe likulamuliridwa ndi mizimu yonyasa. Ithanso kukhala chigawo chomwe ziwandazo zikulamulira. “Katundu” (Mateyu 12:29) wake ndi miyoyo ya anthu omwe ali mu ukapolo wake.

Tikuphunzirapo maphunziro awiri ofunikira mu ndime ziwiri za m'Malemba izi.

1. Mizimu ya m'madera imatulutsidwa kapena kuthamangitsidwa mwa Mzimu wa Mulungu (onani Mateyu 12:27). Mu Luka 11:22, Yesu anafotokoza za Mzimu wa Mulungu monga “wina wake wolimba zedi” kuposa chiwanda cholimba kwambiri. Tingathe kugonjetsa ziwanda zolimbazi kupyolera mu mphamvu ya Mzimu Woyera *basi*.

2. Timalanda mphamvu za munthu wolimbayu pa kulowa m'nyumba mwake ndi “kumumanga” (Mateyo 12:29). Kodi izi zikukhudza chiyani? Ndizofunika kuti ife tilowe mu dera la chiwandacho ndi kuchimanga mu dzina la Yesu. Titha kuchilamula kuti chisamutse mphamvu zake pa anthu omwe chawasunga mu ukapolo. Titha kumanga mphamvu za chiwandacho mu dzina la Yesu kudzera mu mphamvu yopambana ndi kudzoza kwa Mzimu Woyera.

### **Kufalitsa Uthenga Wabwino**

Njira yachitatu yogonjetsera mizimu ya m'madera ndi kulalikira Uthenga Wabwino mu mphamvu ya Mzimu. Mu chaputala 4 taphunzira kuti Uthenga wa Khristu uli ndi mphamvu yayikulu ya Mzimu. Ndi zoonadi kuti ndi “mphamvu ya Mulungu yakupulumutsa munthu ali yense wakukhulupilira” (Aroma 1:16b). Kuwala kwa Uthenga Wabwino kumanyezimira pomwe uthengawo ukulalikidwa. Kugwiritsa kwa mizimu ya m'madera kumafooketsedwa pomwe anthu akumva ndi kukhulupirira Uthenga Wabwino. M'dima umachoka ndipo anthu amamasuka.

### **Zitsogozo Zofunikira Zisanu ndi Chimodzi**

Timaliza chaputala ichi popereka zitsogozo zowonjezera zisanu ndi chimodzi zofunikira mu nkondo ya uzimu yolimbana ndi mizimu ya m'madera.

1. *Khalani pa ubale wabwino ndi Mulungu.* Munthu wopusa yekha ndi amene angamayesere kumenyana ndi mizimu ya kumidima opanda iye mwini kumudziwa Mulungu. Anyamata asanu ndi awiri a Skeva anazindikira za choonadi ichi mowawa monga momwe m'Machitidwe a Atumwi 19:14-17 akulongosolera. M'silikali wa uzimu poyamba ayenera kudziwa kuti iye ndi wobadwanso mwatsopano zenizeni. Ayenera kukhala ndi moyo wokonda kupemphera komanso kukhala pa ubale wangwiro ndi Mulungu. Ayeneranso kuzindikira kudalira kwake kwathunthu mwa Mulungu.

2. *Lapani ndi kusiya machimo onse odziwika.* M'silikali wa Mulungu sayenera kumenya nkondo ali ndi tchimo lomwe sanalivomereze ndi kulilapa m'moyo wake. Yesaya 59:1-2 anati:

*Taonani, mkono wa Yehova sufupika, kuti sungathe kupulumutsa; khutu lake siliri logontha, kuti silingamve; koma zoipa zanu zakulekanitsani inu*

*ndi Mulungu wanu, ndipo machimo anu abisa nkhope yake kwa inu, kuti Iye sakumva.*

Tchimo lililonse lobwerezedwa bwerezedwa, kapenanso ntchito ya thupi ndi machitidwe a tchimo. Machitidwe ogonjetsedwa oterewa ndi zitseko zotsegukira kukuvulazidwa ndi ziwanda (Agalatia 5:19-21). Izi tiyenera kuziyang'anitsitsa ndi kuthana nazo. M'silikali wa Mulungu ayenera amasulidwe iye mwina asanayambe kumenya nkondo ya uzimu.

3. *Valani zida zonse za Mulungu.* Mu Aefeso 6:11, tikulimbikitsidwa kuti “tavalani zida zonse za Mulungu.” Palibe msilikali amene angapite ku nkondo opanda zida zoyenerera. M'silikali wa uzimu sayenera kumenya nkondo ya uzimu asanavale zida zonse za Mulungu zomwe zafotokozedwa mu Aefeso 6:1-18.

4. *Dzadzidwani ndi Mzimu Woyera.* M'silikali wa uzimu amagonjetsa ziwanda kupyolera mu Mzimu wa Mulungu (Luka 11:20). Choncho, poyamba ayenera abatizidwe ndi Mzimu Woyera. Kenako, mosalekeza m'silikaliyu ayenera kumayenda pamaso komanso mu mphamvu ya Mzimu.

5. *Pitirizani kupemphera mpaka chigonjetso chitafika.* Munkhondo iliyonse, chigonjetso kwenikweni sichimabwera pakungomenya kamodzi kokha. Monga Danieli, asilikali a Mulungu ayenera kupitiriza kupemphera mpaka chigonjetso chitafika (Danieli 10:2,12).

6. *Phatikizani pemphero ndi ulaliki wodzozedwa wa Uthenga Wabwino.* M'silikali wolimbikitsidwa ndi Mulungu adzalalikira ndipo zizindikiro ndi zozizwa zidzamsatira. Chipulumutso ndi chigonjetso m'dera lolamuliridwa ndi ziwanda ndichotheka ngati pemphero ndi ulaliki wodzozedwa ziphatikizidwa. Palibe chiwanda chomwe chingagonjetse zionetsero za mphamvu ya Mulungu.

## **Chimangiliro**

Satana amalimbikitsa mizimu ya m'madera kuti izilamulira zigawo, magulu a anthu ndi mabungwe. Mizimuyi imatsutsana ndi kufalitsa Uthenga Wabwino m'maderawa. Zolinga zake ndi kusunga anthu mu ukapolo.

Chipangano Chatsopano chimagwiritsa ntchito maina osiyanasiyana polongosola za mizimu yoyipayi:

- olamulira
- maulamuliro
- mphamvu
- maufumu
- mpando wachifumu
- atsogoleri, akalonga
- olamulira a dziko lapansi

Mizimu ya m'madera itha kugonjetsedwa kudzera mu mphamvu ya Mizimu Woyera. Izi zimachitika pomwe mpingo upanga zinthu zitatu izi:

- Nkhondo mu pemphero
- Kumanga munthu wolimba
- Kufalitsa Uthenga Wabwino.

Mtumiki wamphamvu ayenera kutsatira zinthu zisanu ndi chimodzi izi pomwe akumenya nkhondo ndi ziwanda za m'madera. Zitsogozozi ndi:

- Khalani pa ubale wabwino ndi Mulungu
- Lapani ndi kusiya machimo onse odziwika
- Valani zida zonse za Mulungu
- Dzadzidwani ndi Mizimu Woyera
- Pitirizani kupemphera mpaka chigonjetso chitafika
- Phatikizani pemphero ndi ulaliki wodzozedwa wa Uthenga Wabwino.



## Chaputala 14

# Kupemphera Ndi Okhulupilira Kuti Alandire Mzimu Woyera

## Chiyambi

Mu chaputala 6, tinakambirana za kufunikira kwa ubatizo wa Mzimu Woyera mu utumiki wa mphamvu. Ubatizowu umayenera kuchitika tisanayambe utumiki wa mphamvu. Mu chaputala chino tikambirana momwe tingatsogolere anthu ena ku gawo ili lofunika kwambiri mu Chikristu. Tikambilana izi pakuwonetsera chitsanzo chenicheni cha momwe tingatumikilire. Ndagwiritsapo ntchito chitsanzo cha utumiki ichi ku America komanso ku Africa. Ndipo ndaona anthu mazanamazana akudzadzidwa ndi Mzimu Woyera.

Ena afunsapo mafunso ngati ndi koyenera kuphunzitsa anthu momwe angadzadzidwire ndi Mzimu Woyera. Iwowa amati ubatizowu ndi ntchito ya Mulungu yekha basi. A Stanley Horton (1983) analemba za nkhani yofunikayi:

Kodi munganene kuti ndi kulakwa kuwapatsa anthu malangizo akufikira kwa Khristu Wobatiza kuti awonetsere chikhulupiriro chao kwa Khristuyo? Akhristu ambiri amati sizolakwika kupereka malangizo kwa anthu ofuna kupulumutsidwa. Tsono tilekeranji kuthandiza iwo akufa kulandira ubatizo? (Masamba 241-242).

Kuphunzitsa ndi kulalikira pa nkhani iyi kawirikawiri ndi zofunika zedi. Anthu amadzadzidwa ndi Mzimu Woyera monga zotsatira zake.

## Mafunso Oyambilira

Mu chigawo ichi, tikambirana zopempherera munthu kuti adzadzidwe ndi Mzimu Woyera. Komabe poyamba, tiyenera tiyankhe mafunso atatu ofunika awa:

- Ndani angadzadzidwe ndi Mzimu Woyera?
- Ndani angapempherere anthu ena kuti adzadzidwe ndi Mzimu Woyera?
- Kodi chimafunika ndi chiyani pa kulandira Mzimu Woyera?

### **Ndani Angadzadzidwe ndi Mzimu Woyera?**

Aliyense amene ali wobadwa mwatsopano mwachoonadi atha ndipo ayenera kudzadzidwa ndi Mzimu Woyera. Mphatso yodabwitsayi siyongosungilidwira anthu okhawo omwe ali okhwima mu uzimu. Kapenanso kuti ndi ya anthu okhawo a mpingo wina wake wapaderadera. Ndi lonjezo la kwa Akhristu *onse* a mibado *yonse*.

### **Ndani Angapempherere Anthu Ena Kuti Adzadzidwe ndi Mzimu Woyera?**

Okhulupirira aliyense amene ndi wodzadzidwa ndi Mzimu Woyera atha kutsogolera wokhulupirira mzake kuti alandire ubatizo wa Mzimu Woyera. Chofunika kwambiri ndi kukhumba mwa choonadi kuona ena akudzadzidwa ndi kugwiritsidwa ntchito ndi Mulungu.

### **Kodi Chimafunika ndi Chiyani pa Kulandira Mzimu Woyera?**

Machitidwe anayi auzimu amafunikira kuti munthu adzadzidwe ndi Mzimu Woyera. Awa ndi kukhumba, chikhulupiriro. matamando ndi kudzipereka kwathunthu kwa Mulungu.

1. *Kukhumba*. Poyambilira, tinakambirana za kufunikira kwa kukhumba mukulandira ubatizo wa Mzimu Woyera.<sup>24</sup> Baibulo limatsindika za kufunika kwa kukhumba mukulandira madalitso ochokera kwa Mulungu. Nthawi yina Yesu amaphunzitsa za momwe munthu angadzadzidwire ndi Mzimu Woyera. Iye anati, “*funani* (kunena kuti osalekeza kufunafuna) *ndipo mudzapeza* (*Luka 11:9*). Kufunafuna mwakhama (mosalekeza) ndi chipatso cha kukhumba.

---

<sup>24</sup>Chaputala 6.

Mulungu anatiuza “*Ndipo mudzandifuna Ine ndi kundipeza pamene mundifuna ndi mtima wanu wonse (Yeremiya 29:13).* **Ofunawo** ayenera kukhumba ndi mtima wao onse kuti adzadzidwe ndi Mzimu Woyera. Owatsogolera anthuwa m’pempheho ayenera kulimbikitsa kukhumba.

2. *Chikhulupiriro*. Chikhulupiriro ndi maziko wolandirira m’dalitso uliwonse wochoka kwa Mulungu. Limodzi mwa madalitsowa ndi ubatizo wa Mzimu Woyera! Paulo anawakumbutsa a Galatiya kuti analandira Mzimu Woyera “*ndi kumva kwa chikhulupiriro*” (*Agalatiya 3:2b*). Iwo sanamulandire Yesu pakungosunga lamulo. Yesu anaphunzitsanso kuti timalandira kuchokera kwa Mulungu pakukhulupirira. “*Chifukwa chake ndinena ndi inu, zinthu zirizonse mukazipemphera ndi kuzipempha, khulupirirani kuti mwazilandira ndipo mudzakhala nazo. (Marko 11:24).* Izi zikuphatikiziraponso kulandira Mzimu Woyera. Munthu ayenera kukhulupirira kuti walandira Mzimu Woyera ndipo kuti udzakhala wake. Iwo otumikira wofunafunawo ayenera kulimbikitsa chikhulupiriro m’mitima mwao. Tikambirana zambiri za nkhanayi kutsogoloku.

3. *Matamando*. M’Buku la Machitidwe a Atumwi mwalembedwa nkhanu zambiri zokhudza nthawi zosiyanasiyana momwe anthu anadzadzidwa ndi Mzimu Woyera. Mu nyengo iliyonse timaona anthu akutamanda Mulungu momasuka ndi mosangalala. Tsiku la Pentekoste lisanafike ophunzira “*anakhala chikhalire m’kachisi, nalikuyamika Mulungu*” (Luka 24:53). Baibulo limatiphunzitsa kuti Mulungu amakhala mu “*mapembedzero a anthu ake*” (Masalmo 22:3). Mulungu amazionetsera kupezeka kwake pakati pathu pomwe tikumpembedza (2 Mbiri 7:1-3, Machitidwe a Atumwi 4:31). Atumiki omwe akufunitsitsa kuthandiza ena kuti alandire Mzimu Woyera ayenera kumalimbikitsa matamando kwa Mulungu mokondwera. Ndipo wofunafunayo ayenera azitamanda Mulungu ndichikhulupiriro, kukhulupirira kuti Mulunguyo awadzadza ndi Mzimu wake.

4. *Kudzipereka kwathunthu kwa Mulungu*. Kugonjera kwa Mulungu ndi maziko olandilira Mzimu Woyera. Ofunawo kudzadzidwa ayenera kulimbikitsidwa kuti adzipereke okha kwathunthu kwa Mulungu – mu mzimu, m’magano ndi m’thupi (Aroma 6:13; 12:1). Mzimu Woyera udzatsogolera magano ndi mau a munthuyo. Mzimu Woyera mwini udzayamba kulankhula zotamanda Mulungu kudzera mwa munthuyo. Izi ndi zomwe Baibulo limazitchula kuti “*kulankhula malilime ena.*”

## **Kupemphera ndi Okhulupirira Kuti Alandire Mzimu Woyera**

Machaputala oyambilira okamba za kuchiritsa odwala ndi kutulutsa ziwanda<sup>25</sup> anationetsa chitsanzo cha utumiki chokhala ndi magawo atatu: kufunsa mafunso achidziwitso, nthawi ya kupemphera ndi uphungu wachitsogozo atangotha mapempherero.

### **Kufunsa mafunso achidziwitso**

Munthawi ya kufunsa mafunso achidziwitso m'busa amakhala ndi zolinga zitatu. Mtumikiyu amafuna:

- kutsimikizira ndi kulimbikitsa chikhulupiriro cha munthuyo,
- kuzindikira za moyo wa uzimu wa munthuyo ndi njala yake yofuna Mulungu,
- kulangiza wofunayo zimene angachite kuti adzadzidwe ndi Mzimu Woyera.

*1. Kutsimikizira ndi kulimbikitsa chikhulupiriro.* Tiyenera kutsimikizira ofunayo ndi kuyesetsa kulimbikitsa chikhulupiriro chake. Poyamba munthuyo atha kukhala ndi mantha. Inu mutha kumuza kuti, “ndasangalala kwambiri kuti mwabwera lero. Mwachita chinthu chabwino ndi cholondola. Lero litha kukhala limodzi mwa masiku osayiwalika pa moyo wanu. Mulungu ali ndi chinthu chapaderadera choti akuchitileni.” Mauwa atha kukhazika mtima wa munthuyo m'malo. Chilimbikitsochi chingakonze mtima wake kuti alandire Mzimu Woyera.

*2. Kuzindikira za moyo wa uzimu wa munthuyo ndi njala yake yofuna Mulungu.* Ndikofunika kuzindikira ngati munthuyo ali wa uzimudi. Mutha kukwaniritsa cholinga ichi pogwiritsa ntchito mafunso awa:

- Kodi mukufuna kuti Mulungu akuchitireni chiyani lero? Kodi mwabwera kuti mudzadzidwe ndi Mzimu Woyera? Musangoganizira

---

<sup>25</sup>Chaputala 11 ndi 12.

kuti mwina munthuyo wabwera kuzadzadzidwa ndi Mzimu Woyera. Mwina atha kufuna pemphero pa zifukwa zina. Ngati akufuna ubatizo, ndibwino kuti munthuyo afotokoze yekha. Pakungonena chabe cholinga chake zidzalimbikitsa chifuniro komanso chikhumbokhumbo chake kuti adzadzidwe.

- Kodi munadzadzidwapo ndi Mzimu kale? Ndikutheka kuti munthuyo anadzadzidwapo kale ndi Mzimu Woyera. Ngati ndi choncho munthuyo sangafunenso china koma chilimbikitso kuti adzadzidwensho. Ngati sanadzadzidwepo, adzasoweka malangizo ochuluka.
- Kodi munaonapo munthu wina aliyense wodzadzidwa ndi Mzimu Woyera? Ndikutheka kuti munthuyo anakumanapo ndi anthu ena omwe anadzadzidwa ndi Mzimu Woyera. Ngati ndi choncho munthuyo amakhala akudziwa za zomwe zimuchitikire. Ngati sichoncho, munthuyo adzasoweke chiphunzitso chozama.

Mvetserani mwatcheru kumayankho a munthuyo. Mayankho a munthuyo adzakuthandizani kudziwa nthawi komanso momwe mungapitire ku gawo lina.

### 3. *Kulangiza munthu wofuna zimene angachite kuti adzadzidwe.*

Malangizo athu ayenera kukhala ndi zolinga zitatu:

- kutakasa chikhulupiriro cha ofuna kudzadzidwa,
- kumuthandiza munthuyo kumvetsa zomwe ayenera kuchita,
- kumuthandiza iye kumvetsa zomwe zimuchitikire.

Njira imodzi yotakasira chikhulupiriro ndi kubwereza malonjezo a Mulungu okhudza Mzimu Woyera. Kumudziwitsa munthuyo kuti Mulungu wakonzeka tsopano kuti amudzadze ndi Mzimu Woyera. Kumukumbutsa munthuyo za lonjezo la Khristu: *“Pakuti yense wakupempha alandira”* (Luka 11: 10a). Wofuna kudzadzidwayo ayenera kukhulupirira kuti Mulungu amudzadza ndi Mzimu Woyera akamufunsa kuti atero. Ichi ndi chomwe chimatchedwa *“chikhulupiriro chakuyembekezera.”* Kenako, ayenera kuyembekezera kuti adzadzidwa. Muyenereza kulimbikitsa munthuyo kukhala ndi chiyembekezonchi.

Ntchito ina ndi kuthandiza ofuna kudzadzidwa kumvetsa zoti achite kuti adzadzidwe. Tiyeneranso timuuzze munthuyo zoti ayembekezere kuti zichitika.

Munthuyo ayeneranso kudziwa kuti kulandira Mzimu Woyera sichinthu chovuta kapena chachilendo kwa okhulupirira. Koma ndi chinthu chomwe Akhristu ayenera kulandira. Munthuyo ayenera kudziwa kuti sadzadzidwa ndi Mzimu Woyera “wina wachilendo.” M’ malo mwake, alandira mulingo wonse wa Mzimu Woyera umene uli kale mwa iye.

Mutha kumuuzza munthuyonso izi:

Kulandira Mzimu Woyera ndi kosavuta. Ndi chinthu cha monga mwachilengedwe. Kumbukirani zomwe Yesu anachitapo nthawi ina kwa ophunzira ake: “*ndipo pamene anati ichi nawapumira, nanena nawo, landirani Mzimu Woyera*” (Yohane 20:22). Kupuma ndi chinthu chachilengedwe kwa munthu aliynse. Momwemonso, kulandira Mzimu Woyera ndi chinthu chachilengedwe kwa mwana wa Mulungu.

Pomaliza, ofuna kudzadzidwa ayenera adziwe zomwe mwakonzekera kuchita ndi zomwe zimuchitikire iyeyo. Mutha kulankhula naye motere:

Poyamba, tipemphera limodzi. Kenako, ndikutsogolerani mu pemphero. Timufunsa Ambuye kuti atidzadze ndi Mzimu Woyera. Ambuye amva ndi kuyankha pemphero lathu. Ndikudziwa kuti atidzadza chifukwa tipemphera mwa chifuniro Chake (1 Yohane 5:14). Tikatha gawo ili, ndikufunsani kukhala ndi chikhulupiriro cha kulandira nacho Mzimu Woyera. Ndikutsogoleraninso mu pemphero lina lalifupi. Pempherolo liyenda motere: Ambuye, tsopano lino, mu dzina la Yesu Khristu, ndikulandira Mzimu Woyera. Kenako, ndikufunsani kuti muyambe kutamanda Mulungu ndi mtima wanu wonse. Pamene mukhala mukutero muyembekezere Mulungu kuti akudzadzani ndi Mzimu Woyera. Mumva kupezeka Kwake kukufika pa inu ndi kukudzadzani. Ndipo muyamba kulankhula chilankhulo chomwe simunachiphunzirepo. Musachite mantha aliwonse koma mungopitiriza kulankhulako. Mwakonzeka tsopano kudzadzidwa ndi Mzimu Woyera? Nanga muli ndi funso lililonse?

Ngati munthuyo ali ndi mafunso, mumuyankhe. Ngati alibe mafunso, yambani kupemphera naye.

### **Nthawi ya Kupemphera**

Mu nthawi ya kupemphera muyenera kuchita zinthu ziwiri izi: Poyamba, muyenera kumutsogolera munthuyo mu pemphero, kupempha Mzimu Woyera kuti umudzadze. Kachiwiri, mumutsogolere ku khwerero la chikhulupiriro lakulandilira Mzimu Woyera.

1. *Tsogolerani munthuyo mu pemphero.* Titsogolere munthuyo mupemphero pomupempha Mulungu kuti amudzadze ndi Mzimu Woyera. Izi ndi chimodzimodzi kutsogolera munthu wochimwa mu pemphero lakulapa. Pempheroli lingapempheredwe motere, munthuyo akubwereza kunena motsatira mau amene mukupempherawo:

Ambuye, ndabwera kwa Inu tsopano kuti ndidzadzidwe ndi Mzimu Woyera. Tsopano lino, palibenso china chomwe ndikuchifuna koposa pa moyo wanga. Munalonjeza kuti aliyense amene apempha adzalandira. Choncho, ndikupempha ndi chiyembekezo kuti ndilandira. Pomwe ndiyamba kukutamandani nditsegula chikhulupiriro changa chonse kwa Inu. Ndipo ndidzadzidwa ndi Mzimu Woyera komanso kulankhula ndi malilime ena monga chizindikiro chakudzadzidwaku. Sindiopa kalikonse.

Mutatha pemphero ili mutsimikizireni munthuyo kuti Mulungu wamva pemphero lake. Ndipo mutsimikizireni munthuyo kuti Mulungu wakonzeka kumudzadza ndi Mzimu Woyera.

2. *Kutsogolera ofuna kudzadzidwa mu chikhulupiriro.* Tsopano mufunse munthuyo kuti akweze manja ake m’mwamba ndi kupemphera nanu limodzi pemphero losavutali: “Ambuye, tsopano lino, mu dzina la Yesu, ndikulandira Mzimu Woyera.” Pempheroli limapangitsa munthuyo kukhazikitsa chikhulupiriro chake pakulandira Mzimu Woyera. Mulimbikitse munthuyo kuti alambire Mulungu ndi mtima wake wonse.

Kawirikawiri ofuna kudzadzidwayo amadzadzidwa ndi Mzimu Woyera nthawi yomweyo. Amayamba kulankhula ndi malilime ena ndi chithandizo cha Mzimu Woyera.

Komabe nthawi zina munthuyo sangayambe kulankhula malilime ena nthawi yomweyo. Mulimbikitsemi kuti apitirize kulambira Mulungu. Mwina mungafune kupemphera naye limodzi kuti Mulungu akudzadzeninso ndi Mzimu Woyera. Nthawi zambiri izi zimalimbikitsa munthuyo kuti apitirirebe kufunafuna mpaka atadzadzidwa.

Munthuyo angaoneke ngati kuti akulephera kulumikizana ndi Mulungu. Zikatero, ndinapeza kuti ndizothandiza kubwereza ndondomeko zomwe zaperekedwa koyambilira muchigawo chino. Pomwe mukupanga izi mutchuleponso momwe munthuyo angalumikizirana kwathunthu ndi Mzimu Woyera.

Munthuyo adzayamba kulankhula ndi malilime ena pamene adzadzidwa ndi Mzimu Woyera. Mulimbikitseni kupitiriza pamene ayamba kulankhula malilime ena. Khalani naye nthawi yonse yomwe akhala akupitiriza kupemphera mu m’Mzimu.

Mukumbutseni kuti ndikofunika kwa iyeyo kufunafuna *mphatso* za Mzimu Woyera. Komanso ndikofunika kwambiri kuti azifunatuna *Mpereki* wa Mzimuyo. Ichi ndi chiphunzitso chothandiza kwa munthuyo. Iyeyo ayenera kuyika maso ake pa Yesu osati pakalakhula malilime. Munthuyo sayenera kuyiwala Mulungu wa chisomo wopereka *mphatso* zonsezi.

### **Uphungu Wachitsogozo Atangotha Mapemphero**

Munthuyo adzapindula ndi malangizo omwe tingampatse titatha kupemphera naye. Ngati wadzadzidwa ndi Mzimu, mudzampatsa malangizo a mtundu umodzi. Ngati sanadzadzidwe mudzampatsa malangizo a mtundu winanso.

*1. Ngati wadzadzidwa ndi Mzimu.* Munthuyo adzakhala wokhutitsidwa kotheratu, wodzadzidwa ndi Mzimu Woyera, ndi wolankhula m’malilime ena. Malangizo awa adzamuthandiza:

Awa simathero; ndi chiyambi chabe. Tsopano Mulungu ayamba kukugwiritsani ntchito mu njira yatsopano ndi yamphamvu. Timalandira Mzimu Woyera kuti tilandire mphamvu za umoyo ndi ntchito Yake. Muyembekezere kukhala ndi mphamvu zatsopano m’moyo wanu. Mukachoka pano muyenera kukauza wina wake zokhudza Yesu. Muyeneranso kupeza nthawi tsiku lililonse yopemphera mwa Mzimu Woyera — kupemphera m’malilime. Izi zidzakupatsani mphamvu ndi kukukumbutsani za kupezeka kwa Mzimu Woyera m’moyo wanu.

2. *Ngati sanadzadzidwe ndi Mzimu Woyera*. Uzani munthuyo kuti asakhumudwitsike. Mutsimikizireni kuti lonjezo la Yesu likanali loonadi. “*Pakuti yense wakupempha alandira*” (Lk.11:10a). Muuzeni kuti:

- apitirize kupempha ndipo alandira,
- apitirize kufunafuna ndipo apeza,
- apitirize kugogoda ndipo zitseko zimtsekukila iye.

Mfunseni ngati akufuna kupempheranso. Ngati akufuna, bwerezaninso ndondomeko zaperekedwa kale zija. Ndipo munthuyo alimbikitsidwe kwambiri kuti achite zonse mwa chikhulupiriro.

## **Mfundo Zofunika**

Timaliza chaputalachi pokambirana mwachidule mfundo zitatu zofunika. Mfundozi zimapereka malangizo abwino kwa iwo omwe akufuna kutsogolera anzawo mu ubatizo wa Mzimu Woyera.

### **Mvetsani Phunziroli**

Poyamba, phunzirani china chilichonse chokhudza ubatizo wa Mzimu. Muyenera kudziwa zomwe Baibulo limaphunzitsa zokhudza nkhanayi. Kuchita izi ndiyo nzeru yoyenera. Muyenera kuphunzira za Mzimu Woyera ndi momwe umagwirira ntchito m'miyoyo ya anthu. Pomwe mukuonjezera chidziwitso chanu ndi pomwe mudzathenso kuthandiza ena kuzindikira ndi kulandira m'madalitso wa Mulungu. Mwapadera, muyenera kusanthula Mau a Mulungu, makamaka buku la Machitidwe a Atumwi, pa mutuwu. Muthanso kuwerenga mabuku ena abwino pa za ubatizo wa Mzimu Woyera.

### **Musakhale a Ulesi**

Kachiwiri, simuyenera kulola *ulesi* mu uzimu kukulepheretsani. Kupemphera ndi anthu kuti adzadzidwe ndi Mzimu Woyera ndi ntchito yolemetsa. Abusa ena amazemba kulalikira pa mutu umenewu komanso amazemba kutsogolera anthu kumdalitso wopambanawu. Amachita izi chifukwa cha ulesi. Kodi izi zili choncho ndi inu? Ngati ndichoncho, lapani za ulesi wanu mu uzimu. Dziperekeni nokha ku utumiki wofunikawu ndi mtima wanu wonse.

### **Onetsani Chifundo Ndi Chidwi**

Pomaliza, onetsani chidwi ndi luntha lanu pomwe mukutumikira anthu ena. Muyenera kukhala a luntha, ofunitsitsa ndi a chidwi pamene mukupemphera ndi anthuwa. Nthawi yomweyonso, muyenera kupewa kukhala a chidwi kwambiri. Chifundo chanu pa munthuyo chizionekera poyera. Chifundo chanu ndi chofunika kwambiri koposa chidwi komanso luntha lanu. Apa luntha ndi nzeru ndi zofunika.. Izi zidzakusonyezani muyeso oyenera wa chidwi ndi chifundo pomwe mukulimbikitsa ofuna kudzadzidwa.

## **Chimangiliro**

Muchaputala chino, takambirana za momwe tingatsogolere anthu kuti alandire ubatizo wa Mzimu Woyera. Takambirananso za zinthu zofunika kuti munthu alandire Mzimu Woyera. Komanso tinatchula ndondomeko za utumiki zitatu zomwe zingalimbikitse ofuna kudzadzidwa kuti adzadzidwa.

- Kufunsa mafunso achidziwitso

- Nthawi ya kupemphera
- Uphungu wachitsogozo atangotha mapemphero

Tsopano dziperekani nokha ku utumiki uwu. Kuthandiza anthu kudziwa ndi kulandira madalitso a Mulungu ndi chinthu chonyaditsa kwambiri mu utumiki wa Chikhristu.



## Chaputala 15

# Utumiki wa Mphamvu mu Misonkhano ya Usodzi

## Chiyambi

Machaputala anayi a mu chigawo chino analunjika pa utumiki wa ubusa kwenikweni. Tsopano tikambirana za utumiki wa mphamvu mu **misonkhano ya usodzi**. Nthawi zambiri m’busa amapemphera ndi munthu m’modzi m’modzi pa nthawi. Mosiyaniranapo, mu misonkhano ya usodzi, nthawi zambiri mapemphero amachitika mwachigulu. Izi zikutanthauza kuti mtumiki amapemphera ndi anthu ochuluka pa nthawi imodzi.

Mfundo zomwe takambirana mu chaputala 8 zokhudzana ndi m’busa ziri chimodzimidzinso ndi kwa mlaliki wa m’misonkhano ya usodzi. Monga m’busa, mlaliki asamakakamize kapena kulenga zotsatira za mapemphero ake ndi anthu. Komanso monga m’busa, mlaliki amafuna anthu kuti amve chikondi cha Mulungu pamene iye akutumikira. Choncho, sayenera kuopyeza anthuwo, kapena kuwanyoza chifukwa chakusowa kwao kwa chikhulupiliro.

Mlaliki wa usodzi amakhudzikanso kwenikweni ndi uzimu wa anthu omwe ali mu msonkhano wake. Kunenanso mwatchutchutchu, iye akupangitsa msonkhanowo chifukwa cha anthuwo. Akufuna kutsogolera iwo kukudziwa Yesu monga Mbuye ndi Mpulmutsi wa miyoyo yao. Choncho, mlaliki amayenera kukhumba kuti anthuwo aone mphamvu ya Mulungu. Koma sayenera kukhala okhudzika kwambiri ndi zionetsero za mphamvu ya Mulungu mpaka kuyiwala kuti ndi chifukwa chiyani ali pamalopo.

Njira zambiri zomwe takambirana mu chigawo chino (chaputala 11 mpaka 14) zikhoza kugwiritsidwa ntchito ndi mlaliki wa usodzi popanda kukaika

kulikonse. Komabe, chaputala chino chikuonetsera zinthu ziwiri zofunikira zedi ku utumiki wa mphamvu mu usodzi. Mfundo zake ndi izi:

- kufunikira kwa zizindikiro ndi zodabwitsa mu misonkhano ya usodzi
- mmene tingatumikilire mu utumiki wa mphamvu mu misonkhano ya usodzi.

## **Kufunikira kwa Zizindikiro ndi Zodabwitsa mu Msonkhano wa Usodzi**

### **Chitsanzo cha m’Chipangano Chatsopano**

Utumiki wa Yesu ndi wa atumwi uyenera kukhala chitsanzo chatu cha utumiki lero lino. Yesu anauza ophunzira ake, “*Tiyeni pambuyo panga, ndidzakusandutsani asodzi a anthu*” (Mateyu 4:19). Ili linali lonjezo la Khristu kuti adzaphunzitsa ophunzira ake kuchita ntchito ya utumiki. Yesu mwini adzakhala chitsanzo chao. Iwo adzaphunzira pakutsanza Yesu muzochita.

Yesu analonjezanso omutsatira ake kuti adzalandira mphamvu za utumiki. Mphamvu izi zimabwera kudzera mu kudzadzidwa ndi Mzimu Woyera (Machitidwe a Atumwi 1:8). Kupyolera apo, Yesu analonjeza kuti ophunzira ake adzachita ntchito zodabwitsa chimodzimidzi monga Iye anachitira.

*Indetu, indetu, ndinena kwa inu, Wokhulupirira ine, ntchito zimene ndichita Ine adzazichitanso iyeyu; ndipo adzachita zoposa izi. Chifukwa ndipita ine kwa Atate. (Yoh.14:12)*

Ophunzira analandira lonjezo la Khristu kuti iwo adzatumikira monga momwe Iye anachitira. Pakusanthula Mpingo Woyamba uja mu buku la Machitidwe a Atumwi kumaonetsa kuti izi zinachitikadi. Omutsatira Yesu, makamaka atumwi, anatomikira munjira yomweyo monga mmene Yesu anatomikilira. Mautumiki awo anabeleka zizindikiro ndi zodabwitsa zofanana. Ifenso, talonjezedwa mphamvu ngati yomweyo imene Yesu ndi atsogoleri a Mpingo Woyamba anali nayo (Machitidwe a Atumwi 1:8; 2:38-39).

Monga atumiki a Pentekoste, tiyenera kutsanza utumiki wa Yesu ndi wa atumwi. Choonadi ichi chikuutsa mafunso awiri ofunikira: Loyamba, kodi

Yesu ndi atumwi anachititsapo misonkhano ya gulu ya usodzi? Lachiwiri, kodi zizindikiro ndi zodabwitsa zinalipodi pamene amatumikira kugulu la anthu? Mayankho a mafunso onse awiriwa ndi “Inde.” Onetsetsani zochitika izi m’mautumiki ao.

1. *Utumiki ku gulu lalikuru.* Yesu ndi ophunzira nthawi zambiri anatumikira ku chikhamu cha anthu osonkhana pamodzi. Mu Baibulo mau akuti *khamu* kapena *gulu* akupezekamo nthawi zochulukirapo, pafupifupi makuni asanu ndi atatu kudza mphambu zitatu mu mabuku a Uthenga Wabwino ndi makumi awiri mu bukhu la Machitidwe a Atumwi lokha. Ndipo mau akuti *anthu ochuluka* akupezekamo kakhumi ndi kanayi pa kuphatikiza mabuku onse. Mau awa, nthawi zambiri akukambidwa pamene akunena za anthu amene anali kulandira utumiki wa pantetete. Kotero, tikuona kuti Yesu ndi ophunzira amakhalanso kawirikawiri ndi mautumiki a kugulu la anthu. Mlaliki amatsatira mapazi a Yesu ndi a atumwi pamene atumikira mu misonkhano ya usodzi.

2. *Kuchitika zozizwa.* Yesu ndi ophunzira anachitapo zozizwa pamaso pa chikhamu cha anthu. Yesu anachita zizindikiro zake moonekera ku gulu. Atumwinso nao anachita zozizwa ku gulu la anthu moonekera. Paulo akuchitira umboni kwa Agripa pokhudzana ndi utumiki wa Yesu ndi wa atumwi. Iye anakumbutsa mfumu kuti chilichonse cha utumiki wao “*sichinachitika m’nsere* (Machitidwe a Atumwi 26:26). Koma, utumiki wao unachitika pamaso pa anthu ochuluka.

Mau amene amagwiritsidwa ntchito kawirikawiri a zozizwa zimene anachita ndi *zizindikiro* ndi *zozizwa*.<sup>26</sup> Zizindikiro ndi zozizwa zimene zimaloza ndi kutsimikizira uthenga wa Uthenga Wabwino wachipulumutso. Zodabwitsa ndi zozizwa zimatsekula mitima ya anthu kuti akhulupilire Uthenga Wabwino.

3. *Kulalikidwa kwa Uthenga Wabwino.* Yesu ndi atumwi sanachite zozizwa mwakungowonetsera mphamvu chabe. Zozizwa zao zinachitika mukulozera ku choonadi cha Uthenga Wabwino. Nthawi zonse analalikira Uthenga Wabwino pamene zozizwa zimachitika. Mlaliki wa usodzi sayenera kuyiwala kuti cholinga choyamba cha misonkhano ya usodzi ndi kulalikira Uthenga Wabwino wa chipulumutso. Khristu ayenera kulalikidwa. Zozizwa

---

<sup>26</sup>Mauwa atha kupezeka mu ndime izi: Yohane 20:30; Machitidwe a Atumwi 2:22, 43; 3:10; 4:30; 5:12; 6:8; 7:36; 8:6, 13; 14:3; Aroma 15:13, 19; 2 Akorinto 12:12; Ahebri 2:3,4).

ziyenera, mopanda kukayikira, kuloza ndi kuonetsera Khristu. Komabe, kulalikidwa komveka bwino kokha kwa Uthenga Wabwino kungadziwitse anthu mmene angapulumsidwire. Kulalikirira kokha kungaonetsere kupezeka kwa mphamvu ya Mulungu. Anthu amamva mphamvu ya Mulungu kuchokera m' mau a mlaliki pamene iye adzodzedwa ndi Mzimu Woyera.

### **Mmene Zizindikiro ndi Zodabwitsa Zimapindulira Misonkhano ya Usodzi**

Zizindikiro ndi zodabwitsa zikhonza kupindulitsa msonkhano wa usodzi mu njira zinayi zofunikira. Zimakopa anthu, zimalongosolera khalidwe la Mulungu, zimaonetsera mphamvu za Khristu ndi kukonzetsera anthu kukukhulupilira.

1. *Kukopa anthu.* Chozizwa chimakopa anthu ku msonkhano wa usodzi ndi ku Uthenga Wabwino umene ulikulalikidwa pamalopo. Izi zinachitikapo pamene munthu wina anachiritsidwa pakhomo la kachisi lotchedwa “Lokongola:” *“Anawathamangira pamodzi anthu onse ku khumbi ... alikudabwa ndithu” (Machitidwe a Atumwi 3:11).* Petro anagwiritsa ntchito chozizwa ichi ngati mwayi wakulalikira Uthenga Wabwino (3:12-26). Anthu ochulukana zedi anapulumsidwa monga zotsatira zake patsikulo (4:4).

Nthawi zina chozizwa chochitika mu malo a chinsinsi chikhonza kukhala ndi chikoka chachikulu pa anthu mu msonkhano wa usodzi. Izi ndi zomwe zinachitika ndi Petro pamene anachiritsa Eneya ndi kuukitsa kwa akufa Dorika (Machitidwe a Atumwi 9:32-43). Anthu awa onse analandira chozizwa chao mu malo opanda anthu ambiri. Koma zozizwa zonse izi zinapangitsa anthu ambiri kubwera kwa Yesu moonekera. Nthawi zina, mlaliki atha kuitanidwa ku nyumba ya munthu m' modzi kukapempherera wodwala. Ngati nkotheke iye ayenera kupitako. Chozizwa chimene chingachitikire pakhomo chikhonza kutsekula zitseko za kholola lalikuru mu nthawi ya msonkhano wa usodzi.

2. *Kulongosolera khalidwe la Mulungu ndi chifundo Chake.* Kuona munthu wodwala kapena wolumala atachiritsidwa kapenanso munthu wodwala ziwanda atamasulidwa zimakhala ndi mphamvu kwambiri pa anthu. Kupyolera mu zozizwa zoterezi, omvera amaona chifundo chachikuru cha Mulungu. Amatha kuona kuti Mulungu amasalira kupwetekedwa kwao ndi ululu umene amakhala nao. Izi zimawapangitsa kufunitsitsa kutsatira Mulungu amene adzawathandiza mu nthawi yakusowa. Mlaliki angakhale wanzeru pakuloza mbali imene chozizwa cha machiritso chachitika mu msonkhano.

*3. Kuonetsera mphamvu ya Khristu pakugonjetsa milungu yonyenga.*

Munthu atha kumasulidwa kuchokera ku themberero mu nthawi ya msonkhano wa usodzi. Kumasulidwa kotereku kumaonetsa kuti Mulungu ndi wamphamvu kuposa milungu yonyenga kapena mizimu yamakolo. Anthu tsono atha kuona kuti Chikhristu chenicheni chili champhamvu kuposa milungu yao yonyenga.

*4. Kukonzetsera omvera kukukhulupilira.* Anthu amene amatha kuona Mulungu akuchita zodabwitsa mu msonkhano amakhala otsegukira ku Uthenga Wabwino. Kukwera kwa chikhulupiliro<sup>27</sup> chao kumachitika mu mitima yao. Amakhala okonzekera kuchitapo kanthu pamene apatsidwa mwayi wakulandira Yesu Khristu.

## **Mmene Tingatumikilire mu Mphamvu pa Nthawi ya Misonkhano ya Usodzi**

### **Kukonzekera m'Sonkhano wa Usodzi**

Zithu zingapo ziyenera kuchitika msonkhano wa usodzi usanayambe. Zitatuzi zikambidwa mu ndime ino. Izi ndi:

- kukonzekera mu dera la uzimu
- mapemphero akugwetsa malinga
- kuphunzitsa anthu othandizira ku gome.

*1. Kukonzekera mu dera la uzimu.* Mlaliki aliyense wa Pentekoste amakhala ndi chiyembekezo chakuona mphamvu ya Mulungu ikuchitachita mu nthawi ya msonkhano wa usodzi. Izi zingachitikedi ngati mlalikiyo akuyika chidwi chake pa moyo wake wa uzimu mu kukonzekera msonkhanowo. Ayenera kukhala ndi nthawi ya iye yekha yokwanira bwino yakupemphera ndi kusala kudya. Ayeneranso kupemphera ndi gulu lonse lokonza msonkhanowo. Kusala kudya ndi kupemphera kwa gulu lonse ndi kofunikira. Iyi iyenera kukhala nthawi yakudzipereka ndi kugonjera aliyense payekhapayekha ku chifuniro cha Mulungu.

---

<sup>27</sup>Takamba izi mu chaputala 4

2. *Mapemphero akugwetsa malinga.* Gulu la msonkhanowo liyeneranso kukhala pamodzi ndi kukhala ndi nthawi yakungomenya nkondo yakugwetsa malinga a mdyerekezi. Makamaka ayenera kupempherera kutsanulidwa kwa Mzimu Woyera mu msonkhanowo. Gululi liyenera kugonjetsa zimphamvu ndi maukulu onse a mdyerekezi ndi mizimu ya m'deralo. Ngati nkotheka, gululo liyenera kupita ku malo omwe msonkhanowo ukachitikire. Kumeneko, akhonza kupemphera ndi anthu osiyanasiyana mu nyumba zao. Ena mwa anthu a mugululo atha kuchita mapemphero akuyenda mumiseu ya muderalo. Atha kuchita izi ali awiri kapena atatu mu magulu osiyanasiyana. Mapemphero akuyendawa amathanso kupereka mwayi wakuchitira umboni nthawi ya msonkhano isanafike.

3. *Maphunziro kwa othandizira ku gome.* Anthu othandizira ku gome ndi anthu amene amapemphera ndi iwo amene amabwera kutsogolo kudzapemphererewa munthawi ya msonkhano. Iwo ayanera kuphunzitsidwa mmene angatsogolelere anthu kwa Khristu ndi mmene angaperekere upungu kwa otembenuka mtima. Othandizirawa ayeneranso kuphunzitsidwa utumiki wamphamvu. Bukhu ili litha kukhalanso chida chogwiritsira ntchito powaphunzitsa anthuwo.

### **Kutumikira mu m'Sonkhano wa Usodzi**

Mlaliki amafuna mphamvu ya Mulungu ipezeke mu msonkhano umene akutumikira. Choncho, ayenera kukhala okhudzika ndi zinthu zitatu izi:

- moyo wa uzimu pa malo a msonkhano
- kudzodza kwa Mzimu Woyera pa utumiki wake
- kumakhala ndi nthawi ya utumiki wa mphamvu.

1. *Malo.* Moyo wa uzimu pa malo amene ukuchitikira msonkhano wa usodzi uyenera kudziwika ndi zinthu ziwiri izi: chikhulupiliro ndi chionetsero cha kupezeke kwa Mulungu. Malo oterewa atha kupangidwa ndi mapemphero ndi kulambira. Mau amenenso atha kulankhulidwa ndi otsogolera mapemphero ndi ofunikira. Mau awo ayenera kuonetsa chikhulupiliro pa kuthandizira kupanga malowo kukhala ndi chikhulupiliro chokhala ndi chiyembekezo.

2. *Kudzodza.* Iwo amene ali pamalopo ayenera kuona kudzodza kwa Mzimu pakati pa atumiki. Chiyero, pemphero ndi kugonjera kwa Mzimu ndi

zifungulo za chigonjetso cha uzimu mu msonkhano wa usodzi. Izi zimathandizira kusunga kud zodza kwa utumiki pakati pa atumikiwo.

3. *Nthawi ya utumiki wa mphamvu.* Mu msonkhano wa usodzi uliwonse, mlaliki ayenera kupereka nthawi ya utumiki wa mphamvu. Nthawi iyi payenera pakhale kumasula kwa mphatso za Mzimu komanso kupempherera odwala ndi kuturutsa ziwanda ngati nkofunikira. Komanso mkati mwa izi, mlaliki ayenere kulolo Mzimu Woyera kuchita zionetsero Zake za mphamvu mu nthawi ina iliyonseyo ya msonkhanowo.

### **Kugwiritsa Ntchito Njira za m’Baibulo pa Utumiki wa Mphamvu mu m’Sonkhano wa Usodzi.**

Yesu ndi atumwi ali zitsanzo zathu za utumiki wa lero lino. Zimene Yesu ndi atumwi anachita mu mautumiki ao zikupitirira kugwirabe ntchito lero lino kupyolera mu kud zodza kwa Mzimu. Choncho, mlaliki wa msonkhano wa usodzi atha kuchiritsa odwala mwa:

- kulankhula mau
- kulamulira mwa chikhulupiliro
- kusanja manja pa iwo
- kumasula mphamvu za uzimu
- kugwiritsa ntchito njira ina iliyonse yopezeka mu Chipangano Chatsopano.

Mlaliki ayenera kudzipereka kwathunthu kwa Mzimu Woyera. Ayenera kumvetsera ku mau a Mzimu Woyera kulankhula ku mzimu wake. Mzimu adzamuza zoyenera kuchita nthawi iliyonse yomwe adzakhala akutumikira. Pamodzi naye pali zida zonse zomwe taphunzira mu chaputala 10 zakuthandizira. Iye sayenera kunyalapya zida izi ndi kusazigwiritsa ntchito.

### **Kugwiritsa Ntchito Njira Zitatu za Usodzi**

Takambirana magawo atatu a utumiki wa mphamvu mu machaputala anayi apitawa. Ndi kusintha pang’ono, njira iyi itha kugwiritsidwanso ntchito mu misonkhano ya usodzi. Njirayi imatipatsa ndondomeko yofunikira pakuchiritsa odwala ndi kuturutsa ziwanda.

1. *Kufunsa mafunso achidziwitso.* Mu nthawi ya msonkhano, nthawi imakhala yochepe kotero kuti mlaliki sangathe kuchezerana ndi aliyense amene

abwera kutsogolo kuti atumikiridwe. Ngakhale ziri choncho, iye sayenera kunyalanyaza nthawi yakufufuza ndi kupeza zosoweka mu nthawi ya utumiki wamphamvu. Mlaliki ayenera kukhala wotsegukira ku chitsogozo cha Mzimu Woyera. Nthawi zina, kuzindikira chosoweka kutha kubwera kudzera mu mphatso ya mavumbulutso. Mzimu Woyera atha kuvumbulutsa kwa mlaliki zosoweka zapaderadera pamene akupitiriza kutumikira kwa anthuwo. Kuti atumikire moyenerera, mlaliki ayenera kudziwa zimene Mulungu akuchita (onani Yohane 5:19).

Mlaliki ndi gulu lake ayenera nthawi zonse kupereka malangizo asanapempherere odwala. Ayenera kuwauza iwo amene akufuna pemphero zimene ayenera kuchita kuti alandire machiritso awo. Gulu lothandiziralo liyeneranso kulimbikitsa anthu odwalawo kuchitapo kanthu ndi chikhulupiliro chao ku zimene Mulungu akuchita. Akhonza kuuzanso anthuwo kuyembekezera machiritso pamene akupemphera.

*2. Pemphero.* Mlaliki ayenera kupitiriza kulola Mzimu Woyera kumutsogolera mu nthawi yakupemphera pemphero lamachiritso. Nthawi zina atha kutsogoleredwa kuti angowapempherera muchigulu. Nthawi zinanso atha kumva kuti awapempherere ali munzere ndi kumapempherera m' modzimodzi. Komanso nthawi zina Mzimu Woyera atha kumupatsa mau achidziwitso a chosowa cha munthu wina mugululo.

Mlaliki ayenera kukhala watcheru ku chitsogozo cha Mzimu Woyera pokhudzana ndi njira yoti agwiritse ntchito. Mzimu atha kumuuza kuti angolamulira matenda kuchoka mwa chikhulupiliro kapenanso kusanja manja pa munthuyo. Zotsatira zodabwitsa zidzatsatira pakumvera utsogoleri wa Mzimu Woyera.

Mlaliki wa msonkhano wa usodzi akhozanso kugwiritsa anthu omwe aphunzitsidwa aja mu nthawi yamapemphero iyi. Anthuwa atha kupemphera ndi anthu omwe akusowa machiritso kapena kumasulidwa. Atha kukhala ndi nthawi yapaderadera ndi munthu m' modzimodzi payekha.

*3. Uphungu wotsatira pemphero.* Mutamaliza kupemphera, mlaliki ayenera kupereka malangizo kwa iwo amene apemphereredwa. Ayenera kuwalimbikitsa kupitiriza mu chikhulupiliro, ndi kuchitira umboni kwa ena za chimene chawachitikira.

Mlalikiyo ayeneranso kuwatsogolera ku chipulumutso iwo amene sanapulumsidwe. Anthu ena amene ali ndi zosowa zikuluzikulu atha kufuna uphungu wapaderadera ndi mapemphero.

## **Kutsogolera Okhulupirira Atsopano Kukubatizidwa ndi Mzimu Woyera**

Msonkhano wachigonjetso wa usodzi umabala zipatso zochuluka za ongotembenuka mtima kumene. Mlaliki ayenera kuwatsogolera okhulupilirawa mu ubatizo wa Mzimu Woyera. Ili ndi dongosolo la m’Baibulo. Mu Chipangano Chatsopano, otembenuka mtima kumene amadzadzidwa ndi Mzimu Woyera nthawi yomweyo (Machitidwe a Atumwi 2:38-39; 8:14-17; 10:44-46; 19:1-6).

Pa kudzadzidwa ndi Mzimu Woyera, ongotembenuka mtima kumene amalimbikitsidwa mu kuyenda kwao kwa Chikhristu. Amapatsidwa mphamvu zakuchita umboni ku mabanja ao ndi anza. Komanso amalandira mphamvu zakugonjetsa mayesero ndi kukhala oona kwa Khristu.

### **Njira zitatu za Kutsindika Ubatizo wa Mzimu Woyera.**

Kodi mlaliki wa msonkhano wa usodzi angatsimikizike bwanji kuti ongotembenuka mtima kumene abatizidwa mu Mzimu Woyera? Atha kungwiritsa ntchito njira imodzi kapena zonse za njira izi.

1. *Kukhala ndi nthawi yamapephero usiku uliwonse.* Mwadongosolo lake, msonkhano wa usiku woyamba utatha, anthu ambiri amakhala atapulumsidwa. Choncho mlaliki amayenera kukonza nthawi yapadera yakupemphera nawo usiku uliwonse. Otembenuka mtimawo amayitanidwa kuti akhale ndi mapemphero akulandira Mzimu Woyera.

2. *Misonkhano yakulandira Mzimu Woyera.* Mlaliki ayenera kukonza dongosolo lakulandira Mzimu Woyera usiku wina wa msonkhanowo. Ayenera kulengeza za nthawiyi kumayambiro a masiku a msonkhanowo. Ayambenso kumawalimbikitsa ongotembenuka mtimawo tsiku lirilonse. Pa nthawi imene abwera ku mapemphero a tsikulo, abwere ali ndi chiyembekezo chakulandira Mzimu Woyera. Pa tsiku la msonkhanowo, mlaliki alalikire za ubatizo wa Mzimu Woyera. Pamapeto pake apemphere ndi anthuwo kuti alandire ubatizowo.

3. *Kalasi ya moyo watsopano.* Mlaliki atha kukonza kalasi ya moyo watsopano ya iwo atembenuka mtima. Makalasi ake atha kumachitika ku nthawi ya m’ mawa, masana kapena msonkhano wa madzulo utangotsala pang’ono kuyamba. Makalasi awa ayenera kukhalanso ndi chiphunzitso cha

ubatizo wa Mzimu Woyera. Aphunzitsi ake atenge nthawi yokwanira kupempherera ophunzira awo kuti alandire ubatizo umenewu mu nthawi ya makalasi awo.

Palibe chinthu chofunikira kwambiri kwa ongotembenuka mtima kumene ngati kubatizidwa ndi Mzimu Woyera. Ubatizo wa Mzimu Woyera ndi chifungulo cha kukula mwa Khristu komanso gweronso la mphamvu za kuchitira umboni Khristu. Mlaliki wanzeru sadzachedwetsa kapena kunyalanyaza chinthu ichi chofunikira.

### **Kugwiritsa Ntchito Chitsanzo cha Makwerero Atatu**

Mu chaputala 14, tinakambirana za mmene tingatsogolere munthu kuti alandire ubatizo wa Mzimu Woyera. Mosiyaniranapo, mlaliki wa msonkhano wa usodzi nthawi zambiri amapemphera ndi gulu lalikuru la anthu kuti adzadzidwe. Tsono izi zingachitike bwanji? Mlalikiyo atha kugwiritsabe ntchito magawo atatu aja takambirana mu chaputalacho. Komabe, njirazi ziyenera kugwiritsidwa ntchito moyenerera.

1. *Kufunsa mafunso a chidziwitso.* Nthawi zambiri, gulu lalikulu la anthu limabwera kutsogolo kuti lidzadzidwe ndi Mzimu Woyera. Ndizosatheka kuyamba kulangiza m' modzimodzi. Mlaliki wanzeru amapereka malangizo oyenerera gulu. Ena mwa malangizo amene angapereke ndi awa:

- alimbikitseni chifukwa chobwera kutsogolo kuti adzadzidwe
- phunzitsani anthuwo za zimene angachite kuti adzadzidwe, ndi zimene
- angayembekezere pamene akudzadzidwa
- limbikitsani chikhulupiliro chao kuti alandire lonjezo la Mzimu Woyera.

2. *Nthawi yakupemphera.* Mu nthawi yakupemphera, mlaliki atsogolere gulu lonse mu pemphero. Pemphero ili litha kukhala ndi chitsanzo chomwe chaperekedwa mu chaputala 14. Atsogolere aliyense mu chikhulupiliro.

3. *Uphungu wotsatira mapemphero.* Pamene amaliza kupemphera, mlaliki apereke uphungu kwa onse amene apempheredwa ndipo adzadzidwa. Awalimbikitse kuti apitirize kuyenda mu uzimu. Moonjezera, alimbikitsenso iwo onse amene sanadzadzidwe. Awalimbikitse kuti abwerenso mu mapemphero a usiku winanso pamene adzakhala akupempherera anthu ena

kubatizidwa ndi Mzimu Woyera. Anthu awa ayeneranso kukhala nao pa kalasi ya Mzimu Woyera ngati kalasilo liripo.

## **Chimangiliro**

Utumiki wa mphamvu ndi wofunikira pa magawo a msonkhano wa usodzi. Nthawi zambiri umatsegula zitseko kwa anthu kukuchitapo kanthu ku Uthenga Wabwino ndi kupulumutsidwa. Iwo amene akumva kuyitanidwa ku utumiki wa usodzi ndi aneneri a Mulungu ku anthu otayika. Ayenera kuphunzira kutumikira mmene angatumikire mu mphamvu ndi kudzodza kwa Mzimu Woyera.



## Zowonjesera A

### Utumiki wa Yesu wa Machiristo mu Mabuku a Utenga Wabwino

Ntawi za Machristo	Mateyu	Marko	Luka	Njira zogwiritsidwa Nchito
1. Muntu wa ziwanda		1:23	4:33	Mau, kuturutsa
2. Apongozi a Petro	8:14	1:30	4:38	Mau, kukhudza
3. Chikhamu cha anthu	8:16	1:32	4:40	Kukhudza, mau,
4. Ziwanda zambiri zinaturutsidwa		1:39		Kulalikirira, Kuturutsa
5. Akhate	8:2	1:40	5:12	Kukhudza, mau, chikhulupiliro,
6. Chikhamu cha anthu			5:15	Kachitapo changu ku chosowa
7. Wopuwala	9:2	2:3	5:18	Mau, chikhulupiliro cha
8. Munthu wa dzanja lopuwala	12:10	3:1	6:6	Mau, kumvera, chikhulupiliro
9. Chikhamu cha anthu	12:15	3:10		Kukhudza, chikhulupiliro,
10. Chiwanda cha ku Gadara	8:28	5:2	8:27	Mau, kuturutsa
11. Mwana wa Yairo aukuitsidwa	9:18-	5:23	8:41	Mau, kukhudza, chikhulupiliro
12. Mayi wodwala nthenda ya mwazi	9:20	5:25	8:43	Kukhudza, kuturutsa
13. Anthu odwala ochepa	13:58	6:5		Kukhudza (kuvuta ndi
14. Chikhamu cha anthu	14:35	6:55		Kukhudza, kuturutsa
15. Mkazi wa Kanani	15:22	7:25		Kuzindikira chikhulupiliro
16. Munthu wasamva ndi		7:32		Mau, kukhudza
17. Bambo wakhungu		8:22		Kukhudza (machiristo
18. M'nyamata wodzadzidwa ndi	17:14	9:17	9:38	Mau, kukhudza, chikhulupiliro
19. Bartimeyo wakhungu	20:30	10:46	18:3	Mau, kukhudza, chifundo,
20. Wantchito wa Kenturiyo	8:5		7:2	Kuchitapo kanthu ku
21. Amuna awiri akhungu	9:27			Mau, kukhudza
22. Chiwanda chakhungu ndi	12:2		11:1	Kuturutsa
23. Chiwanda chosalankhula	9:32			Kuturutsa
24. Chikhamu cha anthu (nthenda	4:23		6:17	Kuphunzitsa, kulalikirira,

Zowonjesera

25. Chikhamu cha anthu (nthenda)	9:35			Kuphunzitsa, kalalikira,
26. Chikhamu cha anthu	11:4		7:21	Kutsimikizira kwa Yohane
27. Chikhamu cha anthu	14:4		9:11	Chifundo
28. ChiKhamu cha anthu (opuwala)	15:30			Chikhulupiliro cha anzake
29. Chikhamu cha anthu	19:2			Sipanatchulidwe
30. Wopuwala ndi wakhungu	21:14			Chifundo
31. Mwana wa mayi wa ku Nayini			7:12	Mau, kukhudza, chifundo
32. Mariya wa Magadala ndi ena			8:2	Kuturutsa
33. Mayi womangidwa ndi ziwanda			13:1	Mau, kukhudza
34. Munthu wodwala mbulu			14:1-	Kukhudza
35. Akhate khumi			17:1	Kulamulira
36. Khutu la wantchito wa			22:5	Kukhudza

**Zowonjesera B****Kulamulira mwa Chikhulupiliro**

Nthawi zambiri Yesu anagwiritsa ntchito mau a ulamuliro pakuchiritsa odwala. Analamulira matenda kuti achoke, ziwanda zituruke ndipo matendawo anachoka pa chikhulupilirocho.

<b>Mateyu</b>	<b>Marko</b>	<b>Luka</b>	<b>Yohane</b>
8:13	1:30	4:38	
9:2	2:3	5:17	
12:9	3:1	6:6	
9:18	5:22	8:41	
—	7:32	—	
20:30	10:46	18:35	
9:27	—	—	
—	—	7:11	
—	—	13:10	
—	—	17:11	
—	—	—	4:46
—	—	—	5:12
—	—	—	9:1
—	—	—	11:1

### Chikhulupiliro cha Olandira

Nthawi zina, Yesu anachiritsa ataona chikhulupiliro cha munthu wofuna machiritsoyo.

Mateyu	Marko	Luka	Yohane
8:2	1:40	5:12	—
12:15	3:10	—	—
9:20	5:25	8:43	—
20:30	10:46	18:35	—
—	—	—	—

### Chikhulupiliro cha Anthu Ena

Mu nthawi zina, Yesu anachiritsa ataona chikhulupiliro cha anzake kapena abale ake a wodwala amene amafunafuna machiritso. M'malo mwake

Mateyu	Marko	Luka	Yohane
8:14	1:30	4:38	—
8:16	1:32	4:40	—
9:2	2:3	5:17	—
9:18	5:22	8:41	—
14:34	6:55	—	—
15:22	7:24	—	—
—	7:32	—	—
---	8:22	—	—

Zowonjesera

17:14	9:14	9:38	—
8:5	—	7:2	—
—	—	—	4:46

**Kukhudza**

Nthawi zina Yesu amakhudza anthu pamene anali kuwachiritsa .  
Kukhudza uku kumangokhala kutenga dzanja la munthu wodwalayo kapenanso kukhudza pamalo pamene pakusoweka machiritso.

<b>Mateyu</b>	<b>Marko</b>	<b>Luka</b>	<b>Yohane</b>
8:14	1:30	4:38	—
8:16	1:32	4:40	—
8:2	1:40	5:12	—
9:18	5:22	8:41	—
13:58	6:5	—	—
—	7:32	—	—
—	8:22	—	—
17:14	—	—	—
—	9:14	9:38	—
20:30	10:46	18:35	—
9:27	—	—	—
—	—	—	—
—	—	13:10	—
—	—	14:1	—
—	—	22:49	9:1

**Kuturutsa Ziwanda**

Mu nthawi zinanso, Yesu amachiritsa anthu mwa kuturutsa ziwanda zimene zimabweretsa matenda m'nthupi lao.

<b>Mateyu</b>	<b>Marko</b>	<b>Luka</b>	<b>Yohane</b>
—	1:23	4:33	—
12:15	3:10	—	—
8:28	5:1	8:26	—
9:32	—	—	—
12:22	—	11:14	—
—	—	8:2	—
—	—	13:32	—

### Chifundo

Kuonetsa chifundo kwa odwala ndi ovutika ianlinso njira ina yomwe Yesu amachiritsira odwala. Chifundo chake chinamupangitsa kufikira iwo ndi kwachiritsa.

Mateyu	Marko	Luka	Yohane
8:2	1:40	5:12	—
20:30	10:46	18:35	—
14:14	—	9:11	6:2
—	—	7:11	—

### Machiritso monga Chitsimikizo cha Kulalikira kapena Kuphunzitsa

Yesu nthawi zina anachiritsa monga chitsimikizo cha utumiki wake wa kulalikira kapena kuphunzitsa.

Mateyu	Marko	Luka	Yohane
---	1:39	—	—
4:23	—	6:17	—
9:35	—	—	—
11:4	—	7:21	—

**Machitidwe Apaderadera**

Ambuye wathu nthawi zina anachita zozizwa zachilendo ndi munjira yachilendo.

<b>Mateyu</b>	<b>Marko</b>	<b>Luka</b>	<b>Yohane</b>
9:20	5:25	8:43	—
14:34	6:55	—	—
—	8:22	—	—
—	—	—	9:1

## Mabuku Agwiritsidwa Ntchito a m'Chingelezi

- Duewel, Wesley. 1986. *Touch the World Through Prayer*. Grand Rapids, MI: Zondervan.
- Haltom, Fred. 1989. "Old Testament power encounters." in *Power Encounter, A Pentecostal Perspective*, ed. Opal Reddin, 94–122. Springfield, MO: Central Bible College.
- Horton, Stanley M. 1993. *Pneumatology*. Irving, TX: ICI University.
- . 1976. *What the Bible Says About the Holy Spirit*. Springfield, MO: Gospel Publishing House.
- Jeter, Hugh. 1977. *By His Stripes*. Springfield, MO: Gospel Publishing House.
- Kuzmic, Peter. 1988. "Kingdom of God." In *Dictionary of Pentecostal and Charismatic Movements*, ed. Stanley Burgess, Gary McGhee, and Patrick Alexander, 521–526. Grand Rapids, MI: Zondervan.
- Ladd, George Eldon. 1981. "The Gospel of the Kingdom." In *Perspectives on the World Christian Movement, A Reader*, ed. Ralph D. Winter and Steven C. Hawthorne, 51–69. Pasadena, CA: William Carey Library.
- Marshall, Tom. 1988. *Foundations for a Healing Ministry*. West Sussex, England: Sovereign World.
- Miller, Jim. n.d. "How to Heal the Sick." Unpublished manuscript (available through the author).
- Moon, Jessie K. 1989. "Power Encounter in Evangelism." In *Power Encounter, A Pentecostal Perspective*, ed. Opal Reddin, 232–255. Springfield, MO: Central Bible College.

- O'Donovan, Jr., William. 1992. *Introduction to Biblical Christianity From An African Perspective*. Ilorin, Nigeria: Nigeria Evangelical Fellowship.
- Osborn, T. L. 1955. *How to Receive Miracle Healing*. Nairobi: Evangel Publishing House.
- Otis Jr., George. 1991. *The Last of the Giants*. Tarrytown, NY: Chosen Books.
- Pennoyer, F. Douglas. 1990. "Dungeons of Collective Captivity." In *Wrestling with Dark Angels*, ed. C. Peter Wagner and F. Douglas Pennoyer, 249–279. Ventura, CA: Regal.
- Stamps, Don. 1992. "Acts 4:8, Peter Filled with the Holy Spirit." In *The Full Life Study Bible*, 1651. Grand Rapids, MI: Zondervan Publishers.
- . 1992. "Baptism in the Holy Spirit." In *The Full Life Study Bible*, 1642–1643. Grand Rapids, MI: Zondervan Publishers.
- . 1992. "Power over Satan and Demons." In *The Full Life Study Bible*, 1484–1485. Grand Rapids, MI: Zondervan Publishers.
- Unger, Merrill C. 1971. *Biblical Demonology*. Wheaton, IL: Scripture Press.
- Wagner, C. Peter. 1990. "Territorial Spirits." In *Wrestling with dark angels*, ed. C. Peter Wagner and F. Douglas Pennoyer, 73–91. Ventura, CA: Regal.
- Williams, Don. 1989. *Signs, Wonders, and the Kingdom of God*. Ann Arbor, MI: Servant Publications.
- Wimber, John. 1986. "The Power Encounter." In *Power evangelism*, ed. John Wimber with Kevin Springer, 13–31. San Francisco: Harper & Row.

## **Mabuku Ena a m'Chingelezi Othandizira**

- Bennett, Dennis and Rita Bennett. 1971. *The Holy Spirit and You*. Plainfield, NJ: Logos International.
- Bonnke, Reinhard. 1994. *Mighty Manifestations*. Eastbourne, UK: Kingsway Publication.
- Bosworth, F. F. 1973. *Christ the Healer*. Old Tappan, NJ: Revell.
- Carter, Howard. 1968. *Spiritual Gifts and Their Operation*. Springfield, MO: Gospel Publishing House.
- Evans, W.I. 1954. *This River Must Flow*. Springfield, MO: Gospel Publishing House.
- Exley, Richard. 1988. *Perils of Power: Immorality in the Ministry*. Tulsa, OK: Honor Books.
- Fitzpatrick, Graham. 1987. *Miracles, Faith, and God's Will*. N.S.W., Australia: Spiritual Growth Publications.
- Gramenz, Stuart. 1986. *How You Can Heal the Sick*. Chichester, UK: Sovereign World.
- Jeter, Hugh. 1977. *By His Stripes: a Biblical Study on Divine Healing*. Springfield, MO: Gospel Publishing House.
- Marshall, Tom. 1991. *Healing From the Inside Out: Understanding God's Touch for Spirit, Soul and Body*. Lynnwood, WA: Emerald Books.
- Pyches, David. 1985. *Spiritual Gifts in the Local Church*. Minneapolis: Bethany House Publishers.
- Summerall, Lester. 1979. *Demons, the Answer Book*. South Bend, IN: LeSEA

Publishing.

Wimber, John. 1986. *Power Evangelism*. San Francisco: Harper and Row.

\_\_\_\_\_. 1987. *Power Healing*. San Francisco: Harper & Row.



**Acts in Africa Initiative**